

CHISINDIKIZO CHACHISANU



Tiyeni tiweramitse mitu yathu tsopano kwa pemphero.

² Atate Achisomo Akumwamba, Mulungu Wamphamvuzonse, Yemwe munamubweretsa kachiwiri Yesu Khristu kuchokera kwa akufa, ndipo mwamupereka Iye kwa ife mmasiku otsiriza ano, mu Mphamvu ya Mzimu Woyera, ife tiri oyamikira chifukwa cha kuchezero kwamphamvu uku kwa Mulungu wa chisavundi. Ndipo tsopano, Atate, ife tikuyang'anizana nalo ora lina, ora limene likhoza kusintha kopita Kwamuyaya kwa anthu ambiri.

³ Ndipo kuyandikira ichi, Ambuye, ife ndife osakwanira. Chifukwa, izo ziri m'Malemba, kuti, "Mwanawankhosa anatenga Bukhu ndipo anatsegula Zisindikizo."

⁴ O Mwanawankhosa wa Mulungu, bwerani patsogolo, ife tikupemphera. Ife tikuyitanira pa Inu, Ambuye, Muwomboli wamkulu. Bwerani patsogolo ndipo mudzatiwonetse ife dongosolo Lanu la chiwombolo limene lakhala lobisika kudutsa mu zakazi, kudzamatula Chisindikizo Chachisanu ichi kwa ife usikuuno, Atate, ndi kudzawulula zomwe ziri pansi pa Chisindikizo chimenecho kwa ife; kuti ife tikakhoze kuchoka tiri Akhristu abwinoko kuposa momwe ife tiriri tsopano, kuti tikakhoze kukhala okwanira ku ntchito imene yagona patsogolo. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Khalani pansi.

⁵ Usiku wabwino, abwenzi. Ine ndikuwutenga uwu ngati mwayi wopambana kudzakhala pano usikuuno, pa chochitika chachikulu ichi. Ine sindikudziwa kulikonseko kumene ndingakhoze kumverera bwinoko, kuposa kudzakhala pa ntchito ya Mfumu. Ndipo tsopano kubwera makamaka pa maphunziro awa pamene ife tikungoyembekezera; ngati Iye akanati asawulule Izo kwa ine, ine sindikanakhoza kuzipereka Izo kwa inu. Ine sindikuyesetsa kugwiritsa ntchito lilirionse la maganizo anga anga kapena chirichonse; basi monga Iye ati andipatsire Izo. Uko nkulondola. Ndipo ine—ndine wotsimikiza, kuti ngati sindigwiritsa ntchito malingaliro anga anga, ndipo Izo nkumabwera mwanjira yomwe Izo zakhala zikubwereramu. Ndipo monse kudutsa mmoyo Izo sizinakhalepo zolakwika. Izo sizikhalanso zolakwika nthawi ino.

⁶ Tsopano, ndife mwaulemerero ndiponso, othokoza kwambiri pa zomwe Iye watichitira ife, dzanja lalikulu lachinsinsi la Mulungu wamoyo! Chingakhale chinthu chopambana bwanji, ife tingakhalenso anthu amwayi mochuluka chotani, kuposa kukhala naye mu kukhalapo kwathu Mfumu ya mafumu, Mbuye wa ambuye?

⁷ Ife mwinamwake tingalize malikhweru ndi—ndi kukweza mbendera, ndi kuyala makalapeti ndi chirichonse, kwa Purezidenti wa fuko kuti wabwera mu mzinda. Koma, tangoganizani, izo zingakhale zabwino, ndipo icho chingakhale cha ulemu kwa mzindawu.

⁸ Koma taganizani. Mu kachisi wathu wamng'ono, wonyozeka, usikuuno, ife tikumuitana Mfumu ya mafumu, Mulungu. Ndipo ife sitiri...Iye samakhumba makalapeti kuti ayalidwepo, ndi zina zotero. Iye amafuna mitima yodzichepetsa kuti iyalidwe, kuti Iye akakhoze kutenga mitima yodzichepetsa iyi ndi kuwulula kwa iyo—zinthu zabwino zomwe Iye wawasungira iwo onse amene amamukonda Iye.

⁹ Tsopano, ife tinafunsa. . . Ndipo ine ndiri ndi umboni umene ine ndikufuna kuti—kuti ndiwupereke. Tsopano, ngati ine ndikulakwitsa pa izi; ine ndinangozimva izo, ndipo ine ndikhoza kukhala kuti ndikulakwitsa. Koma ndikuganiza kuti anthuwo ali pano, amene umboniwo ukuwakhudza.

¹⁰ Ndiyeno, masiku angapo apitawo, pamene ine ndinali kwathu tsopano, ku—ku Arizona, ife tinalandira a—foni yonena kuti kunali mnyamata wamng'ono amene anali ndi nyamakazi. Ndipo iyo imapita ku mtima. Ndipo iye anali chotero. . . Abambo ake ndi amayi ake ndi okondedwa chomwecho, azimzanga ofunika a ine. Anali athu. . . mmodzi wa madikoni athu pano, a mpingo, M'bale Collins. Mnyamata wake wamng'ono, Mikey wamng'ono, amene amasewera ndi Joe, anali akuvutika ndi nyamakazi ya mtima. Ndipo madokotala anali atamutumiza iye kwawo, anakamuyika iye pa bedi, ndipo anawauza makolo kuti asamulole iye ngakhale kuti adzukepo, kapena kudzutsa mutu wake, kuti amwe madzi. Amamwera iwo kudzera mu kapaipi; iye anali moyipa kwambiri. Ndipo makolowo, okhulupirika, amabwera ku kachisi kuno, ndipo amakhulupirira.

¹¹ Ndipo mausiku angapo apitawo, posafuna kuti ayesere kuyembekezera, ife tinalengeza misonkhano ya machiritso pa Lamlungu. Koma, powona kuti ife timayenera kuyankha mafunso, kotero ndiye ife tinayenera kuchotsapo msonkhano wa machiritsowo.

¹² Ndiyeno ine ndinali nako kenakake kakang'ono kamene ine ndakhala ndikukasunga mkati mwanga, mu mtima mwanga.

¹³ Ndipo mayi ndi bambowo ankafuna kudziwa ngati iwo akanakhoza kumubweretsa mwanayo a—mchipindamo. Ndipo iwo anamubweretsa mwana wamng'onoyo kumeneko, ndipo Mzimu Woyera unamuuzza iye kuti wachiritsidwa.

¹⁴ Ndipo kotero, makolowo, pokhala olemekeza chimenecho, anamutengera mnyamata wamng'onoyo kunyumba ndi kukamutumiza iye ku sukulu, anangomutumiza iye ku sukulu.

¹⁵ Adokotalawo anazimva zimenezo, kotero adokotalawo sanakondweretsedwe bwino ndi chinthu choterocho. Chotero,

iyе anawauza amayiwo kuti mwanayo ayenera kukhala akugona, ndithudi. Ndipo mayiyo anawauza iwo nkhaniyo. Ndipo ine ndikuganiza kuti munthuyo ali, ine ndikumva, kuti ndi Mkhristu wokhulupirira, mwa chipembedzo. Wa—wa Seventh-day Adventist, dokotalayo wa kumeneko. Ndipo kotero iye anati, “Chabwino, inu muyenera...ndi nthawi yoti mwanayo, yoti ine ndimupime iye.” Anati, “Inu muyenera kutero, bolani, akhale atapimidwa.”

Mlongoyo anati, “Zabwino kwambiri.”

¹⁶ Anamutengera mwanayo uko, ndipo dokotalayo anamupima iye, mmagazi, mmene nyamakaziyo imakhala. Ndipo kotero ine ndikumva kuti dokotalayo anali wodabwitsidwa kwambiri mwakuti sanadziwe choti achite. Mwana wamng’ono alibwino bwino mwangwiro, wathanzi ndi wabwino, palibe a...?...kanapezeka.

¹⁷ Tsopano, kodi alipo a Collins pano? Ine ndikhoza kukhala kuti ndinazinena zimenezo molakwika. Ine ndikufuna...Kodi nkulondola uko, Mlongo Collins? Eya. Chabwino. Eya. Ameneyo ndi Mikey Collins wamng’ono, pafupifupi zaka sikisi, zaka seveni zakubadwa.

¹⁸ Ndipo zimenezo zinachitika mchipinda momwemo, pafupifupi mausiku atatu apitawo. Oh, iwo...Muyenera kuti munali Winawake mchipindamo pambali pa munthu chabe! Anali a—Yehova wamkulu ndi wamphamvu, uko nkulondola, amene amabwera kudzalemekeza Mawu Ake. Ndipo ine—ndine woyamikira kwambiri pakumva zimenezo. Mukuona? Ine ndikudziwa kuti ife tonse tiri. Osati ine ndekha, koma tonsefe ndi choncho, chifukwa nanga bwanji ngati ameneyo akanakhala—akanakhala mnyamata wanu wamng’ono kapena mnyamata wanga wamng’ono?

¹⁹ Ndipo, kumbukirani, ine ndikupereka umboni, monga ngati umodzi wokha, ndipo ndikutenga umodzi apa ndi apo. Izo zikuchitika kulikonseko, koma ndikungokudziwitsani kuti—kuti utumiki wanga weniweni uli pa machiritso Auzimu. Koma inu...Ine ndiri pano chifukwa cha Zisindikizo izi. Chifukwa, pakapita kanthawi pang’ono, inu mudzamvetsa chifukwa chimene ine ndimayenera kudzachita izi. Ndipo, chotero, ine sindine mphunzitsi, ine sindine wafiolole. Ine—ine ndimangopempherera odwala, ndipo ine ndimawakonda Ambuye. Ndipo tsopano, tsopano mu izi, ngakhale, kuti...

²⁰ Usiku wathawu ife tinapereka umboni wa mtsikana wamng’ono...Ine ndiri nalo dzina lake. Ndipo Billy ali nalo ilo apa tsopano, penapake, la makolo ndi amene iwo ali. Ndipo mtsikana wamng’ono uyu anali mu siteji yotsiriza ya leukemia, pafupifupi basi...Moyipa kwambiri basi mwakuti iwo samakhoza kumudyetsera iye ndi kamwa iyi nkomwe; iye amayenera kukhala...magazi ake ankalowetsedwa kudzera

mmitsempha. Ndipo iye anali kanthu kakang'ono kokongola. Iye anali wamng'ono kutengera ndi usinkhu wake, pafupifupi monga dona wamng'ono uyu apa, ine ndikuganiza. Koma iye anali pafupifupi wamtali *chonchi*, kwambiri. . . Iwo anali monga ambiri a ife. Inu mukanakhoza kuzindikira ndi kavalidwe ka mwanayo, kuti. . . ndi makolowo, kuti iwo anali osauka kwambiri, basi osauka kwambiri, ndipo, kotero, koma aulemu kwenikweni. Ndipo Mzimu Woyera unalengeza kuti mwanayo wachiritsidwa.

²¹ Tsopano, tangoganizani za zimenezo, ali ndi leukemia, mwana wamng'ono ameneyo. Ndipo magaziwo anali atayipa kwambiri mwakuti iwo samakhoza ngakhale kumudyetsa iye kudzera pa kamwa nkomwe. Izo zinachita kutengera, kupita ku chipatala ndi kukatenga magazi, kapena kulowetsa kudzera mmitsempha, kumamudyetsa iye; ine ndikuganiza, gulukosi, kapena chirichonsecho. Ine sindikudziwa dzina la zamankhwala lomwe liri kwa matenda amenewo, koma, komabe, iye ankayenera kumadyetsedwa mwanjira imeneyo. Ndipo mwanayo asanachoke pamalopo, analirira chitumbuwa.

²² Ndipo makolowo, atha kuwumva Mzimu Woyera, za PAKUTI ATERO AMBUYE, mwaona, iwo. . . Ndipo, iwo, pokhala alendo, anali asanakhalepo kuno nkale lomwe. Koma iwo. . . A—banja lokoma lachikulire amene angokhala kumene pa mipando yawo apa, maminiti pang'ono apitawo, M'bale ndi Mlongo Kidd, anali atawalangiza iwo choti achite, ndi chakuti amvetsera. Ndipo mwanayo amadya chakudya chake akupita kwawo.

²³ Masiku awiri kapena atatu zitachitika zimenezo, ku sukulu. Ndipo anapita kwa dokotala, ndipo dokotalayo anali wodabwa kwambiri! Iye anati, “Palibe ngakhale chisonyezo chimodzi cha leukemia chomwe chapezeka mwa mwanayu.” Mukuona? Tsopano, ndicho cha pomwepo, pa malo omwewo, Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse, kutenga mpita wa magazi ndi kuwutsuka iwo, pomwepo monga chomwecho, ndi—ndi kuyika kugunda kwa—kwa moyo watsopano kuwubwezeretsanso mmenemo. Chifukwa, wanu—mpita wanu wa magazi ndi moyo wanu, wachivundi. Ndi kulenga makhungu atsopano, ndi kuchotsa akalewo! Ndipo—ndipo chimene icho chiri, icho chiri mwamtheradi. . . Ine ndingakhoze kunena ichi, ako ndi kachitidwe kolenga ka Mulungu Wamphamvuzonse; kutenga a—mpita wamagazi umene wayipitsidwa ndi khansa, mpaka mwana wamng'onoyo, anakhala wachikasu ndi wotupa, ndipo, mu mphindi zochepa chabe, nkudzakhala mpita wamagazi atsopano!

²⁴ Ine ndikukhulupirira. . . ine sindiyankhula izo mu Dzina Lake; ine ndiyankhula izo mu langa. . . mu vumbulutso la chikhulupiro changa, chimene chinachitika mu Sabino Canyon tsiku lina. Ine ndikukhulupirira kuti ora likuyandikira, pamene

ziwalo zosowa zidzabwezeretsedwa, ndi Mphamvu yaulemelero ya Mlengi. Ine—ine ndikukhulupirira, ngati Iye angapangitse gologolo kuwonekera, amene alibe... Apa pali mwamuna kapena mkazi, basi ali nacho chiwalo chosowa. Ndipo ndicho chinyama chathunthu, mwa icho chokha. Iye ndi Mulungu. Ine—ine ndimamukonda Iye.

25 Chabwino, tsopano, ine ndikayamba pa maphunziro amenewo, ndipo ife timangoyankhula mopitirira. Ndipo anthu atazungulira makoma, ndipo ataimirira mmaholo ndi m'zipinda, ndi zina zotero, kotero ine ndifika molunjika kumene ku Uthenga.

26 Ndipo ndikufuna kunena ichi, ndipo ine ndikufuna kupereka mathokoza kwa Iye Yemwe ali wopezekapaliponse. Ndipo, kuti, lero, osadziwa kanthu kamodzi kokhudza Chisindikizo Chachisanu icho, Icho chinabwera mwanjira yomweyo yachinsinsi, mmawa uno, pafupifupi ora limodzi kusanache, pamene ine ndinali kunja mu pemphero. Ndipo lero. . .

27 Ine ndangokhala basi masiku faivi apitawa kapena sikisi, ndiri mchipinda chaching'ono, osamuwona mmodzi aliyense. Kumangotuluka ndi kukadya zakudya zanga ndi—ndi mzanga, ndi ena a abwenzi apa. Ndipo, zedi, inu mukumudziwa yemwe mzanga ameneyo ali, ndi M'bale ndi Mlongo Wood. Eya. Ndipo—ndipo inu mukudziwa, ndipo ine ndinapita kumeneko ndi—ndi kukakhala nawo iwo, ndipo aliyense wakhala ali wabwino. Ndipo sipanakhale pali chirichonse, mophweka chabe. . .

28 Ine ndikuyesetsa kuti ndikhale ndi Uthenga umenewo wa Zisindikizo izi. Ndi wofunikira, ine ndikukhulupirira kuti ndiro—ndiro ora la nthawi Yake yowulula, vumbulutso la Zimenezo.

29 Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti inu mukhale otsimikiza tsopano, mofulumira, isanafike, mwamsanga momwe inu mungathere, mulembe kusamvetsetsa kwanu kosadziwika kwa—kwa Zisindikizo Zisanu Ndi Ziwiri izi, ngati inu muli nazo izo, ndipo mudzaziyeke izo pa desiki. Ndipo mwinamwake M'bale Neville kapena winawake akhoza kuyika bokosi pamwamba apa. [Winawake akuti, “Apa pali bokosilo.”—Mkonzi]. Oh, apa—apa, ine ndikuwawona iwo tsopano. Izo ziribwino. Kulibwino ine ndikhale nawo iwo usikuuno, kuti ine ndikhoze mwinamwake kuwawerenga iwo kwa kanthawi, kukonzekera Lamlungu mmawa. Tsopano, musati, nthawi ino, pa nthawi ino pomwe, musapange zopempha zakuti, kumati, “Kodi *uwu* ndi umboni wa Mzimu Woyera?” Mukuona? Ine—ine ndikufuna kudziwa za, zimene ine ndaphunzitsa, inu mukuona, kotero kuti ife tikhoza kutenga phunziro limodzi ili (monga Mibadwo ya Mpingo) molunjika, mwaona, chifukwa ndizo zimene ife tikuchita nazo tsopano.

³⁰ Tsopano, monga ife titati tipempherere odwala, ndiye izo zimatengera mwinamwake a—pemphero losiyana. Ndipo iwe umadzozedwa, umalowa mkati kuti udzachite chinthu chosinthika, inu mukudziwa. Ndipo iwe umafunafuna Mulungu, kuti upeze, “Kodi kukakhala wina kumeneko usikuuno, Ambuye?”

³¹ “Inde, akakhala winawake atavala diredi la chikasu, atakhala pa ngodya ya kudzanja lamanja. Ndipo pamene iwe ukamuyitana iye, ukamutche iye *ichi*. Ndipo ukati *chakuti* ndi *chakuti* chimene iye wachita. Ndipo iye ali ndi *chakuti-ndi-chakuti*.” Ndiye iwe umapita kumeneko ndi kukayang’ana, ndipo pamenepo iye amakhala alipo. Mukuona? Ndi zimenezotu, mwaona. Ndi zosiyana. Mukuona?

³² Ndipo mwanjira iyi, ine ndikupemphera, “Ambuye Yesu, tanthauzo la Ichi ndi chiyani? Wululani Icho kwa ine.” Amen.

³³ Tsopano tiyeni titulutse athu—titulutse Malupanga athu kachiwiri tsopano, ndipo, Mawu.

³⁴ Ndipo ine ndikuyamikira thandizo lauzimu la M’bale Neville, komanso chikondi chake chapaubale, kumbuyo kuno kuseri kwanga, akundipempherera ine. Ndi anu onsewo kunja uko, nawonso. Ndipo, tsopano, usikuuno pokhala Lachisanu usiku, ife tiyesetsa, kungolipanga ilo ngati...ife...

³⁵ Iwe sungakhoze mothekera kugunda zinthu zonsezo. Iwe... Chifukwa, iwe ukhoza kutenga Icho, chimodzi chokha cha Zisindikizo zimenezo, ndi kukhalapo, basi—kungochibweretsa Icho kudutsa mu Lemba, mpaka mmusi momwe. Mukuona? Zingakhoze kutenga miyezi ndi miyezi ndi miyezi, ndipo iwe osakhoza kukhala nachobe Icho, chifukwa chi—Chisindikizochi Pachokha chimamangiriza Lemba lonse, kuchokera ku Genesis mpaka ku Chivumbulutso, Chisindikizo chimodzi cha Izo.

³⁶ Kotero chimene ine ndikuyesetsa kuchita, ndi, kupewa kuchoka kupita kutali kwa Icho, ine ndimalemba Lemba, kapena—kapena kamfundo kakang’ono apa penapake, ndi kupewa ku...Kumangopitirirabe pa chinthu chimodzi chimenecho, ine ndimayenera kumayang’ana mmbuyo, chifukwa, ine ndimango...Kuyankhula, ine ndimayankhula mwa—mwanjira...Ine—ine ndikuyembekeza kuti ndiko kudzoza koyenera. Ndiyeno pamene ine—pamene ine ndiyang’ana mmusi kuti ndiwone...Ndipo ine—ine ndimayamba kuyankhula, ndipo ndimadzimverera ndekha ndikuchoka pa phunziro, ine ndimachewuka pozungulira, nkuyang’ana mmbuyo kumbali ina, kuti ndiyesetse kupeza Lemba lina, kuti ndifike pa chimenecho, inu mukuona, kukhala ngati kuchiwalitsira icho pang’ono ku mbali imeneyo, mmalo moyesetsa kumapitirira ndi chimenecho.

³⁷ Ndipo kotero tsopano ife tiphunzira usikuuno, mwa chisomo cha Mulungu, mwa kuthandiza Kwake, chi—Chisindikizo

Chachisanu. Ndipo Icho ndi chimodzi chachifupi. Ndi chotalikirapo pang'ono kuposa chinacho. Okwera pa kavalo anayi aja, tsopano, zimakhala ndime ziwiri pa chirichonse, ndipo ichi ndi ndime zitatu mu chimodzi ichi. Tsopano, Chisindikizo Chachisanu chikuyambira, pa mutu wa 6 wa Chivumbulutso, ndime ya 9.

³⁸ Ndipo, tsopano, ngati inu mungakhale kuti ndinu a—mlendo amene simunawamve akavalo anayi awa, chabwino, inu... Mwaona, nthawizina iwe—iwe umangobwerera mmbuyo ndi—ndi kukhala ngati ukusomeka chinachake, ndipo, pamene iwe utero, iwe umayembekeza kuti anthu amvetsa Zimenezo. Kotero ngati pali chinachake chaching'ono chimene inu simukuchimvetsa, chabwino, mungokhala ngati mungopirira pang'ono. Kapena, mudzatenge tepi ndipo mudzamvetsere kwa Izo, ndipo—ndipo ine ndikutsimikiza kuti inu muka—mukalandira mdalitso kuchokera kwa Zimenezo. Ine ndiri. Ine—ine ndikuyembekeza kuti inu—kuti inu mutero.

³⁹ Tsopano, aliyense wakonzeka, kuchokera pa ndime ya 9 tsopano mpaka ya 11, kapena kuphatikiza ya 11.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansi pa guwa miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anawugwira:

Ndipo iwo anafuula ndi mawu okweza, kunena, Mpaka liti, O Ambuye, woyera ndi woona, muti mudzachite... mudzaweruze ndi kubwezera magari athu pa iwo amene anakhala padziko lapansi?

Ndipo mikanjo yoyera inapatsidwa kwa aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti apumulebe kwa ka—kanthawi pang'ono, kufikira antchito amzawo nawonso... abale awo, kuti ayenera kuphedwa monga iwo anachitira, kuti zikwaniritsidwe.

⁴⁰ Tsopano, ichi ndi chokhala ngati chachinsinsi. Ndipo tsopano chifukwa cha matepi, ndi azibusa ndi aphunzitsi amene akhala pano, tsopano, ngati inu muli ndi lingaliro losiyana ndi Ichi; ine ndimatero, nanenso. Koma ine ndikungochitenga Icho kuchokera ku kudzoza, kumene mwathunthu kunasinthia lingaliro langa la Icho. Mukuona?

⁴¹ Ndiyeno ine ndikupeza kuti, pamene inu mukuwona izi zikuwululidwa, Izo zikubwerera mmbuyo momwe ndi kubweretsa mibadwo ya mpingo iyo ndi Malembawo pamodzi, ndi kudzazimangiriza Izo. Mukuona? Ndipo ndi chifukwa chake ine ndikukhulupirira kuti Izo zikuchokera kwa Mulungu. Tsopano, ife tikuzindikira zimenezo.

⁴² Ndipo ine ndikuganiza kuti nthawi zina ife timadalira pa zomwe mphunzitsi wina wamkulu anayankhula zokhudza Icho. Mukuona? Ndipo ndizo—ndizo zonse zabwino. Ine

sindikumutsutsa mphunzitsiyo, osati mwanjira iliyonse. Ndipo ine sindimatsutsa aliyense. Ine ndimangotsutsa tchimo, kusakhulupirira; osati winawake.

⁴³ Ndipo anthu ena anenapo kuti, “Inu mumatsutsa bungwe.” Ayi, ine sinditero. Ine—ine ndimatsutsa kachitidwe ka bungwe; osati anthuwo mmenemo, gulu la anthu limene limapanga bungwe, inu mukudziwa. Koma kachitidwe komwe iwo akulamulidwa nako, ndiko kamene ine ndimakatsutsa, Chikatolika ndi Chiprotestanti, mofanana. Mai! ine ndiri . . .

⁴⁴ Ena mwa azimzanga abwino kwambiri amene—amene—amene ine ndikuwadziwa, ndi Achikatolika, basi . . . ? . . . Kodi inu mukuzindikira . . . Ndipo munthuyo mwina akhoza kukhala kuti ali pano usikuuno, mwinamwake ali. Njira yokhayo imene ife tinamangira kachisi uyu, ndi chifukwa chakuti Mkatolika wa Chiroma anayima pa mapazi ake mu bwalo lamilandu kumeneko, ndipo anapita kutsogolo mmalo mwanga, ndipo, mnyamata, ngati palibe aliyense akanachita. Uko nkulondola. Ndipo iwo sakanakhoza kuchikana icho. Uko nkulondola.

Ndipo anati, “Iwo anali ataziwunikira izo, ‘Anthu ochuluka kwambiri.’”

⁴⁵ Iye anati, “Oh, sangabweretse eyite ena owonjezera mu tchalitchi chimenecho, monga chomwecho.” Anati, “Tchalitchi chimenecho chiri kumeneko.” Anati, “Ine—ine ndikumudziwa m’busayo, ndi zonse monga choncho.” Ndipo anati, “Tchalitchi chimenecho chakhala chiri kumeneko.” Anati, “Ena nonse inu mumakhoza kuwonjezera kwa icho, ndiye bwanji kuti iwowo alephere kutero?” Wa Roma Katolika, mzanga wabwino wa ine. Mukuona? Inde, bwana.

⁴⁶ A—mnyamata amene ali a—Mkatolika, mzanga weniweni womvana ndi ine, anali kuyankhula ndi ine, anali nayo sitolo inayake ya zipangizo, ine ndisanachoke, iye anati, “Billy, ine—ine ndikudziwa kuti iwe sumakhulupirira mu kachitidwe kathu ka chipembedzo.” Iye anati, “Koma ine ndikukuwuzwa iwe pakali pano,” anati, “Mulungu walemekeza kwambiri mapemphero ako kwa ife! Ine ndikukhulupirira, kuti ngati utakhala mu vuto kulikonse mu fukoli,” anati, “Mkatolika aliyense mdzikoli adzabwera kwa iwe.” Kotero, inu mukuona, ndiko . . .

⁴⁷ Iye anati, “Aliyense wa mtandapansana,” iye ankadzitcha chimenecho. Ine ndizinena izo basi monga momwe iye ankanenera. Chifukwa, iwo amadzinenera kuti ali chimenecho chifukwa Akhristu oyambirira ankanyamula mitanda pamisana pawo. Ife timadziwa zimenezo mwa mbiriyakale. Ndipo iwo amadzinenera kuti ndi Akhristu oyambirira, chimene iwo anali, koma kachitidweko kawachotsa iwo pa njira imeneyo, inu mukuona.

⁴⁸ Ndipo anthu amenewo, Achikatolika, kapena Myuda, kapena aliyense amene ali, iwo ndi anthu ochokera pa mtengo

womwewo umene ife tinachokerako. Mukuona? Uko nkulondola. Iwo ali—iwo ndi anthu amene amakonda, ndipo amadya, ndi kumwa, ndi kugona, ndi monga basi wina aliyense. Ndipo kotero ife sitiyanera kumawatsutsa anthu pawokha, ayi, osati mmodzi, mwaona. Koma, ife tisamawatsutse anthu pawokha.

⁴⁹ Koma, monga mtumiki, ine ndiyenera kumayikantha njoka imeneyo kunja uko, imene ikumawaluma anthu amenewo, mukuona. Ndipo ine sindi—ndipo ine sinditi nkomwe... Basi ineyo, ndipo ndekha, ine sindikanamachita zimenezo ngati iwo ukanapanda kukhala utumiki wochokera kwa Mulungu, umene ine ndimakhala wokakamizidwa kuchita izo, mwaona. Ndipo ine ndiyenera kuwugwira iwo mooni ndi mokhulupirika.

⁵⁰ Koma ngati Mkatolika, Myuda, kapena aliyense amene iye anali, abwera kuno, ngati iye anali wa Chimuhamadi, Mgriki, kapena wa Orthodox, kapena chirichonse chimene angakhale, ngati iye abwera kuno kuti adzapemphereredwe, ine ndingakhoke kumupempherera iye moonantima basi monga ine ndingachitire kwa wanga yemwe. Uko nkulondola. Ndithudi, chifukwa iye ndi munthu. Ndipo ndawapemphererapo Achibuddha, ndi Achisikh, Achijaini, Achimuhamadi, ndi—ndi a mtundu uliwonse, mukuona, monga choncho. Ndipo ine sindimawafunsa iwo mafunso; ine ndimangowapempherera iwo, chifukwa iwo ndi winawake, munthu amene akufuna kupeza bwino, ndipo ndimayesetsa kuwupanga moyo kukhala wophwekerako pang'ono panjirayo kwa iwo.

⁵¹ Tsopano ife tikuzindikira, kuti, mu ichi, ndipo ambiri a inu pano ine ndikukudziwani, pali pafupifupi awiri kapena atatu ophunzira enieni akhala pano. Ndipo—ndipo iwo ndi anzeru, ndipo awerengapo kuchokera—kuchokera mu ziphunzitso za anthu ena pa phunziro ili. Ndipo ndikufuna kuti abale awa adziwe kuti ine—ine sindikuwatsutsa anthu awa. Ine ndikungofotokoza kokha chimene Ambuye akundiwonetsera ine. Ndipo ndizo zonse zimene ine ndiri nazo.

⁵² Tsopano, ife sitikufuna konse kumaganiza zimenezo, chifukwa mkazi wina wochapa kapena—kapena mnyamata wamng'ono wolima kunja uko, sangakhoke kupeza vumbulutso kuchokera kwa Mulungu. Chifukwa, inu mukuona, izo... Mulungu, Iye makamaka amadziwulula Yekha mu kuphweka. Ndizo, ife tinali nazo zimenezo Lamlungu lija, kuti tiyambirepo izi, momwe Iye amadziwululira Yekha mu kuphweka Kwake. Ndicho chimene chimamupanga Iye kukhala wamkulu.

⁵³ Tsopano mulole—ndiroleni ine basi—Ndiroleni ine ndingobwerezanso izo kwa miniti yokha. Chimene chimamupangitsa Mulungu kukhala wamkulu, ndi chifukwa kuti Iye akhoza kudzipangitsa Yekha wophweka kwambiri. Ndicho chimene chimamupanga Iye kukhala wamkulu. Mulungu ndi wamkulu, ndipo akhoza kudzipanga yekha

mwa mawonekedwe ophweka chotero mwakuti anzeru a dziko lino sangakhoze kumupeza Iye. Iwo basi sangakhoze kumupeza Iye, chifukwa Iye amadzipangitsa Yekha kukhala wophweka kwambiri. Tsopano penyani. Ndipo ichi, mwa icho chokha, ndi chinsinsi cha vumbulutso la Yesu Khristu. Mukuona? Ichi, mwa icho chokha, kuti pa...Pali...sipangakhale chinthu chachikulu kwambiri choposa Mulungu. Ndipo inu simungakhoze kupanga chirichonse mophweka chotero monga momwe Iye amadzipangira Yekha. Mwaona, ndicho chimene chimamupanga Iye kukhala wamkulu. Mukuona?

⁵⁴ Tsopano, munthu wamkulu, iye akhoza kungokhala wokulirapo pang'ono, kapena mwinamwake iye akhoza kuwerama pansi ndi kuti, “Iwe uli bwanji?” kwa iwe, mwaona, kapena chinachake chonga chimenecho. Koma iye sangakhoze kudzipanga yekha kukhala wamng'ono. Pamakhala chinachake basi chokhudza iye. Iye ndi munthu. Iye sangakhoze basi kudzipanga yekha kukhala wamng'ono. Chifukwa, pamene iye afika potsika nkukhala wamng'ono kwambiri, ndiye, chinthu choyamba inu mukudziwa, iye ayenera kulozera ku chimene winawake anachita, ndipo monga chomwecho. Ndipo kenako iye amayamba kudzikokera yekha mmbuyo kachiwiri, mukuona.

Koma, njira yopitira mmwamba ndi pansi, mwa Mulungu. Inde.

⁵⁵ Anzeru a mdziko akuyesetsa, mu nzeru yawo, kuti amupeze Iye. Iwo amangokwera kutali kuchoka kwa Iye, pochita zimenezo. Mwaona, anzeru a mdziko, ngati iwe ukuyesetsa kufotokoza chinachake mwa masamu ena kapena chinachake. Kumbukirani, Iye anayika ngakhale zimenezo...Mu Baibulo, mu Chivumb-...Ayi, ndikupempha kukhululuka kwanu.

⁵⁶ Yesaya 35, ine ndikukhulupirira iye ali, kuti ngakhale ziri chomwecho—izo ndi zophweka kwambiri mwakuti ngakhale a—a—munthu wamakhalidwe oyipa akhoza kuzimvetisa Izo. Mwaona? Oh, “Ngakhale chitsiru sichidzaphonyetsa mmenemo.”

⁵⁷ Anzeru amaziphonya izo kutali, mwa nzeru zawo, amapita kutali kuchoka kwa Iye, poyesetsa kuti amupeze Iye mwa nzeru. Tsopano, musaiwale zimenezo. Izo zijambulidwa, mukuona. Anzeru, mu nzeru zawo, amapita kutali kwambiri poyesetsa kuti amupeze Iye mwa nzeru zawo, iwo amamuphonya Iye, mwaona. Ngati iwo angakhoze kukhala aakulu mokwanira kuti akhale ophweka mokwanira, iwo akhoza kumupeza Iye. Ngati utakhala wamkulu mokwanira kuti ukhale wophweka mokwanira! Mukuziwona zimenezo? Ndipo, inu mukudziwa, kuti—izo kwenikweni ndi Choonadi.

⁵⁸ Ine ndapitapo kwa anthu, mmaofesi awo, ndi zina zotero, amene anali kwenikweni amuna, aakulu, mafumu, mwaona, ndi olamulira, atsogoleri, ndipo kawirikawiri iwo amakhala anthu aakulu. Ndiye, ndapitapo mmalo mmene munthu amakhala

ndi zovala zosinthira, mwinamwake mtumiki wina amene ankafuna kutsutsana nane ine kwa kanthawi, ndipo iwe—iwe ukhoza kuganiza kuti dziko silingakhoze kuyenda popanda iye, mwaona. Ndipo yemwe—yemwe amangodzitukumula mmutu, mwaona. Koma munthu wamkulu, munthu wamkulu amakhala pansi ndi kumayesetsa kukupanga iwe kuganiza kuti *ndiwe* munthu wamkulu. Mukuona? Mukuona? Iye amakhoza kudzichepetsa yekha.

⁵⁹ Ndipo, inu mukuona, Mulungu ndi wamkulu kwambiri mpaka Iye akhoza kudzichepetsa Yekha, kufika kumalo, amene munthu sangakhoze kutsika pansi utali woterewo, mukuona. Ndizo zonse. Ndipo mkati mwawo . . .

⁶⁰ Ndipo iwo akuyesetsa kuti amupeze Iye. Tsopano taonani. Iwo akuyesetsa kuti amupeze Iye powatumiza anyamata ku sukulu, ndi kukatenga digirii ya Bachelor of Art. Ndipo—ndipo iwo akuyesetsa kuti amupeze Iye mwa kufotokoza kwa fioloje kwa—kwa—kwa—kwa Baibulo. Ndipo iwo akuyesetsa kuti amupeze Iye mwa madongosolo a maphunziro, ndi mwa madongosolo a zabungwe, ndi mwa kukongoletsa zinthu, ndi kumayesetsa kuti apeze. Iye siali mmenemo, nkomwe. Inu mukungomenyana ndi mphepo, ndizo zonse. Ndinu—inu mukupita kutali kwa Ichu.

⁶¹ Ngati iwo angakhoze kukhala aakulu mokwanira kuti akhale—kuti akhale ophweka mokwanira, iwo akhoza kumupeza Iye kumbali imeneyo, pokhala ophweka. Koma malingana ngati iwe ukupita ku nzeru, iwe ukupita kutali ndi Iye.

⁶² Tsopano ndiroleni ine nditenge zimenezo kuchitira kuti musaziphonye izo. Malingana ngati ukuyesetsa kuti umupeze Mulungu mwa nzeru, monga izo zinali mmunda wa Edeni, monga izo zinali mmasiku a Mose, monga izo zinali mmasiku a— a Nowa, monga izo zinakhalira mmasiku a Khristu, mmasiku a Yohane, mmasiku a atumwi, ndipo mpaka ku tsiku lino! Pamene iwe uyesetsa kuchilingalira Ichu, ndi kuyesetsa kumupeza Mulungu mwa nzeru, iwe ukupita kutali kuchoka kwa Iye nthawi zonse. Iwe ukuyesetsa kuchimvetsa Ichu. Palibe njira yochitira zimenezo. Ingochirandirani Ichu. Mukuona? Ingochikhulupirirani Ichu. Musamayesere kuchimvetsa Ichu.

⁶³ Ine sindingakhoze kumvetsa chifukwa, chimene, chabwino, zinthu zambiri. Si zinthu zambiri zimene ine ndimazimvetsa kapena ndingakhoze kuzimvetsa. Ine sindingakhoze kumvetsa momwe mnyamata wamng'ono uyu wakhala apayu amadya chakudya chomwecho chimene ine ndimadya, ndipo—ndipo, apa iye ali, ali ndi mutu wodzaza ndi tsitsi, ine ndiribe lirilonse. Ine sindimazimvetsa zimenezo. Iwo amandiuza ine kuti kashiyamu amapanga ilo; ndipo ndikadula zikhadabo zanga sizimachedwa kumerera, ndipo wopanda tsitsi nkomwe lakuti ndilidule. Ine—ine sindimamvetsa zimenezo. Monga mwambi wakale uli, ine . . .

⁶⁴ Osati kukhala ngati ndisinthe malowo, kutsimikizira kwake; koma, Iko ndi kutsimikizira, koma ine sindinafike ku Chisindikizochi panobe.

⁶⁵ Momwe ng'ombe yakuda ingakhoze kudya msipu wobiriwira, ndi kumapereka mkaka woyera, womwe umapanga batala wa chikasu! Ine—ine ndithudi sindingakhoze kufotokoza zimenezo, mwaona. Chifukwa, inu mukuona, chirichonse ndi chotuluka mwa chinacho. Ndipo momwe izo zimachitira, ine sindingakhoze kufotokoza zimenezo.

⁶⁶ Sindingakhoze kufotokoza momwe akakombo awiri amaimira, kapena maluwa awiri, amtundu wofanana, ndipo lina lofiira, ndi linalo la chikasu, ndipo lina la bulawuni, ndi lina la buluu. Ine sindimazimvetisa zimenezo. Dzuwa lomwelo pa iwo. Kodi mtunduwo umachokera kuti? Mukuona? Ine—ine sindingakhoze kuzifotokoza zimenezo, komabe iwe umayenera kuzivomereza izo.

⁶⁷ Ine ndimangokhumba kuti wina wafioloje wamkulu afotokoze kwa ine momwe dziko ili limaimira mu mlengalenga. Ine ndikukhumba inu mukanakhoza mwasayansi kundiponyera ine mpira mu mlengalenga, ukuzungulira, ndipo nkuwulola iwo kuti upange kuzungulira kawiri, mmalo omwewo. Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Ndipo komabe ili ndi loyikidwa mwangwiro kwambiri mwa nthawi mpaka iwo amakhoza kudziwa kadansana wa dzuwa pa miniti, zaka twente kuchokera pano. Iwo alibe wotchi kapena koloko, kapena chidutswa chirichonse cha makina, chomwe chiri changwiro chomwecho. Ndipo komabe ilo likuyima pamenepo. Ndipo, ndiye, litapendekera chammbuyo. Bwanji ngati ilo litadziwongola pang'ono pokha? Eya. Iwe ungangodzipusitsa wekha, kuti uyesere, mwaona.

⁶⁸ Kotero, mukuona, musamayesere kuti mupeze nzeru, kuti mumvetsetse. Musingokhulupirira zimene Iye akunena. Ndipo mophweka kwambiri momwe inu mukumvera, ndiye kuti mwafikapo, inu mudzachipeza Icho. Tsopano, ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha chimenecho, wothokoza kuti Iye ali, wadzipanga Yekha kukhala wophweka. Tsopano, ife tikupeza, mutu wa 6 ndi ndime ya 9. Ndiroleni ine ndiyambe tsopano.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona panso pa guwa miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni... iwo anawugwira:

⁶⁹ Zindikirani, apo palibe kutchula kwa Chamoyo china, kapena chamoyo—Cholengedwa chamoyo, ku kulengeza uku kwa Chisindikizo Chachisanu. Tsopano kumbukirani, chinalipo, pa Chisindikizo Chachinayi. Chinalipo, pa Chisindikizo Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, ndi Chachinayi, koma palibe apa. Mukuona?

⁷⁰ Tsopano, ngati inu mungazindikire, tiyeni tingowerenga mmbuyo, chimodzi cha Zisindikizozo. Tiyeni tibwerere ku Chisindikizo Chachinayi, mwaona. Ndipo ndiyo ndime ya 7.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachinayi, ine ndinamva liwu la chamoyo chachinayi chikuti, Bwera . . . udzawone.

. . . pamene iye . . . anatsegula chisindikizo chachitatu, ine ndinamva liwu la—la chamoyo chachitatu chikuti, Bwera ndipo udzawone.

. . . la chamoyo chachiwiri . . . Bwera . . . udzawone.

. . . ndipo chamoyo choyamba chinati, Bwera ndipo udzawone.

⁷¹ Koma ndiye pamene ife tikufika ku Chisindikizo Chachisanu, apo palibe Chamoyo. Tsopano tangozindikirani.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansu pa guwa . . .

⁷² Mwamsanga ndithu! Mwaona, apo palibe—palibe Chamoyo pamenepo. Ndipo Chamoyo chimaimira mphamvu. Ife tikudziwa zimenezo, mwaona. Apo palibe Cholengedwa chamoyo.

⁷³ Tsopano, chimodzi cha Zolengedwa zimenezo, ife tikupeza, mu kuphunzira kwa—kwa—kwa vumbulutso mmipingo, kuti chimodzi cha izo chinali ndi . . . chinali mkango; ndipo chinacho—chinacho chinali ng'ombe; ndipo chinacho chinali munthu; ndipo china chinali mphungu. Ife tinapeza Mmibadwo ya Mpingo kuti Zamoyo zinayi izo, kutanthauza mphamvu zinayi, zimasonkhana pozungulira Machitidwe a Atumwi, basi monga momwe uja—kachisi mu chipululu. Ndipo inu mukumvetsa zimenezo, chifukwa ine sinditenga nthawi kuti tilowe mu zimenezo. Momwe ife tinazijambulira izo apa, ndipo tinawonetsa ndendende basi! Iwo anali kuyang'anira pa Izi, Mwanawankhosa ndi Mawu, kuti achite Mawu basi monga momwe iwo ankachitira—likasa la pangano mu Malo Oyera mu chipululu, ndi zina zotero.

⁷⁴ Tsopano, ife tinawonetsa ngakhale malowo, mwa mitundu ya mafuko a Israeli, ndi mwa . . . Ndi angati anamvetsera—Mibadwo Isanu Ndi Iwiri ya Mpingo? Ine ndikuganiza pafupifupi, theka, magawo awiri pa atatu a inu. Zindikirani, kuti ngakhale chikhalidwe cha Chamoyocho chimakhala ndendende chizindikiro cha fukolo, mbali yomwe zinayizo . . . mafuko thwelovuwo amakhala, anayi ku mbali iliyonse, kapena—kapena mafuko atatu ku mbali iliyonse. Ndipo Zamoyo zinayizo zimakhala ndi kumayang'anira, mafuko awa, kuchokera kumbali zinayi zonsezo.

⁷⁵ Ndipo, pamene, ife tinapita ndi kukatenga Mauthengawo, ndi kuwonetsera ndendende. Pamene iwe ulowa mu likasa, izo zinali kulondera likasalo, pangano. Ndiyeno ife tinapeza

kuti pangano la Mpingo watsopano, choimira Chake pa dziko lapansi, chinali Mzimu Woyera. Magaziwo anali atatumiza, kwa ife, Mzimu Woyera. Ndipo Zamoyo zinayizo zinkaimira, ndipo monga—mafuko thwelovu a Israeli, pamene izo zinkalondera. Ndipo tinapeza zikhaliidwe zawo, ndipo tinatenga chikhaliidwe chomwecho ndi kuchibweretsa icho kwa uliwonse wa Mauthenga anayi amenewo, ndendende, zinali zofanana ndendende. Chimodzi chinkayankhula kwa mkango, chinacho kwa ng'ombe, ndipo china... Mauthenga Anayiwo! Ndi zimenezo apo. Mauthenga anayi amenewo ndi chitetezero cha Mzimu Woyera. Amen.

⁷⁶ Ine nthawizonse ndimangodabwa... Icho chinandikakamira ine. Tsopano, izi ndi pafupifupi zaka sikisi, ine ndikuganiza, chiyambireni pamene ine ndinamumva munthu wamkulu akunena kuti izo zinali... "Machitidwe a Atumwi anali miyanga chabe." Ine ndazimvapo izo zikuyankhulidwa nthawi zambiri. Koma kumumva mwamuna wa udindo wake, monga mlaliki ndipo monga mphunzitsi, amene analemba ena a mabuku otchuka amene anthu amawawerenga kulikonseko, ndipo nkunena kuti Machitidwe a Atumwi sanali kwenikweni ofunikira kwa chiphunzitso cha Mpingo!

⁷⁷ Pamene, Machitidwe a Atumwi ndi maziko kumene a Iwo; osati miyanga. Maziko! Chifukwa, Baibulo limanena kuti— a—a—maziko a Mulungu "anamangidwa pa Chiphunzitso cha atumwi," kulondola, "Khristu, Mutu, Mwalawapangodya."

⁷⁸ Ndipo pamene munthu uyu anaimirira pamenepo napanga ndemanga imeneyo, ine—ine—ine—ine basi... Mtima wanga unangolephera. Ndipo ine ndinaganiza, "Nzosadabwitsa." Chabwino, ine ndikuwona tsopano, mu Zisindikizo. Izo zinali basi zisanawululidwe. Ndizo zonse. Mukuona?

⁷⁹ Kotero, kuti, apo iwo anali, atayima pamenepo, koma panali chinachake basi chikungonena zimenezo. Tsopano, zindikirani, iwo amalondera.

⁸⁰ Tsopano, pamene ife tinatenga Mateyu 28:19, ndi kuchiyendetsa chinthu chimenecho kutsika kudutsa mu Mateyu, chimene chinkaimira mkango. Ndi kubwera, mkati umo, ife tinadzapeza ndendende chifukwa chimene iwo amabatizira mu Dzina la Yesu Khristu. Ndipo apo Iye anali atayima pamenepo ali ndi Lemba lomwelo, kuti alondere chidaliro chopatulika cha ubatizo wa Dzina la Yesu Khristu. Chabwino. Chabwino, ine ndikuchoka ku mibadwo ya mpingo tsopano.

⁸¹ Zindikirani. Koma, apa, pamene ife tikufika ku Chisindikizo Chachisanu ichi tsopano, apo pali—apo pali—apo palibe wokwera amene akupita, ndipo palibe Chamoyo choti chilengeze Icho. Yohane basi... Mwanawankhosa anatsegula Icho, ndipo Yohane anachiwona Icho. Panalibe aliyense pamenepo wonena kuti, "Tsopano bwera, udzawone. Bwera, udzawone."

Zindikirani, panalibe mphamvu ya Cholengedwa chamoyo. Kapena apo pali...

⁸² Ndipo pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chimodzi, palibe Chamoyo choti chilengeze Ichu; ndipo pa Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri, palibe Chamoyo choti chilengeze Ichu, palibe mphamvu yoti ilengeze Ichu, mwaona, palibe amene akuchita zimenezo. Pa, penyani, pa... Pambuyo pa Chisindikizo Chachinayi, palibe kulengeza kwa mphamvu iliyonse ya Chamoyo, kuyambira pa Chisindikizo Chachisanu, Chachisanu Ndi Chimodzi, kapena Chachisanu Ndi Chiwiri, palibe nkomwe.

⁸³ Tsopano zindikirani, ine ndikuzikonda izi, monga mmene zinaliri mu nthawi za wokwera wa akavalo anayi, wokwerayo, mmodzi, wa akavalo anayi osiyanasiyana, panali Chamoyo chimene chinkalengeza mphamvu. Nthawi iliyonse pamene wokwera akwera kavalo wina ndi kubwera kudzakwera, Chamoyo cha mtundu wina chinkatulukira ndi kudzalengeza izo, “Ndicho chinsinsi chachikulu.” Mukuona? “Ichu ndi chinsinsi.” Chifukwa chiyani? Kulengeza chinsinsi.

⁸⁴ Ndi chifukwa chiyani palibe chimodzi apa pa Chisindikizo Chachisanu kuti chilengeze Ichu? Ndi izi apa, molingana ndi vumbulutso limene Ambuye Yesu anandipatsa ine lero, mwaona, kapena, mmawa uno, molawirira: Ndicho kuti chinsinsi cha mibadwo ya mpingo chatsirizika kale pa nthawi iyi, chinsinsi cha wotsutsakhristu chawululidwa pa nthawi iyi, wotsutsakhristu anatenga kukwera kwake kotsiriza, ndipo ife tinamupeza iye ali pa kavalo wotumbululuka uyu, wosakanizidwa ndi mitundu yake yambiri, ndipo akukwera njira yonse mpaka ku chitayiko (Ife tidzazipeza zimenezo pa Malipenga, ndi zina zotero, pamene tizidzaphunzitsa zimenezo. Ine ndikanapita kwa izo tsopano, koma ife tichoka pa phunziroli kachiwiri. Ndipo ife—ife tizipita... iye akukwera...), ndi chifukwa chake palibe mmodzi aliyense pamenepo.

⁸⁵ Tsopano, ife tikudziwa, zinalembedwa chifukwa pamakhala chifukwa kwa chinachake. Tsopano, inu mukukumbukira, poyambirira, pachiyambi, ine ndinati sipangakhale kanthu popanda cholinga. Mukukumbukira dontho laling’ono la inki? Mukuona? Tsopano, inu muyenera kupeza cholinga.

⁸⁶ Chabwino, pali chifukwa chinachake chimene iwo sanasowe kukhala nacho Chamoyo, kapena mphamvu, kuti ilengeze Chisindikizo ichi chikumatulidwa, ndipo ndi Mulungu yekha amene angakhoze kuwulula chifukwacho, ndizo zonse, chifukwa izo zonse—zonse zagona mwa Iye.

⁸⁷ Koma chifukwa chimene Iye akuwululira Ichu, ine, monga momwe ine ndikuzimvetsera, ndi chakuti ndi chifukwa chakuti chinsinsi cha Bukhu la Chiwombolo, chokhudza wotsutsakhristu chawululidwa, ndipo pa nthawi yomweyo,

Mpingo wapita, ndipo zinthu izi sizikuchitika ngakhale mu m'badwo wa mpingo nkomwe. Uko nkulondola. Izo ziri—izo ziri kutali ndi m'badwo wa mpingo. Mpingo mwamtheradi wakwatulidwa pa nthawi iyi. Mpingo ukupita mmwamba, mu mutu wa 4 wa Chivumbulutso, ndipo sukubwereranso mpaka Iwo ukubweranso limodzi ndi Mfumu Yake mu mutu wa 19. Koma Zisindikizo izi apa zikuwulula zimene zakhala ziripo, zimene ziri, ndi zimene ziti zidzakhale. Mukuona? Ndipo tsopano, zomwe zinali zoti zidzakhale za m'badwo wa mpingo, zinawululidwa ndi Zisindikizo izi. Ndipo tsopano yang'anani zomwe zikutenga Icho.

⁸⁸ A—magawo anayi a wokwera wake awululidwa kale. Magawo anayi a wotsutsakhristu, akukwera, awululidwa pa nthawi ino, kotero iwo sakusowa kukhala nawo enanso.

⁸⁹ Ndipo panali Zolengedwa zamoyo zinayi za Mulungu, kuti zilengeze wokwerayo pamene iye ankakwera. Zamoyo zinayi ndizo mphamvu zinayi. Tsopano, ife tikudziwa kuti *Chinyama*, mwa kutanthauzira kwa manenedwe a zophiphiritsa za Baibulo, chimatanthauza “mphamvu.” Tsopano, tiyeni titenge izo mwatcheru. Zinayizo ndi Zinyama, mu Baibulo, zikuyimira mphamvu pakati pa anthu.

⁹⁰ Tsopano, ngati ife tingapeze, monga mu Daniele, pamene iye anawona fuko linalake likuwuka, izo zikhoza kukhala mwinamwake chimbalangondo chitagwira nthiti mmbali mwake, mophiphiritsa. Kenako iye anawona mphamvu ina ikuwuka, mbuzi. Iyo inkaimira chinachake. Kenako iye anawona mphamvu ina ikuwuka, ndipo—ndipo uyo anali kambuku wokhala ndi mitu yambiri. Iye ankayimira ufumu winawake. Kenako iye anawona ina ikuwuka, mkango waukulu uli nawo mano, ndipo—ndipo unakapondereza zotsalira. Izo zinkaimira mphamvu yosiyana, pamodzi. Umodzi unali u—ufumu wa Nebukadinezara; ndipo wina, mtundu wa—wa loto. Daniele anawona masomphenya; Nebukadinezara analota loto. Koma Daniele anamasulira loto lakelo, ndipo linali molondola ndi masomphenya.

⁹¹ Amen! Pysii! Oh! Ngati inu mukanangodziwa zomwe zinachitika! Chinachitika ndi chiyani ife tisanachoke apa? Inu mukumvetse? Bwanji, maloto sikisi olunjika anabwera mogwirizana ndendende ndi masomphenyawo. Amen! Mukuona? Loto, lomasuliridwa, limakhala masomphenya. Chifukwa munthu mwinamwake posakhala kuti anabadwa ndi chikumbumtima kuti azikhala, ali mmaso pamene iye akuziwona izo, ndiye Mulungu amabwera mu chikumbumtima ichi ndipo amadzayankhula kwa iye. Chimene, Iye analonjeza kuti, mmaloto, mmasiku otsiriza, Iye akanadzawachezera anthu, ndiponso mmasomphenya. Mukuona?

⁹² Tsopano, masomphenya ndi pamene iwe uli chipenyere

mmaso, utayimirira kumene munga chonchi, ndipo zinthu zina nkumawululidwa. Ndi kuyima, nkumawauza iwo kumene za izo; kumawona zomwe zinachitika, ndi zimene ziti zidzakhalepo, ndi zina zotero.

⁹³ Koma, tsopano, loto limakhala pamene iwe ukugona, ndipo mphamvu zako zisanu zisakugwira ntchito, ndipo iwe umakhala—iwe umakhala mu chikumbumtima chako. Iwe umakhala kwinakwake, chifukwa, pamene iwe ubwererako, iwe umakumbukira kumene iwe unali, umakumbukira izo moyo wako wonse. Mukuona? Kotero, ndicho chikumbumtima chako. Ndiye polinga kuti, mwaona. . .

⁹⁴ Monga Congressman Upshaw anakonda kunena kuti, “Iwe sungakhale chinachake chimene iwe siuli.” Ndipo ndicho pafupifupi kulondola basi, mwaona.

⁹⁵ Ndiyeno, ngati iwe unabadwa uli mpenyi, tsopano, mukuona, kuti uchite zimenezo, zikumbumtima zonse izo ziyenera kukhala pamodzi kumene; osati chimodzi chiri *apa* ndi zokhudzira zisanu, zikugwira ntchito, ndipo chinacho chiri *apa* pamene iwe uli chigonere ndipo zokhudzira zisanu izi zisakugwira ntchito. Koma, mukuona, pamene zonsezo, iwe umabadwa, zonse ziri pamodzi pomwe, iwe sumapita kukagona. Iwe umangopita kuchokera ku chimodzi nkupita ku chinacho, munga—munga chomwecho. Iwe sumapita kukagona. Palibe malo okwanira kuti ukagone. Ndipo iwe sungakhoze kudzipanga wekha mwanjira imeneyo.

⁹⁶ Kotero, “Mphatso ndi maitanidwe zimakhala zokonzedweratu ndi Mulungu.” Izo zimakhala—izo zimakhala mphatso za Mulungu ndi maitanidwe, ngakhale “popanda kulapa,” Baibulo linatero. Mukuona? Izo zinakonzedweratu kusanakhale maziko a dziko lapansi. Mukuona?

⁹⁷ Tsopano, tsopano, ife tikupeza kuti, chamoyo, cha Daniele, icho chinkatanthauza kuti iyo inali mphamvu ikuwuka pakati pa anthu. Chabwino. Ndipo—ndipo masomphenya a Yohane apa, nawonso, anawonetsa kuti zinali mphamvu, mafuko akuwuka. Monga, United States amawonekera mu Chivumbulutso 13, munga mwanawankhosa. Ndiyeno ngati iwe ukufuna kudziwa, kusiyana. . .

Inu mukuti, “Chabwino, izo, izo zikuyankhula za mphamvu ya fuko.”

⁹⁸ Izo zimaimiranso mphamvu yoyera, aponso, chamoyo. Kodi inu mumadziwa zimenezo?

⁹⁹ Zindikirani Rabekah; pamene—pamene a—wantchito wa Abrahamu, Elieza. . . Pamene iye anabwera kudzamutenga Rabekah, iye. . . Iye anamukweza iye pa ngamira, ngamira yomweyo imene iye anaimwetsa madzi. Ndipo iye anakwera ngamira iyi, kukakumana naye mkwati wake wosawoneka. Chinthu chomwecho chimene anachimwetsa madzi, chinali

chinthu chimene chinamutengera iye kwawo kwa mtsogolo ndi kwa mwamuna wake.

¹⁰⁰ Ndipo ndicho chinthu chomwecho lero, mwaona. Chinthu chomwecho chimene Mpingo ukuchimwetsa madzi, imeneyo ndi Mbewu, Mbewu ya Mawu. Ndi Mawu omwewo amene akukhala amoyo ndi kudzatinyamulira ife kwa Mkwati wathu wosawoneka. Mukuona? Mukuona?

¹⁰¹ Ndipo taonani momwe zikukhalira mwangwiro. Isaki anali atachoka kwawo, ndipo anali kunja mminda, kutali ndi kwawo, pamene Rabekah anamuwona iye.

¹⁰² Ndipo Mpingo udzakumana naye Khristu mu mlengalenga, ndipo kenako Iye adzamutengera Iye kubwerera Kwawo, Kwawo kwa Atate, kumene nyumba zazikulu zikukonzedwako. Isaki anamutenga Rabekah mwanjira yomweyo.

¹⁰³ Ndipo, zindikirani, icho chinali chikondi pa kuwonana koyamba. Oh, mai! Iye anangothamanga kukakumana naye iye.

¹⁰⁴ Ndipo umo ndi momwe Mpingo udzakumanirane naye Khristu, mu mlengalenga, ndi kukakhala naye Iye kwanthawizonse.

¹⁰⁵ Tsopano, mwamanenedwe a Baibulo, Zamoyo izi ndi mphamvu. Zindikirani. Ine ndikufuna, tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire.

¹⁰⁶ Mdierekezi anali nazo zinayi zake, zikusinthana, zamoyo zamitundumitundu, zoti azikwera akamapita. Iye anali nazo zamoyo zake zinayi. Zimenezo zinali zonse zitatu za izo, zitayikidwa mu mtundu wa chimodzi, ndipo anapanga chimodzi chimenecho a—kavalu wotumbululuka; kavalu woyera, kavalu wofiira, kavalu wakuda. Ndipo ife tinawona, kuti aliyense wa iwo anali gawo la utumiki wake, gawo la mpingo woyambirira umene unali utapangidwa kukhala chipembedzo, ku Nicaea. Mpingo wapachiyambi wa Chipentekoste, pa umene Mzimu Woyera unatsanuliridwapo, ukubwera mmusi, unadzatenga mzimu wotsutsakhristu, unadzapanga bungwe, unabala ana aakazi ena abungwe. Unasintha mphamvu yake, nthawi zitatu, ndi kuziyika izo mwa imodzi, ndipo anapanga kavalu wotumbululuka. Ndipo kenako anadzapatsidwa dzina lotchedwa Imfa, ndipo anamukwera iye kumapita ku Muyaya. Momveka basi monga momwe zingakhali! Tsopano, tsopano zindikirani, iye wapatsidwa uyu—kavalu uyu, ndipo iye akumukwera iye.

Mulungu, Mulungu watero, nayenso, monga nthawi iliyonse...

¹⁰⁷ Tsopano penyani. Pamene wotsutsakhristu anawonekera, poyamba, kodi iye anawonekera mwa chiyani? Kavalu woyera. Mwaona, bwanji, wosalakwa monga iye akanakhoza kukhalira, chiphunzitso chabe mu mpingo. Iwo ankafuna chiyanjano.

Chiyanjano chanu chiri ndi Khristu. Koma iwo ankafuna chiyanjano. Iwo samakhoza basi kupirira nazo izo, iwo ankafuna kuti apeze. . .

¹⁰⁸ Chabwino, inu mukudziwa, monga timagulu tating'ono timawuka mu mpingo. Inu, inu mukudziwa zimenezo, inu azibusa. Mukuona? Iwo, momwe iwo amanenera, “Mbalame za nthenga zofanana.” Koma ngati ife tiri obadwa kachiwiri, abale, iko—sindikio kachitidwe koti tikatenge, mwaona. Ayi. Tsopano, ife—ife—ife. . .

¹⁰⁹ Ngati ife tiwona chinachake cholakwika mwa abale athu, tiyeni ife tingopemphera ndi kuchipereka icho pamaso pa Mulungu, ndi kumukonda munthu ameneyo mpaka ife titamubweretsa iye mu Kukhalapo komwe kwa Mulungu. Mukuona? Ndiyo njira yake, kwenikweni njira yochitira zimenezo.

¹¹⁰ Inu mukudziwa, Yesu anatero. “Mudzakhala mawudzu mmenemo,” chifukwa Yesu anati adzakhala mmenemo, “koma musawadzule iwo; inu mudzazulira limodzi ndi tirigu.” Mwaona, “Ingozisiyani izo zokha.” Iye adzachita. . . Musiyeni Iye adzachte kulekanitsako pamene nthawiyo idzafika. Mukuona? Zisiyani izo zonse zikulire limodzi.

¹¹¹ Zindikirani, pamene chamoyo chinatuluka, wotsutsakhristu anapita pa chirombo, mphamvu yake.

¹¹² Oh, ine ndikuzikonda izi! Ine ndikungoyamba kumverera mwachipembedzo pakali pano, mwaona, mwinamwake kukondoweza. Zindikirani, pamene wotsutsakhristu. . . Oh, amenewo—mavumbulutso amenewo, mu Kukhalapo kwa mpira wa Moto uwo utapachikika pamenepo mchipindamo! Mpaka. . . Oh, m'bale! Ngakhale ine ndakhala ndikuwuwona Iwo, kuyambira ndiri mwana, nthawi iliyonse imene Iwo ufika pafupi ndi ine, Iwo umandiwopsyeza ine. Iye pafupifupi amandiyika ine mu chikhalidwe cha kukomoka. Iwe sumazolowerana nawo Iwo; iwe sungakhoze. Ndi chopatulika kwambiri.

¹¹³ Zindikirani, pamene wotsutsakhristu anapita (zinayi) pa zirombo zake za utumiki, pamenepo, Mulungu anatomiza Chamoyo kuti chikamenyane nacho icho. Mukuona? Tsopano penyani. Ndiye, nthawi iliyonse (chirombocho chinkakwera) pa kavalo wake, wotsutsakhristu ankakwera pa kavalo wake, pa chirombo chake, kuti chilengeze utumiki wake; Mulungu ankatumiza Chamoyo Chake, nayenso, ndipo Iye anali pa Ichu, kukalengeza kumenyana Kwake ndi ichu.

¹¹⁴ Tsopano, Lemba limati, “Pamene mdani abwera mkati monga kusefukira kwa madzi, Mzimu wa Mulungu umadzutsa muyezo womutsutsa iye.”

¹¹⁵ Ndipo kotero pamene mdaniyo anapita kunja monga wotsutsakhristu, Mulungu anatomiza mtundu winawake wa mphamvu kukakumana naye iye. Ndiyeno pamene iwo. . .

116 Iye anapita kunja uko kachiwiri, monga wokwera pakavalo wofiira, mtundu wina, mphamvu ina, utumiki wina; Mulungu anatumiza ina pambuyo pa iye, kukamenyana nayo iyo, kuti akawugwire Mpingo Wake.

117 Anatomiza yachitatu; apanso, Mulungu anatumiza Chake, Chamoyo chachitatu chinabwera ndipo chinalengeza izo.

118 Iye anatumiza yachinayi; Mulungu anatumiza Chake chachinayi. Ndipo kenako wotsutsakhristu anatsiriza, ndipo mibadwo ya mpingo inatha, nayonso, pa nthawi imeneyo. Penyani. Tsopano, oh, izi nzabwino kwenikweni!

119 Tsopano, ife tikuwona kuti mdierekezi akusintho, zinayi—zirombo zinayi, zinkatanthauza mphamvu zimene zinawululidwirako... kapena mphamvu imene iye anaiwulula ku dziko, ndi momwe iwo anathera pa wotumbululuka uyu, “imfa” kavaloyo.

120 Tsopano tiyeni tiyang’ane pa mphamvu za Mulungu, za Zamoyo izi, kuti zikamenyane nazo.

121 Chamoyo choyamba cha Mulungu, chimene Iye anatuluka nacho kukakomana naye wotsutsakhristu, mzimu wotsutsakhristu pamene unali mu kuphunzitsa kwake kokha. Tsopano kumbukirani, pamene wotsutsakhristu anakwera koyamba, iye anali mu utumiki wophunzitsa. Wotsutsakhristu anakwera, koyamba, mu utumiki wophunzitsa. Tsopano yang’anani amene anapita kukakomana naye iye: mkango, Mkango wa fuko la Yuda, amene ali Mawu. Pamene chiphunzitso chake chabodza chinapita, Mawu owona anapita kukakomana naye iye.

122 Ndi chifukwa chake ife tinali naye Irenaeus, ndi Polycarp, ndi—ndi—ndi—ndi anthu amenewo, Martin Woyera.

123 Pamene wotsutsakhristu ameneyo anali kukwera ndi chiphunzitso chake chabodza, Mulungu anatumiza Kuphunzitsa Kwake, Mawu, Mkango wa fuko la Yuda, amene ali Mawu owonetseredwa mwa Mzimu Woyera. Ndi Mzimu Woyera, mmenemo, kuti umuwonetsere Iyemwini, amene ali Mawu!

124 Ndi chifukwa chake Mpingo woyambirira unali ndi machiritso, ndi zozizwitsa, ndi masomphenya, ndi mphamvu, ndi chifukwa chakuti iwo anali Mawu amoyo, mwa mawonekedwe a Mkango wa fuko la Yuda, ukukwera chotuluka kukamenyana nacho chimenecho. Amen! Tsopano inu mwamvetse zimenezo? Iye akutumiza mphamvu yake, wotsutsakhristu; Mulungu akutumiza Yake, Mawu. Wotsutsakhristu, kuphunzitsa kwabodza; Kuphunzitsa kowona kunapita ndi iwo, kukamenyana nacho icho! Tsopano, uwo unali woyamba. Tsopano, uwu unali Mpingo woyamba, wautumwi, umene unapita kukakomana naye iye.

125 Tsopano, chirombo chachiwiri chimene wotsutsakhristu anachitumiza, chinali chirombo chofiira, chimene chinali kuka... chimene iye anakwerapo, chinali chakuti chikachotse mtendere (ndi) kuchokera pa dziko lapansi, ndi—ndi nkondo.

126 Tsopano, chachiwiri chimene chinapita kukamenyana naye iye, chinali Chamoyo cha ng'ombe. Ng'ombe imatanthauza kuvutikira, Chamoyo cha kulemedwa.

127 Ndipo tsopano ngati tingakhoze kungoyima kwa miniti chabe. Ndiroleni ine, eya, ndiroleni ine, basi kuchitira kuti inu mukhale otsimikiza kuti mwaziwona izi tsopano. Tsopano, ndicho cha mtundu umene ungakhale wododometsa pang'ono kwa inu. Koma tiyeni titenge Tiyatira cha apa. Penyani ndipo muwone ngati siuli a—a—Mpingo wovutikira, mwaona.

*Ndipo kwa mngelo wa mpingo wa ku Tiyatira lemba;
Zinthu izi anena Mwana wa Mulungu, yemwe maso ake
ali ngati malawi a moto, ndipo mapazi ake ali monga
mkuwa wonyezimira;*

Ine ndikudziwa ntchito zako, . . .

128 Mwaona, zonse zikukhala ntchito tsopano, mukuona, chifukwa ndicho chimene chinali kukwera naye iye.

*. . . ndi chikondi chako, ndi utumiki, (mwaona, zonse
ziri basi. . .) ndi chikhulupiro, ndi. . . chipiro, ndi
ntchito zako (kachiwiri, kawiri, “ntchito zako”), ndipo
zotsirizazo kukhala zochuluka kuposa zoyambazo.*

129 Mwaona, izo zikuwonetsa kuti, M'badwo wa Tiyatira, wotsutsakhristu atatha kukhazikika pansu ndi kubwera mu M'badwo wa Tiyatira, Mpingo wawung'ono uja sukanachita kanthu koma basi—basi mophweka umangovutika.

130 Ndipo chinthu china, ng'ombe ndi, aponso, ndi Chamoyo cha nsembe. Mukuona? Iwo ankapereka miyoyo yawo mwaulere basi monga iwo akanakhoza kuyipereka iyo, mmibadwo ya mdima, m'zaka chikwi kumeneko zomwe Chikatolika chinkalamulira dziko lapansi. Ndipo iwo ankangolowa mkati momwemo, inde kapena ayi. Iwo sankasamala za kufa. Ngati iyo inali imfa, izo zonse zinali bwino. Iwo ankapita ndi kukafa, mulimonse. Chifukwa chiyani? Mzimu kumene wa m'badwowo!

131 Ndi chifukwa chake iwo, ndi chifukwa chake Irenaeus, ndi chifukwa chake Polycarp, Yohane, Paulo, amuna amphamvu ndi opambana amenewo kumeneko, ankamenyana nacho chinthu chimenecho!

132 Paulo anachiwona icho. Iye anati, “Ine ndikudziwa, kuti pambuyo pa kuchoka kwanga, kuti mimbulu idzalowa pakati panu, abale, nkumadzaphunzitsa zinthu zosokonezeka, ndipo izo zidzakukokerani inu kutali.” Tayang'anani pa mtumwi wamphamvu, wamng'ono, wokalamba uyo atayima pamenepo, nsana wake utamenyedwa utadzaza ndi mikwingwirima,

maso ake akuchita misonzi. Koma iye ankakhoza kuyang'ana patali kuposa chawo...choyang'anira icho akuchiseweretsa kutsidya uko, chimene iwo angakhoze kupenyera zaka zowala mamillioni handiredi ndi twente za kuwala kwa mlengalenga. Iye ankakhoza kupenya mpaka mu Muyaya. Ndi ameneyo uko. Ndipo iye ananeneratu zimenezo ndipo anati ndizo zomwe zikanadzachitika. Ndipo anati, kenanso, anapita mpaka mmusi ku m'badwo wina wakudza. Tsopano zindikirani, ndi ameneyo pamenepo.

¹³³ Potsatira, iye atapita, Yohane Woyera anakhala moyo wotalika kwambiri. Ndipo pamene Yohane Woyera anali kuyesetsa kuti atolere Makalata onse opatulika, atadzozedwa ndi Mzimu Woyera, ndi kuwayika iwo pamodzi kuti apange Baibulo, ufumu wa Chiroma unamugwira iye ndipo anakamuyika iye pa chisumbu cha Patmo. Iye anali kunja uko pa Chisumbu cha Patmo chifukwa cha Mawu a Mulungu. Polycarp anali kumuthandiza iye kuwamasulira Iwo.

¹³⁴ Ine ndinawerenga, tsiku lina, kalata imene Maria iyemwini analemba kwa Polycarp. Ndi kumudzudzula...osati kumudzudzula iye. Koma kumuyamikira iye chifukwa chokhala mwamuna wochirimika yemwe amakhoza kuphunzitsa ndi kuvomereza zophunzitsa za Yesu Khristu, Yemwe anali wobadwa mwa iye, kuchokera kwa Mulungu. Zolemba zake zomwe za Mariya zimene iye analemba kwa Polycarp.

¹³⁵ Polycarp anadyetsedwa kwa mikango, inu mukudziwa. Ayi, iye anawotchedwa. Izo—izo zinali zochedwa kwambiri kwa iwo kuti awumasule mkango mochitira maseweramo, ndipo kotero iwo anangophwasula bafa, nyumba yosambiramo yakale kumeneko, ndi kumuyika iye mu—mu—mu bwalolo ndi—ndi kudzamuwotcha iye.

¹³⁶ Ndipo ali pa panjira yake, akubwera kumeneko, iye anali akuyenda ali ndi mutu wake wozyolika. Kenturiyo wa Chiroma anati, “Ndiwe munthu wachikulire, ndi wolemekezeka bwino. Bwanji iwe osachinyoza chinthu chimenecho?”

¹³⁷ Iye ankangopitirira kuyang'ana Kumwamba. Ndipo Liwu linayankhula kuchokera kwinakwake. Iwo sanakhoze kumvetsa kuti kunali kuti. Linati, “Polycarp, usawope. Ine ndiri ndi iwe.” Uh-huh. Chifukwa chiyani? Iye anali kuyima ndi Mawu amenewo.

¹³⁸ Ndipo pamene iwo anayamba kuwunjika zipapati pa iye, kuti amuwotche iye, panali nyimbo ya Kumwamba inkatsikira pansi. Ndipo—ndipo nyimbo zochokera kwa Angelo ena kwinakwake zinayimbidwa. Iye sanakhoze ngakhale nthawi imodzi kuphethira diso kwa wonyozayo.

¹³⁹ Ndiwo amuna ochirimika. Ndiwo amuna amene angakhoze kuyima. Oferawo mmusi kudutsa mmibadwo, kumeneko,

anavutika moyipa. Koma kodi iwo anali chiyani? Iwo anali pansu pa kudzoza, Mzimu wa Mulungu, mphamvu. Ine . . .

¹⁴⁰ Musayiwale izi, mpingo. Ndipo abale inu, pa tepi, ine ndikufuna kuti muziringalire izi. Anthu angakhoze bwanji kuchita china chirichonse pambali pa mphamvu ya Mulungu imene yaperekedwa kwa iwo? Ine ndiyika bokosi ili apa, kuti liyimire chimenecho. Ngati Mulungu atumiza Mzimu winawake pakati pa iwo, ndicho chinthu chokhacho chimene iwo angagwire nacho ntchito, ndi Mzimu umene ukugwira ntchito pakati pawo. Tsopano titsimikizira kwa inu, mwa mbiriyakale ya Mpingo, ndi mwa—kutsegula kwa Zisindikizo, ndi mphamvu zimene zinamasulidwa; ndipo mupenye, ndendende, Mpingo unkayankhira ku—kudzoza, ndipo iwo sankakhoza kuchita kanthu kena kalikonse.

¹⁴¹ Tsopano, choyamba chinali mkango uja umene unabangula, Mawu angwiro, osakhudzidwa aja.

¹⁴² Chachiwiri, mu Tiyatira, chinali ng'ombe. Ndipo Ichu chinali—cholemedwa . . . Chamoyo cholemedwa. Mundikhululukire ine. Ndipo Ichu chinalinso Chamoyo chansembe. Ndipo kodi sunali ndendende Mpingo wosauka, wawung'ono uja? Roma anali atakhazikika pansu kumeneko, kwa zaka sauzande za mibadwo ya mdima, ndipo chirichonse chimene sichinkavomereza kuti chinali cha mpingo wa Roma chinkayikidwa ku imfa nthawi yomweyo. Ndipo iwo ankachita kuvutikira, ankapita malo ndi malo.

¹⁴³ Inu a Masons, ine ndiyitanira tcheru chanu. Inu mukukumbukira chizindikiro cha mtanda? Tsopano inu—inu mukudziwa chimene ine ndikuchikamba.

¹⁴⁴ Tsopano zindikirani. Tsopano, ngati inu—ngati inu mungazindikire, uko kunali kunyamula ndi kusamalira Baibulo limenelo. Mukuona? Ndipo iwo ankachita kuvutikira pakati pa wina ndi mzake. Ndi zimenezotu, ng'ombe. Ndipo pamene inafika nthawi . . . Ife tinaziwerenga izo usiku wathawu. Mwaona, pamene chinthucho chinapita, ndipo nsembeyo nkubwera, ndipo iwo ankayenera kupita.

Iye anati, “Usapweteke vinyo ndi Mafuta.”

¹⁴⁵ Kodi iwo anachita chiyani? Iwo mololera anapita kumeneko ndipo anakafa. Iwo sankasamala, chifukwa Mzimu wa Mpingo mu tsiku limenelo unali nsembe, kuvutikira. Ndipo iwo ankayenda akubwera momasuka basi momwe iwo akanakhoza kuyendera, atadzozedwa ndi Mzimu wooka wa Mulungu wa m'badwo umenewo, ndipo anafa ngati agonjetsi, nsembe; masauzande kuchulukitsa masauzande, sikisite-eyiti milioni a iwo pa kawundula.

¹⁴⁶ Ng'ombe, nsembe! Oh, mai! Kodi inu mukumvetsa zimenezi? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Chabwino. Zabwino. Tsopano, nsembe, iyo ikanakhoza kugwira ntchito kokha mu

m'badwo umenewo, kuti imenyane nako kutsutsa kwakukulu kwa zaka sauzande uko.

¹⁴⁷ Tsopano, chirombo chachitatu chimene chinatuluka kuchokera kwa mdierekezi, chinali kavalo wakuda uyu. Mukuona?

¹⁴⁸ Tsopano, Chamoyo chachitatu chimene chinatuluka, mphamvu yochokera kwa Mulungu, kukamenyana naye iye, kukamenyana nayo mphamvu za kavalo wakuda, anali munthu, wochenjera, wanzeru, ali nazo nzeru za Mulungu. Inu mukudziwa, munthu ndi wanzeru kwambiri, kuposa chamoyo chirichonse. Mukuona? Iye ndi wanzeru kwambiri, chifukwa iye akhoza kumugonjetsa iye, kwambiri. Iye ndi wochenjera, wothyathyalika. Mukuona? Ndipo iye. . .

¹⁴⁹ A—m'badwo, kuchokera ku m'badwo wa mdima, tsopano kutuluka mu m'badwo wa mdima; tsopano, mbali ina iyi, pamene kavalo wakuda uyu anali kukwera, pamene iwo ankaliipitsa zawo—zawo—zawo—nsembe zawo ndi chirichonse chimene iwo ankachita. Ndipo ndalama zinali basi. . . Oh, inu mukudziwa momwe izo zinkakhalira.

¹⁵⁰ Tsopano, chinthu chotsatira chimene chinatuluka, kukamenyana nacho icho, chinali Chamoyo chokhala ndi nkhope ya munthu; wanzeru, wophunzira, wothyathyalika, wabwino, wodzozedwa ndi Mzimu umenewo wa tsiku limenelo. Inu mukuzindikira zimenezo? Tsopano, iye anapita kukamenyana naye, ndi kuchenjera kwa nzeru za Mulungu limodzi naye. Umenewo unali m'badwo wa kukonzanso, Martin Luther, John Wesley, ndi ena otero. Mwaona, uko kunali kukonzanso. Zwingli, ndi, oh, onse amene, Knox, Calvin, ndi onse amene, mwaona, anatuluka. Uko kunali kuchenjera. Ndipo tsopano, inu penyani, ndendende kuchokera ku m'badwo wa mdima, kuchokera ku kukonzanso, mwanjira iyi, yang'anani, iko kunali kuthyathyalika kwa munthu.

¹⁵¹ Ngati inu mungatsitse mazenera anuwo pang'ono chabe! Ine ndikukhulupirira kuti anthu akukhala ngati atenthedwa pang'ono, eya, mwina mwake, mkati umo. Ngati mutangotsitsira mazenerawo panso pang'ono pokha! Chifukwa, ine ndikudziwa, ngati ine ndaima pano ndikulalikira, ndikumva kutentha, ine ndikudziwa kuti inu muyenera kutero, kumenekonso.

¹⁵² Chabwino, zindikirani, iko kunali kuthyathyalika kwa munthu. Tsopano, kodi inu mukumvetsetsa?

¹⁵³ Chirombo chachitatu chimenecho chimene Satana anachitumiza, iye anadzakhala wothyathyalika, nayenso. Yang'anani, "Muyezo wa tirigu wogula ndi ndalama. Miyezo itatu ya barley yogula ndi ndalama." Mukuona? Oh, mai! Mukuona? Njira yopangira-ndalama, kuthyathyalika, kuti atenge golide wa mdziko, ndi chuma, zinabweretsedwa mmenemo. Ndizo ndendende kuti akwaniritse. Ndicho

chimene chinayambitsa kulipiritsa mapemphero. Ndipo kwa . . . Anapanga malo otchedwa purigatorio, ndipo ankapempherera makolo awo kuti achokeko. Ndipo, oh, iwe unkayenera kupereka chikalata chaumwini ndi chirichonse, katundu wako. Mpingo, ndi boma, zinali zofanana, ndipo mpingo unkalanda katundu wako.

¹⁵⁴ Ndipo kodi inu simukuwawona, ena a alaliki awa, tsiku lino, akadali nako kudzoza komweko pa iwo? Kuwapangitsa anthu okalamba kupereka mapenshoni awo a ntchito, ndi kulembetsa nyumba zawo pa zinthu zina zake. Bwanji, m'bale, ine—ine sindikufuna kufika ku zimenezo, mwaona. Koma tsopano ine ndikhala kumene ndi chomwechi; ine ndimayang'ana mmbuyo kuti ndiwone kumene ndikupita. Tsopano zindikirani, anthu amenewo, izo ziri ndi iwowo. Izo ziri ndi iwowo. Izo—izo—izo ziribe kanthu kamodzi kochita ndi ine. Ine ndiri ndi udindo pa Izi apa.

¹⁵⁵ Tsopano zindikirani, a—Chamoyo chimene chinabwera kudzamenyana ndi icho, tsopano, chinali munthu. Ndipo ife tonse tikudziwa kuti Chamoyo ichi, cha munthu, mphamvu iyi ya munthu, mu luntha lake, anazindikira kuti mkate uja umene Martin Luther anali nawo mdzanja lake, pamene iye anali kukwera masitepe amenewo . . .

¹⁵⁶ Iwo anati, “*Awa* ndi Magazi a Yesu Khristu. *Ili* ndi thupi la Yesu Khristu.”

¹⁵⁷ Ndipo Luther anaziponyera izo pansi, ndipo anati, “Ndi mkate ndi vinyo. Si thupi la Khristu; chifukwa, ilo linakwezedwa, ndipo likukhala pa dzanja lamanja la Mulungu, likupanga mapembedzero.” Mwaona, nzeru; mwaona, munthu.

¹⁵⁸ Ndipo pamene John Wesley anabwera motsatira, Zwingli atabwera, ndi Calvin . . .

¹⁵⁹ Ndipo iwo anawufikitsa mpingo ku malo, pa chitetezero, mpaka iwo sanafune zitsitsimutso zinanso. “Chirichonse chimene chiti chidzakhalepo chidzakhala.” Izo zinali zonse. Ndipo iwo ankangokhala miyoyo ya mtundu uliwonse. Mpingo wa Chilutera ndi wopotozedwa kwambiri, ndi mpingo wa Anglican! Oh, mai! Dziko lonse linadzakhala lovunda, basi monga momwe liliri tsopano. Mipingo inali itapotoza. Pamene Mfumu Henry ya—ya VIII, inadzabwera ku England, ndipo pambuyo pa Maria wamagazi, ndipo zinthu zonsezi zinachitika. Ndipo, kenako, mpingo unali utadzaza ndi chiwawa ndi chivundi. Ambiri akumadzinenera Chikhristu, ndi kumakhala ndi akazi foro kapena faivi, kapena kumachita chirichonse chimene iwo ankafuna kumachita, ndi kumapitirirabe, ndi zonyansa.

¹⁶⁰ John Wesley, powerenga Lemba, akuliyang'ana Ilo, izo zinawululidwa kwa iye kuti Magazi a Yesu Khristu amamuyeretsa wokhulupirira. Ndipo inu . . . simukuyenera . . .

Ndiye kodi iye anachita chiyani? Iye anatuluka mu kukonzanso kwina. Iye anapulumsa dziko mu tsiku lake, monga Luther anachitira. Mukuona? Chinali chiyani icho? Munthu ameneyo, mphamvu ya Chamoyo, ikupita kumeneko.

¹⁶¹ Kumupatsa munthu nzeru, za kumvetsa, kuti chinthucho ndi cholakwika. “Amenewo si Magazi a Yesu Khristu. Iwo si—thupi la Yesu Khristu. Iwo ukuyimira thupilo.” Mukuona?

¹⁶² Iwo ukadali mkangano waukulu pakati pa Akatolika ndi Achiprotestanti tsopano. Ndicho chinthu chokhacho chimene inu simungakhaliye pamodzi nacho pakali pano. Pa china chirichonse, iwo akhoza kukhalira limodzi, koma chimenecho; izi mmabungwe amenewo akumakhala nazo. Zindikirani tsopano. Koma, ichi, koma iwo—iwo sakanakhoza kusunkhana limodzi pa chimenecho. Mukuona?

¹⁶³ Mmodziyo, “Ndi Magazi, ndipo,” amati, “ndi Magazi enieni; kuti wansembe ali nayo mphamvu yosintha mkate uwu kukhala thupi lenileni la Khristu.” Ndicho chimene kachisi wamng’ono ali, mu—mu—mu mpingo, inu mukudziwa. Ndi chifukwa chake iwo amapanga zizindikiro ndi nsembe yachikunja yamtundu uliwonse yomwe iwo amachita nayo, inu mukudziwa, ndi kudziweramitsa okha, ndi kuvula zipewa zawo, ndi zina zotero. Izo si za kwa nyumbayo; ndi za kwa mkate uwo umene uli mu—kachisi. Ndipo zindikirani momwe Satana anakokera izo mothyathalika!

¹⁶⁴ Koma, taonani, pa nthawi imeneyo, pa umunthu wa munthuyo, mwaona, Mulungu anayika Mzimu wa nzeru pa munthu, kuti amvetse kuti icho chinali cholakwika. Tsopano, iwo unali woti ukamenyane nacho chirombo chachitatu icho, chimene chinawufikitsa mpingo povunda kwambiri, chimene iye anali kuchikwera, kuti chinali chowopsya. Okonzansowo, kodi iwo anachita chiyani pamenepo, iwo a mu m’badwo wa okonzanso? Iwo anawubweretsa Mpingo, kuchokera ku miyambo yake yachikunja yopembedza mafano, nkubwerera kwa Mulungu kachiwiri. Mukuona? Ndicho chimene Chamoyocho chinatulukira, kuthyathyalika kumeneko kwa munthu, wokwerayo, kukachita zimenezo.

¹⁶⁵ Tsopano, koma, werengani tsopano ndime ya 3 ndi... kapena, Chivumbulutso 3:2, miniti yokha. Tsopano, ine ndazilemba izo apa pa chifukwa chinachake. Tsopano izi ndizo, zikulowa mkati tsopano, m’badwo wa Chilutera, mu m’badwo wa okonzanso, wa Chivumbulutso 3:2.

¹⁶⁶ Chimene iwo anachita, iwo anapanga bungwe. Mwamsanga pamene Luther anawuyambitsa mpingo wake, iwo anawupanga iwo bungwe. Chabwino, chinthu chomwecho Wesley anachita. Chinthu chomwecho Chipentekoste chinachita, chimodzimodzi, anawupanga bungwe iwo. Ndipo iwo akuchita chiyani? Iwo

akumatenga kachitidwe komweko kamene iwo anatulukamo. Mukuona?

¹⁶⁷ Tsopano penyani izi, Chivumbulutso, akuyankhula za mpingo wa Sarde uwu. “Kwa mngelo wa mpingo,” imeneyo ndi ndime ya 1, ndithudi. Mukuona? Chabwino.

Khala woyang'anira, ndipo limbitsa zinthu zimene zatsalira,

¹⁶⁸ Amenewo ndi, “Mawu amene iwe waphunzitsidwa,” mukuona, “zinthu zimene zatsalira.”

...zimene zakonzeka kuti zife:...

¹⁶⁹ Iye ali pomwepo wakonzeka kuti ayambe kubwerera mu bungwe basi munga mpingo wa Katolika kumene iye anatulukako. Mukuona?

...pakuti ine sindinapeze ntchito zako zangwiro pamaso pa Mulungu.

¹⁷⁰ Ndi zimenezotu. Apo pali...Apo iye akupita, kubwerera mmbuyo momwe kachiwiri. Kodi inu simukuwona chifukwa chimene kachitidwe ka bungwe kali kolakwika? Anayambitsa iko ndi ndani? Kodi anali Mulungu? Kodi anali atumwi? Mpingo wa Roma Katolika unachita zimenezo. Tsopano mungomulola wazambiriyakale aliyense anene mosiyana. Kulibeko kumeneko. Iwo ali, iwo amati iwo ndi manthu wa mpingo, ndipo iwo ali. Koma anachipanga bungwe chinthucho, ndipo anayikamo kachitidwe, ndi utsogoleri wa munthu kwa icho. Ndipo sitinamutenge munthu mmodzi, munga iwo anachitira; ife tinatenga gulu lonse la anthu, kuwayika iwo pamodzi, ndiyeno inu munasokonezeka kwenikweni. Uko nkulondola. Bungwe lingakhoze bwanji, mulimonse?

¹⁷¹ Basi ziri munga, ife timaganiza kuti demokalase ndi yolondola. Ine ndimakhulupirira kuti iyo ili, nanenso, koma iyo siyidzagwira ntchito molondola. Iyo siyingakhoze. Ndi gulu la ma Ricky kuno kuti aziyiyendetsa iyo, mungakhoze bwanji mdziko kuyipangitsa iyo kukhala yolondola? Inu simungakhoze. Zindikirani, chinthu chenichenicho chinali mfumu yaumulungu.

¹⁷² Zindikirani Chamoyocho, Chamoyo chachitatu, tsopano, chinali kuthyathyalika kwa munthu. Ndipo iye ankaimira okonzansowo amene anatulukira.

¹⁷³ Kuchokera ku fano, la kutenga, kumati, “Uwu ndi mkate.” “Uyu ndi vinyo.” Mwaona, wotsutsakhristu akadali nacho chinachake choyimira Chikhristu. Iye ayenera kutero, chifukwa iye ndi “wotsutsa,” mukuona. Ndiyenyo, ngati iye ayenera kukhala wotsutsa chinachake...

¹⁷⁴ Tsopano, ngati atabwera njira yonseyo, nkudzati, “Oh, ndine wa Buddha.” Chabwino, icho chiribe chochita chirichonse. Iwo onse amatero. Ameneyo ndi wachikunja basi, kuyamba ndi kuyamba.

175 Koma wotsutsakhristu ndi wotheathyalika. Iye ali nayo mitundu yonse ya zinthu zimene zimayimira Chikhristu kumeneko. Kokha kuti, wazitengera izo kumbali ina, chinachake chotsutsa Chiphunzitso chapachiyambi cha Izo. Mwaona, ndicho chimene chimamupangitsa iye kukhala wotsutsakhristu. Mukuona?

176 Koteru, okonzansowo, pamene Chamoyocho chinapita mmawonekedwe a—a munthu, kukamenyana nacho icho!

177 Tsopano, musayiwale ichi, kalasi! Musayiwale ichi! Mukuona? Muzikumbukira Zimenezo, masiku onse a moyo wanu! Mukuona? Zamoyo izi zikukhoza. Izo ndi PAKUTI ATERO AMBUYE. Mukuona?

Zindikirani, kupembedza mafano kunabweretsa . . .

178 Chamoyo chonga munthu chinapita ndi mphamvu ya Mulungu, mwa nzeru zimene Mulungu anamupatsa iye, ndipo anawubweretsa Mpingo kuchoka ku kupembedza mafano, kubwerera kwa Mulungu. Koma mu . . .

179 Iye tikupeza, mu m'badwo wa mpingo womwewo, pamene iwo anayamba kupanga chipembedzo, kuti achite chinthu chomwecho chimene iwo anachichita pachiyambi, chimene Roma anachichita, tsopano iye apanga ana aakazi kwa mpingo umenewo. Ndipo kodi mkaziyo akuti chiyani?

180 Anati, “Tsopano pakuti ndiwe . . . Ine sindinakupeze iwe wangwiro. Ndipo uyenera kulimbitsa mphamvu zapang'ono izo zomwe iwe watsala nazo.” Tsopano mvetserani kwa Iye akuwachenjeza iwo, mu Chivumbulutso apanso, 3:3. Tiyeni titenge . . . Chabwino, ine ndikukhulupirira kuti ine ndinazitenga zimenezo, maminiti pang'ono apitawo.

Kumbukira kuchokera momwe iwe unalandirira ndi kumva, ndipo ugwiritsitse, ndipo ulape.

181 Basi, mwanjira ina, “Kumbukira kuti iwe unachokera ku chivundi chonga chimenecho.” Mukuona? Ndipo taonani apa.

. . . Chotero ngati iwe suyang'ana, Ine ndidzabwera kwa iwe ngati mbala, (uh-huh), ndipo iwe udzadziwa . . . ndipo iwe sudzadziwa ora limene Ine ndidzafika pa iwe.

182 Mpaka mmusi, Iye adzasuntha choyikapo nyalicho, mwaona. Chotero, ndi zimenezotu. Ndi chiyani chimenecho? Kuwala kwa Mpingo.

183 Ndipo iye anapita kumene mu kachitidwe kabungwe komweko ka mdima wachikunja kamene iye anatulukamo, ndipo uko iye adakali chonchobe lero, ndipo anthu owona mtima akumaganiza kuti ndicho Choonadi, chimodzimidzi basi momwe aliri Akatolika. Ndipo Achiprotestanti amawaseka Akatolika; pamene, iwo ndi sikisi kwa mmodziyo, ndi theka la

dazeni la winayo, ndendende, molingana ndi Mawu. Nzeru za munthu!

¹⁸⁴ Tsopano zindikirani. Oh, momwe ine ndimazikondera Izi! Mvetserani kwa Iye tsopano akuwachenjeza iwo. Tsopano, tsopano ife... Inu mwangwiro mukuvomereza, aliyense wa inu? Tsopano, ngati simukutero, mundilembere ine funso. Kuti, Zamoyo zimenezo zikuzindikiritsidwa ndendende mu m'badwo uliwonse, monga Baibulo lazizindikiritsira izo apa. Ndizo ndendende zomwe iwo anachita kumeneko. Mbiri yakale ikuwonetsa zomwe iwo anachita. Ife tikuyang'ana pomwe apa ndi kuwona zomwe iwo anachita.

¹⁸⁵ Ndipo apa, Zamoyo zimenezo, ine—ine—ine sindinkazidziwa izo mmbuyomo. Ine ndinali nditangokhala pamenepo. Ine ndimakhoza kuziwona izo zikuyenda kuntunda uko, chimodzimodzi basi monga momwe inu mukuyang'anira pa ine. Mukuona? Ndipo izo ziyenera kukhala zoon, chifukwa ziri pomwe apa ndi Baibulo. Kotero iwe ungachite bwanji china chirichonse kupatula kunena kuti izo nzolondola? Zindikirani.

¹⁸⁶ Tsopano, Chamoyo chachinayi, chimene chinatumizidwa kukamenyana naye wotsutsakhristu, mu Chamoyo chotsiriza ichi. Kodi inu mwakonzeka? Chamoyo chotsiriza chimene chinatumizidwa, kapena mphamvu yotsiriza kuti ikamenyane naye wotsutsakhristu amene anali kutsutsa kuphunzitsa kwa Mulungu, wotsutsakhristu, inali mphungu. Mukuona? Challengedwa Chamoyo chachinayi chinali mphungu. Tsopano, ingowerengani mibadwoyo, werengani Malemba. Ndi mphungu! Ndipo mu Baibulo, m'badwo wotsiriza unali m'badwo wa mphungu. Ndipo Mulungu amafanizitsa aneneri Ake ndi mphungu. Mukuona? Izo... Tsopano penyani. M'badwo wotsiriza, m'badwo wa mphungu, a—woulula wa Mawu owona. Mukuona?

¹⁸⁷ Mulungu asanasunthe kuti achite kanthu, monga Iye anachitira mmasiku a Nowa, Iye anatumiza mphungu. Pamene Iye anabweretsa Israeli, ndipo ankondo a Farao atakonzeka kuti azipita, Iye anatumiza mphungu. Nthawi iliyonse, Iye amatumiza mphungu potsiriza, pa mapeto a izo.

¹⁸⁸ Ndipo apa Iye akutumiza mphungu, kenanso. Ndizo ndendende ndi Mawu. Kotero inu mungachipange bwanji icho kukhala chinachakenso? Amatumiza mphungu, (chifukwa chiyani?) woulula wa Choonadi chomwe chakhala chikugwa konseko kudutsa mu m'badwo.

¹⁸⁹ Chotero ikanakhoza motani mdziko a—ng'ombe, kapena—kapena munthu, kapena Chamoyo chirichonse chimene anali kukwera, izo zikanakhoza bwanji kuwululidwa kupatula mphungu itadzabwera? Izo zinali ndi malo awo; izo zinali Zamoyo zaumulungu, zotumidwa, mofanana basi monga anali wina aliyense.

¹⁹⁰ Mkango, umenewo unali chiyambi. Apo ndi pamene wotsutsakhristu uyo anatulukira mu—mu kulimbana.

¹⁹¹ Kenako iye anadzutsa mphamvu ina; Iye anatumiza mphamvu kukakumana nayo iyo.

¹⁹² Kenako iye anadzutsa mphamvu ina; Iye anatumiza mphamvu ina kukakumana nayo iyo.

¹⁹³ Ndipo kenako pa mphamvu yotsiriza, Iye akubweretsa pansi mphungu, “Kudzabwezeretsa ana kuti abwerere ku Chikhulupiriro chapachiyambi kachiwiri, cha makolo awo.” M’badwo wa mphungu! Ndiye, mukuzindikira, kulibenso Zamoyo. Ndizo zonse za izo. Amenewo ndi mapeto. Tsopano, ngati inu mungatenge tsopano Chivumbulutso 10:1, 7. Ine ndakhala ndikulozera kwa iwo. Kumbukirani, mu m’badwo wa mtumiki wotsiriza, mwaona, chimayenera kudzachitika ndi chiyani? “Zinsinsi zonse za Mulungu zikanadzaululidwa.” Mphungu! Ameni!

¹⁹⁴ Tsopano inu mukuona zamoyo zinayi zimene zinakwera. Izo zinali zoonu mwangwiro. Kodi mukuzikhulupirira zimenezo? Ndipo tsopano apa pali m’badwo uliwonse, kapena mphamvu iliyonse imene inakwera pambuyo pa iwo. Ndipo pamenepo pali Lemba limene likuwonetsa chimene mdani wokwerayo anachita. Zimenezo zawululidwa mu Zisindikizo izi. Ndiponso zawululidwa tsopano kuti Chamoyo chirichonse, mphamvu imene Mulungu anayitumiza, kukamenyana nayo, zikugunda ndendende pa dontho, mpaka ku nthawi ya mphungu. Tsopano, ngati iyi ili nthawi yotsiriza, kudzabwera mphungu, kulondola, ndipo kwa iyo. Tsopano, kumbukirani.

¹⁹⁵ Tsopano, mmasiku amene mkango uwo unabwera, Mawu apachiyambi, pafupifupi mmodzi pa handiredi a iwo anamvetsera kwa mkango.

¹⁹⁶ Mmasiku amene a—ng’ombe inabwera, kadontho kakang’ono chabe ka iwo anamvetsera kwa uthenga wa ng’ombe.

¹⁹⁷ Mmasiku amene a—munthu unabwera, iye anagwira ntchito pakati pa anthu, inu mukuona, kotero Iye anali wothezathyalika. Iye anatulutsa kagulu kakang’ono.

¹⁹⁸ Ndipo kodi iwo anachita chiyani? Satana anachiwona icho, kotero iye anangowatumiza iwo mmbuyo kumene ndi kukawakwatitsa iwo mu icho.

¹⁹⁹ Ndipo kumbukirani, pamene mphungu potsiriza ikubwera, adzakhalapo gawo limodzi pa handiredi la wani peresenti amene ati adzamvetsere. Iwo ndi m’badwo wa mphungu. Kumbukirani, ndi okwera ena onsewa... Ndiyeno ngakhale Yesu ananeneratu, “Ngati Iye akanapanda kufulumizitsa Kudza Kwake, sipakanadzakhala mnofu uliwonse, nkomwe, wopulumutsidwira Mkwatulo.” Kodi ndi Lemba limenelo?

Inu mukuona pamene ife tiri ndiye, sichoncho inu, m'bale ndi mlongo? Mukuona pamene ife tiri?

²⁰⁰ Mulungu, ndine wokondwa kwambiri, ine—ine—ine sindikudziwa choti ndichite! Koma ine... Uyu si ine basi ndaima pano ku—kuti ndiyankhule. Ine ndiri muno, nanenso. Ine, ine ndiri pakati panu. Mwaona, ine, Ndi ineyo. Ine ndiri ndi banja. Ndipo ndiri nawo abale ndi alongo amene ine ndimawakonda. Ndipo Mulungu wa Kumwamba, wakhala wachifundo mokwanira kubwera pansi ndi—ndi kudzawulula chinthu chimenecho, mwa Ake Omwe... mwa masomphenya amene atsimikiziridwa kwa zaka sarte, ndi Choonadi. Ife tiri pano. Ife tiri... Ife tafika. Ndizo zonse. Kafukufuku wa sayansi watsimikizira Izo. Kutsimikizira kwa Mawu kwatsimikizira Izo. Ndipo ife tiri pano! Ndipo Vumbulutso ili likuchokera kwa Mulungu, ndipo Ilo ndi Choonadi!

²⁰¹ Kodi inu mwagwirapo chirichonse? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ine ndimangodabwa ngati mwatero. Mukuona? Inde, bwana. Ine mwina sindidzasowa kuti ndidzakuwuzeni inu panthawiyo, Lamlungu. Zindikirani. Zindikirani. Zodabwitsa! Tsopano, tsopano, zindikirani tsopano.

²⁰² Ndiyeno molingana ndi—nthawi imene Mulungu anali woti akukawombola dziko la chigumula, Iye anatumiza mphungu.

Ndipo nthawi imene Iye anali kukawombola Israeli, Iye anatumiza mphungu.

²⁰³ Kodi inu mukukhulupirira kuti nthawi, ngakhale pa Yohane, pa chisumbu cha Patmo, Uthenga uwu unali wangwiro kwambiri mwakuti Iye sakanakhoza kumudalira Mngelo kuti awutenge Iwo? Inu mukudziwa, mngelo ndi mtumiki. Koma kodi inu mukudziwa kuti mtumikiyo anali mneneri? Inu mukukhulupirira zimenezo? Tiyeni titsimikizire izo. Chivumbulutso 22, tiyeni tiwone ngati iyo inali mphungu. Eya. Mwaona, iye anali... Ndithudi, iye anali mngelo, iye ndi mtumiki, koma uyo anali mneneri amene anawulula Bukhu lonse ili la Chivumbulutso kwa iye.

²⁰⁴ Chivumbulutso, mutu wa 22 ndi ndime ya 19, ine ndikukhulupirira kuti izo nzolondola ngati ine ndazilemba izo apa... 22:19, ine ndikhoza kukhala kuti ndikulakwitsa. Ayi. [Winawake akuti, “Ndi 22:9, mwinamwake.”—Mkonzi]. 22:9, ndiyo imene ili. Ine ndinali kuyang’ana pa 22:9. Uko nkulondola. Oh, inde, apa.

Ndiye iye ananena kwa ine, Onetsetsa iwe kuti usachite chimenecho: pakuti ine ndine wa antchito amzako, ndi wa abale ako aneneri,...

²⁰⁵ Penyani chimene Yohane anawona apa.

...Ine Yohane ndinawona zinthu izi, ndipo ndinazimva izo.

206 Tsopano iye akutsekera. Uwu ndi mutu wotsiriza.

...Ndipo pamene ine...ndinamva ndi kuwona, ndinagwa pansi kuti ndipembedze pa mapazi a mngelo yemwe anandiwonetsa ine zinthu izi, yemwe anandiwonetsa ine zinthu izi.

207 Ndipo, “iye,” ndiye, “mngeloyo,” mwaona.

Ndiye ananena iye kwa ine, Onetsetsa kuti iwe usachite zimenezo:...

208 Palibe mneneri woona amene angapembedzedwe, kapena mtumiki wa mtundu uliwonse, mwaona. Izo ndi za kwa Mulungu yekha.

Ndiye ananena iye kwa ine, Ona kuti iwe usachite izo ayi: pakuti ndine wantchito mzako, ndi wa abale ako aneneri, ndi wa iwo amene amasunga zonena za bukhu ili: umpembedze Mulungu.

209 Mukuona? Tsopano, Bukhulo linali lofunikira kwambiri, mwakuti, ilo ndi Mawu a Mulungu. Tsopano penyani. Ndipo pamene Mawu a Mulungu abweretsedwa, Iwo amayenera kubweretsedwa ndi mneneri, chifukwa ndi yemwe Mawu a Mulungu amafikirako.

210 Ine ndimayembekeza kudzalandira funso pa zimenezo, mu—mu bokosi ili apa. Ine ndimaganiza kuti ine ndingochita izo iwo asanafikeko, pang’ono pokha, inu mukudziwa. Ine ndikungomverera kuti lirimo limodzi mmenemo longa limenelo, ndizo zonse. Ine—ine ndimangoganiza kuti ine ndingofika kwa ilo, mwaona. Mukuona?

211 Mawu aliwonse a Mulungu amabweretsedwa. Baibulo silimasintha kachitidwe, nkomwe, mwaona. Ndi chinthu chomwecho. Iwo ayenera kubwera kwa mpenyi uyu yemwe ife tikumuyembekeza kuti afike, tsopano zindikirani, Chivumbulutso 10:1, 7.

212 Tsopano tiyeni tiwerenge—ndime ya 9 kachiwiri. Tsopano ife titenge...ife...Tsopano, ife tisanafike ku ndime imeneyo, ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake.

213 Kodi inu mukuona, mwangwiro, ife tisanasiye Zisindikizo izi? Tsopano kumbukirani, palibenso mphamvu zomwe zikutuluka itachoka mphungu imeneyo, mwaona, palibe inanso. Nthawi iliyonse pamene wotsutsakhristu atumiza chinachake, Mulungu ankatumiza mphamvu. Pamene wotsutsakhristu anatumiza mphamvu ina; Mulungu anatumiza chinachake kuti chikamenyane nayo iyo. Kenako iye anatumizanso mphamvu ina; Mulungu anatumizanso chinachake kuti chikamenyane nayo iyo. Mukuona? Ndiyeno pamene Iye anakafika mpaka kwa

mphungu, amenewo anali Mawu Ake, kubwerera monga Iwo anakhalira mmalo oyambirira.

²¹⁴ Tsopano penyani. Kodi si mneneri yemwe ife tikumuyembekezera kuti abwere, munthu wina wodzozedwa ndi—ndi Mzimu wonga wa Eliya? Iye sadzakhala Eliya, ndithudi. Koma iye adzakhala munthu, wonga ameneyo, adzabwera kumeneko. Ndipo utumiki wake womwe ndi woti udzatumize, kudzabwezeretsa, kwa anthu akugwa awa kudutsa mu zopotoka zachipembedzo izi, kubwerera ku Chikhulupiro chapachiyambi cha makolo. Tsopano, ngati icho sichikumangiriza Baibulo limenelo pamodzi, ine—ine sindikudziwa chimene chikutero. Ine—ine—ine sindinganenenso zochuluka za icho, chifukwa ndi chimenecho. Inu mwafika basi. Ndicho Choonadi. Inu mukachotsapo chirichonse pamenepo, inu muchipotoza icho. Mukuona? Kotero, izo—izo zikungoyenera kukhala mwanjira imeneyo.

²¹⁵ Tsopano zindikirani, tsopano, mu ndime ya 9, “Miyoyo pansi pa guwa.” Tsopano, apa ndi pamene ine nditi ndipeze kusamvana kwina kwenikweni. Koma mungoyang’ana miniti yokha. Ndipo basi. . . Mukuona? Ine ndinkaganiza zimenezo, nanenso, koma izo sizinabwere mwanjira imeneyo. Ife takhala. . . Ine ndakhala nthawizonse ndikuganiza kuti miyoyo iyi ya pansi pa guwa anali o—o—ofera a Mpingo woyambirira. Ndipo ndikutsimikiza kuti, chabwino, Dr. Uriah Smith, ndi mmodzi aliyense wa iwo, amati iwo ali. Mukuona? Koma, ine ndinkaganiza chomwecho, inemwini. Koma pamene Mzimu Woyera unadzawonetse masomphenya a izo, izo sizinali; iyo si miyoyo imeneyo.

Tsopano, tsopano inu mukuti, “Chabwino, tsopano, ine sindikudziwa za zimenezo.”

²¹⁶ Chabwino, tsopano, miniti yokha, ife tipeza. Taonani. Iyi si miyoyo ya—ya Mpingo wa Mkwatibwi, ayi nkomwe. Ife tinkaganiza kuti umenewo unali Mpingo wa Mkwatibwi ukuyembekezera uko, miyoyo ya pansi pa guwa, mwaona, ikulira, “Mpaka liti, Ambuye, mpaka liti?” Mundirole ine ndiwerenge zimenezo kachiwiri tsopano, kuchitira kuti tizimvetse izo molondola.

Ndipo pamene iye anatsegula chisindikizo chachisanu, ine ndinawona pansi pa guwa miyoyo ya iwo amene anaphedwa chifukwa cha mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anawugwira:

²¹⁷ Mwaona, “Mawu a Mulungu, ndi umboni umene iwo anawugwira.” Tsopano, musati—musasunthe kuchoka pamenepo. Miniti yokha, mwaona.

Ndipo iwo anafuula. . . Mpakana liti. . . Ambuye, mpakana liti? . . . (mukuona?) . . . woyera ndi woona, muchite inu. . . mukaweruze ndi kukabwezera magari athu pa iwo amene akukhala padziko lapansi?

Ndipo mikanjo yoyera inaperekedwa kwa aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti apumulebe kwa kanthawi pang'ono, kufikira antchito amzawo nawonso ndi—ndi... abale, kuti aphedwe monga iwo anali, ziyenera kukwaniritsidwa.

²¹⁸ Tsopano, pakuti iwo, pa nthawi iyi, ngati inu mungazindikire, Chisindikizo Chachisanu ichi kukhala chikutsegulidwa, mwaona, Mpingo wapita. Iyo siyingakhale basi, miyoyo yapansi pa—Mpingo woyambirira.

²¹⁹ Tsopano, tsopano, chonde, ngati inu munaperekapo tcheru ichi tsopano, chifukwa uwu ndi mtsutso waukulu... mtsutso, kotero ine ndikufuna kuti inu mumvetsera mwatcheru kwenikweni tsopano. Ndipo inu muli nawo mapepala anu, ndi zinthu zoti mulembere nazo. Tsopano, ine ndikufuna kuti inu muzindikire.

²²⁰ Tsopano, iyi siyingakhale miyoyo imeneyo. Chifukwa, a—miyoyo ya o—olungama, ophedwa, ndi anthu olungama, Mpingo, Mkwatibwi, yatengedwera kale mmwamba, kotero iwo sangakhale pansu pa guwa. Iwo angakhale ali mu Ulemelero, limodzi ndi Mkwatibwi. Tsopano penyani. Pakuti, iwo apita mu Mkwatulo, mu mutu wa 4 wa Chivumbulutso. Iwo anatengedwera mmwamba.

²²¹ Tsopano, miyoyo imeneyi ndi iti, ndiye? Ndicho chinthu chotsatira. Kodi iwo ndi ndani, ndiye, ngati iwo siali Mpingo woyambirira? Uyu ndi Israeli yemwe ati adzapulumutsidwe monga fuko, iwo onse amene anakonedweratu. Ameneyo ndi Israeli. Ameneyo ndi Israeli, iyemwini.

²²² Inu mukuti, “Oh, dikirani miniti.” Inu mukuti, “Iwo sangakhale.” Oh, inde, iwo ali woti adzapulumutsidwe.

²²³ Apa, tiyeni tichikhazikitse icho, miniti chabe. Ine ndiri nawo Malemba foro kapena faivi. Ine nditenga limodzi. Tiyeni titenge Aroma, miniti yokha, ndipo tipeze ngati iwo ali. Tiyeni titenge Bukhu la Aroma, ndipo tipite ku—ku mutu wa 11 wa Aroma, ndipo ife tipeza. Basi... Tiyeni tingowerenga pamenepo, ndiyeno ife tidzipezera izo tokha. Aroma, mutu wa 11, ndime ya 25 ndi ya 26. Tsopano mveterani kwa Paulo apa.

²²⁴ Ndipo Paulo anati, “Ngati wina aliyense, ngakhale Mngelo, alalikira uthenga wina uliwonse,” (chiyani?) “Iye anali woti adzatembereredwe.” Yang'anani.

Pakuti sindikanafuna, abale, kuti inu mukhale osadziwa za chinsinsi (uh!), kuti mungadziyese anzeru mwa kudzikiza kwanu (ndi zimenezotu pamenepo); khungu mwa kagawo linachitika kwa Israeli, kufikira kukwaniritsika, chidzalo cha Amitundu chitabweramo.

225 Mkwatibwi wotsiriza wa Amitundu akadzabweretsedwa mkati, kwa Mkwatibwi, khungu linabwera kwa Israeli kwa cholinga chimenecho.

Ndipo chotero Israeli yense adzapulumutsidwa: monga kunalembedwa, Kudzabwera kuchokera mu Zioni Muwomboli, ndipo adzachotsa kupanda umulungu kwa Yakobo:

226 Kulondola! Tsopano, iwo ndi Israeli, amene ali pansi pa guwa ili. Penyani. Israeli anachititsidwa khungu kwa cholinga chomwecho kuti ife tidzapulumutsidwe. Inu mukukhulupirira zimenezo? Tsopano, ndani anawachititsa iwo khungu? Mulungu. Mulungu anawachititsa khungu ana Ake Omwe.

227 Nzosadabwitsa, Yesu, atayima pamenepo pa mtanda, ndipo Ayuda amenewo akulirira Magazi Ake! Amenewo anali ana Ake Omwe. Ndipo Iye anali Lembalo. Iye anali, Iyemwini, Mawu. Ndipo apa, Iye podziwa kuti anthu amenewo akanadzamulandira Iye mokondwera! Ndipo ndi chifukwa chake Iye anawachititsa iwo khungu, kuchitira kuti iwo asamuzindikire Iye. Iye anabwera mwa njira yophweka chomwecho, ndi kuwachitisa khungu iwo kwa icho, kuti iwo asachilandire icho. Mukuona? Lemba linati iwo akanadzachita zimenezo. Ndipo Iye anawachititsa khungu. Anachititsidwa khungu! Yesu anawamvera iwo chisoni, ngakhale mochuluka kwambiri, pamene Iye anati, “Atate, akhululukireni iwo. Iwo sakudziwa chimene akuchita.” Mukuona? Iwo anali akhungu. Paulo anati iwo anachititsidwa khungu kwa cholinga, chifukwa cha ife.

228 Zindikirani. Tsopano ine ndikufuna kuti inu muyang’ane izi mwatcheru kwenikweni. “Iwo anapatsidwa mikanjo.” Iwo analibe iyo. Iwo anapatsidwa mikanjo, mikanjo yoyera, aliyense wa iwo. Tsopano, oyera tsopano ali nayo, ali nayo kale; iwo akuyipeza iyo kuno. Koma, uko, “Iwo anapatsidwa mikanjo.” Ndipo oyera anali nayo kale yawo, ndipo anali atapita kale. Mukuona? Mukuona? Iwo anali—analibe...

229 Iwo, mwaona, iwo analibe mwayi, chifukwa iwo anachititsidwa khungu ndi Mulungu, Atate wawo yemwe; kotero kuti chisomo cha Mulungu chikhoze kukwaniritsidwa, kotero kuti Mkwatibwi akakhoze kutengedwa kuchokera mwa Amitundu. Nkulondola uko?

230 Ndiroleni—ndiroleni ine ndikuwonetseni inu choyimira chokongola apa mwa Yosefe; Yosefe, munthu Wauzimu, mphungu. Iye anabadwa pakati pa abale ake, basi monga momwe Mpingo weniweni uliri pakati pa ina. Ndipo iye ankakhoza kutanthauzira maloto ndi kuwona masomphenya. Ndipo ena onsewo ankamuda iye. Atate ake ankamukonda iye.

231 Zindikirani, ndiye, iye anali kunja, atakanidwa ndi abale ake, osati ndi abambo ake. Kunja, ndi abale ake, ndipo

anagulitsidwa kwa pafupifupi zidutswa sarte za siliva. Anaponyedwa mu dzenje, ndipo nkumaganiziridwa kuti anali atafa.

²³² Anatulutsidwako, ndipo anakaikidwa kudzanja lamanja la Farao. Ndipo chifukwa chakuti iye anakanidwa ndi abale ake, mwaona, iye anapatsidwa mkwatibwi wa Amitundu, osati wa anthu ake omwe. Kupyolera pamenepo, iye anabala Efraimu ndi Manase, omwe anawonjezedwa kwa Israeli.

²³³ Pamene Israeli ankawadalitsa iwo, popingasitsa manja ake, kuchokera kwa wamng'ono kwambiri nkupita kwa wamkulu kwambiri, kupingasitsa madalitso kuchokera kwa Myuda, kubwerera... kapena kuchokera kwa Ayuda kupita kwa Amitundu. Mukuona? Anapingasitsa manja ake, kupita kwa mwana wamng'onoyo, umene uli Mpingo wawung'ono woti udzabweremo. "A—mayi mpingo anayima mu dzuwa; iye anabala mwana uyu." Ndipo zindikirani, kuti amutenge iye, Israeli anapingasitsa manja ake, mwa choyimira. Ndipo Yosefe...

Ana omwewo, anali mayi wa Amitundu.

²³⁴ Mkwatibwi wa Israeli, kumbuyo uko, anapingasitsidwa, kuchokera ku Orthodox yakale, kupita ku njira ya Chikhristu, mwa Mzimu Woyera umene unapingasitsa manja a Israeli. Iye anati, "Mulungu wapingasitsa manja anga." Iye analibe kanthu kochita nacho icho.

²³⁵ Zindikirani. Ndiye, Yosefe, atakanidwa ndi abale ake omwe, anthu ake omwe, anatenga mkwatibwi wa Amitundu. Ndendende basi chimene Yesu anachita; atakanidwa ndi Ayuda, anadzatenga Mkwatibwi wa Amitundu.

²³⁶ Tsopano tiyeni tiwerenge chinachake apa. Ine ndiri nalo Lemba ndalilemba apa, Machitidwe 15. Ndipo, oh, izi ndi basi mtundu wa zomwe ife tiyenera kuziphunzitsa, mulimonse. Tsopano, ine ndikukhulupirira ndiri nazo izi molondola, tiwerenge Machitidwe 15:14. Chabwino. Ine ndikuyembekeza kuti izi ndi za pompano. Chabwino. "Simeon wafotokoza momwe Mulungu..." Ayi, tiyeni tiyambire pa ndime ya 13.

Ndipo atatha iwo kukhala chete, Yakobo anayankha,...

²³⁷ Tsopano, inu mukuona, chimene chinali chitachitika, iwo anali atapita kwa Amitundu. Mukuona? Ndipo mkanganowo unalipo, chifukwa iwo anali Ayuda. Mukuona?

Ndipo atatha iwo kukhala chete, Yakobo anayankha, anati, Amuna ndi abale, mvetserani kwa ine:

Simeoni (ameneyo ndi Simoni Petro) wafotokoza momwe Mulungu poyamba anawachezera Amitundu, kuti akatenge kuchokera mwa iwo anthu kwa dzina lake.

238 Huh! Mwaona, dzina la mkazi wanga linali Broy. Pamene ine ndinkamutenga iye, iye anadzakhala Branham. Mukuona?

239 Yesu akuwutulutsa Mpingo Wake, kapena Mkwatibwi Wake, kuchokera mwa Amitundu. Ndiro Lemba, loimiridwa, chimodzimodzi monga momwe Yosefe anachitira.

240 Tsopano zindikirani izi, tsopano, miyoyo iyi pansi pa guwa. Chabwino, a...iyi, “Miyoyo iyi,” mvetsani tsopano, “yomwe ili pansi pa guwa,” bwanji iwo anaphedwa ndi anthu ochimwa monga Eichmann. Mukuona? Iwo akuyembekezerabe, mamillioni a iwo, mwaona, koma iwo akadali Ayuda.

241 Tsopano, kumbukirani. Chinali chiyani icho? “Iwo anaphedwa chifukwa cha Mawu a Mulungu,” osati chifukwa cha umboni wa Khristu. Kodi inu munazimvetsa zimenezo?

242 Koma, kumbukirani, Mpingo unadzabweramo, nawonso, ofera a Mpingo, zinali chifukwa cha Mawu a Mulungu ndi umboni wa Yesu Khristu. Ndi angati akudziwa zimenezo, apa pa...? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Eya. Chabwino.

243 Tsopano, koma awa analibe umboni wa Yesu Khristu.

... chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndi chifukwa cha umboni umene iwo anawugwira:

244 Ayuda! Ndipo Hitler ankawada iwo, chimodzimodzinso Eichmann, chimodzimodzinso Stalin, ena onse a mdziko. Mukuona? Koma iwo anakhala owona kwa chimene iwo ankachikhulupirira. Ndipo iwo anawapha iwo chifukwa iwo anali Ayuda.

245 Kodi inu mukudziwa kuti Martin Luther anakhala ngati anali nalo lingaliro lomwelo, nayenso? Izo nzoona. Iye anati, “Ayuda onse ayenera kutulutsidwa. Iwo ndi otsutsakhristu.” Mukuona? Koma iye anali basi pansi pa nyengo ina, ndipo sanachiwone icho, sanawawone Mawu.

246 Tsopano Mawu, Choonadi, chikubwerapo. Inu mumuchitisa motani khungu Israeli? Inu simungakhoze kuchita zimenezo. Ayi.

247 Oh, mneneri ameneyo akanakhoza kuyima bwanji pamenepo, tsiku lijali, ndi kudzanena kuti, “Iwe ukuwoneka ngati chipembere, Israeli”? Pamene iwo anali kuyesetsa kuti amuwonetse iye mbali zoyipitsitsa za iye! Iye anati, “Bwanji,” iye anati, “aliyense amene ati adzakudalitse iwe adzadalitsidwa, ndipo aliyense amene ati adzakutemberere iwe adzatembereredwa.” Uko nkulondola. Oh, munthu! Inu mudzachita motani zimenezo?

248 Nthawi ina iwo ankaganiza kuti Mulungu akanakhoza kuyiwala, pamene mneneri anawona chinthu chakuda icho chikubwera kwa Ayuda. Munthu ameneyo atayima pamenepo, ndipo Mawu a Mulungu anatsanuliridwa kwa iye. Iye anati, “O Ambuye, kodi Inu muwataya anthu Anu?”

Iye anati, “Nchiyani icho chagona pambali pako?”

Iye anati, “Ndodo yoyezera.”

249 Anati “Ndi kotalika bwanji kukafika Kumwamba? Tayeza iko.” Uh-huh. “Nyanja ndi yakuya chotani?”

Iye anati, “Ine sindingakhoze kuchita zimenezo.”

250 Iye anati, “Ngakhalenso Ine sindingakhoze, ngakhalenso Ine sindingakhoze kumuyiwala konse Israeli.” Ayi, bwana. Iye sadzamuyiwala iye.

251 Iye anachita kumuchititsa khungu mwana Wake Yemwe. Tsopano, taganizani za zimenezo. Kumuchititsa khungu mwana Wake Yemwe, kuti atipatse ife mwayi, ndipo ife tikuwukana Iwo. Tsopano, kodi zimenezo sizikukupangani inu kumverera pafupifupi wochepa kwambiri mwakuti inu mukanakhoza kukwawira pansi pa buloko ya konkire mutavala chipewa cha magaloni teni, ndipo osaikhudza iyo konse? Ndiko kuchepa kwambiri, inu mukudziwa. Oh, mai! Inde.

252 “Iwo anagwiritsitsa chifukwa cha Mawu a Mulungu.” Iwo anali Ayuda. Iwo anali nawo malamulo awo; iwo anakhala nawo iwo. Mukukumbukira usiku wathawu, tsopano? Mukuona? Iwo anakhala nawo iwo. Ndipo iwo anali Ayuda, ndipo iwo anali nalo lamulo. Ndipo lamulo linali Mawu a Mulungu, ndipo iwo anakhala molondola ndi ilo. Uko nkulondola. “Ndi chifukwa cha umboni umene iwo anawugwira, iwo anaphedwa.” Ndipo apa panali miyoyo pansi pa guwa, Mpingo utapita kale.

253 Tsopano penyani. Iwo anali, mu khungu lawo, atapha Mesiya wawo, ndipo tsopano iwo anali kukolola chifukwa cha chimenecho. Iwo anazindikira zimenezo. Iwo anazindikira izo, izo zitapita kale. Iwo anamuwona Iye pamenepo, pamene iwo anabwera patsogolo pa guwa la Mulungu. Koma tsopano chisomo cha Mulungu chiri kwa iwo.

254 Penyani. Tsopano, iwo sakanakhoza, mwanjira iliyonse, kukhala oyera, chifukwa iwo akanakhala atavekedwa kale mkanjo. Koma apa iwo ali tsopano, basi “miyoyo ya pansi pa guwa, chifukwa cha Mawu a Mulungu, ndi umboni umene iwo anawugwira,” pokhala anthu a Mulungu, Ayuda.

255 Koma tsopano, penyani, chisomo cha Mulungu chikubwera kwa iwo. Ndipo Yesu akuwapatsa iwo, mmodzi aliyense, mwinjiro woyera, (oh, mai, penyani; kutsidya uko, Mpingo utapita kale), chifukwa iwo anali okhulupirika kwa cholinga chawo. Ndipo iwo anachititsidwa khungu, ndipo iwo sanachidziwe icho. Iwo sanachidziwe icho. Iwo anali kusewera ndendende gawo limene Mulungu anali atalidzozzeratu kuti iwo adzalisewere. Ndipo apa, apa, Yohane akuyang’ana uko ndipo akuwona miyoyo ili pansi pa guwa. Tsopano yang’anani, iye akuyiwona miyoyo imeneyo. Yang’anani chimene iye akuwatchesa iwo.

Iwo akulira, “Ambuye, mpaka liti?”

Penyani, “Kanthawi kotalikirapo pang’ono chabe.” Mukuona?

²⁵⁶ Tiyezi tizitenge zimenezo, pamene ife tikupita mmusi, kudutsa mu Lemba momwe tsopano. Iwo akuzindikira kuti anali atamupha Mesiya wawo. Mukuona? Ndipo iwo sankadziwa zimenezo, koma kenako iwo anadzazindikira. Iwo ana—iwo anaphedwa, mowabwezera, kuti alipire zimenezo: pochita kwawo molakwitsa. Ndipo tsopano taonani chinthu chimene iwo ankayenera kuchita! Mwaona, iwo anali olakwa pa kupha, kotero iwo anaphedwa. Mukuona? Iwo anafuula kuti, “Magazi Ake akhale pa ife!” Mukuona? Uko nkulondola. Ndipo iwo anachititsidwa khungu.

²⁵⁷ Tsopano, ngati iwo akanapanda kuchititsidwa khungu; Mulungu akanati, “Asiyeni iwo okha. Iwo siali oyenera.” Koma pokhala kuti iwo anachititsidwa khungu ndi Mulungu, chisomo Chake chinafikira pansi kwa iwo. Amen! Kuyankhula za chisomo chodabwitsa! Ndipo anamupatsa mmodzi aliyense wa iwo mkanjo, chifukwa Israeli yense adzapulumutsidwa, aliyense amene ali nalo dzina lake litalembidwa. Uko nkulondola. Yesu anawapatsa iwo mikanjo.

²⁵⁸ Monga Yosefe anachitira kwa abale ake; choyimira. Penyani, pamene Yosefe anayima pamenepo, ndipo pamene iye potsiriza...Iye anadzizindikiritse yekha pamenepo pa guwa, guwa lake lomwe, mu nyumbayachifumu yake, mpandowachifumu wake. Iye anati, “Aliyense andichokere ine.” Mkazi wake anali mmenemo mnyumbayachifumu; kumene Mkwatibwi ati adzakakhaleko.

²⁵⁹ Ndipo iye anati kwa iwo, iye anati, “Kodi inu simukundidziwa ine?” Hei, iye akuyankhula Chihebri tsopano. “Ndine m’bale wanu, Yosefe.” Oh, mai!

Iwo anati, “Tsopano, oh, iwe utipezeketsa ife.”

²⁶⁰ Anati, “Dikirani miniti. Dikirani miniti. Mulungu anachita zimenezo kwa cholinga. Zinatengera inu kundiponyera ine kunja, polinga kuti apulumutse moyo.” Ulemelero! Ndi zimenezotu pamenepo, ndendende. Anati, “Musati—musadzikwiye nokha.” Mukukumbukira kuti Yosefe ananena zimenezo? Anati, “Musadzikwiye nokha. Chirichonse chiri bwino bwino tsopano. Zonse zatha. Mulungu ananditumiza ine kuno, patsogolo pa inu.”

²⁶¹ Inu mukudziwa, Baibulo linati iwo adzanena kwa Iye, pamene iwo adzamuwona Iye atabwera, adzati, “Kuti, Inu ndinu Mesiya, ife tikudziwa. Koma, koma, nanga bwanji mabala awo?” Mukuona?

²⁶² Iye adzati, “Oh, Ine ndinawatenga iwo mnyumba ya abwenzi Anga.” Abwenzi?

²⁶³ Ndiyenyo pamene iwo ati adzazindikire izo, iwo amene atsalirawo, handiredi ndi forte-foro sauzande, Baibulo linanena kuti iwo adzadzapatula, nyumba imodzi kwa imzake. Ndipo adzatenga masiku, kuti angolira, ndi kubuma, ndi kumayendayenda pansi; kumati, “Ife tinachita bwanji zimenezo? Tinachita bwanji zimenezo? Bwanji, ife tinamupachika Mesiya wathu yemwe.” Anati, kulira monga mmene nyumba ikanachitira chifukwa cha mwana wawo yekhayo, “Ife tinachita bwanji zimenezo?”

²⁶⁴ Ayuda amenewo, ndiwo—ndiwo anthu achipembedzo kwambiri mdziko; osankhidwa a Mulungu. Koma Iye anawachititsa khungu iwo, kuti atitenge ife, ndipo ife tikuchikana Icho. Chiweruzo cha mpingo wa Amitundu ndi chiyani! Ndi inu pamenepo. Mukuona? Kuchititsidwa khungu mwacholinga, ndi Mulungu, kuchitira kuti Iye adzakhoze kutitenga ife, Mkwatibwi wa Yesu. Kuwatenga iwo kuchokera... Mukuona? Ndipo anachifanizitsiratu icho, ndi chirichonse.

²⁶⁵ Tsopano kodi inu mukuona imene miyoyo iyo ili? Iwo si oyera ophedwawo. Amenewo anapita kale. Uko nkulondola. Zindikirani, iwo anali, iwo anali atapita kale. Mukuona?

²⁶⁶ Kotero, awa akupatsidwa mikanjo, aliyense wa iwo. Ndipo tsopano ine ndikufuna kuti inu muzindikire. Koma tsopano chisomo cha Mulungu chikutsikira kwa iwo. Yesu akumupatsa aliyense wa iwo mkanjo woyera, monga Yosefe anachitira, chisomo chake kwa abale ake.

²⁶⁷ Tsopano penyani. Ngakhale iwo anayesetsa kumuchotsa Yosefe, aponso, koma chisomo chake chinafikira kumene kwa iwo. Mukuona? “Oh, zonse ziri bwino. Izo ziri bwino. Inu simunatanthauze kuchita zimenezo. Koma, mukuona, ameneyo anali Mulungu anachita zimenezo. Mukuona? Mulungu anakulolani inu nonse kuchita zimenezo kuti Iye akhoze kundithamangitsira ine kunja, ndi kundibweretsa ine kumusi kuno kuti ndidzakhoze kupulumutsa miyoyo ya anthu, Amitundu awa kuno, kumene ine ndinapezako mkazi wanga. Ine sindikanakhala naye mkazi ngati—ngati ndikanatsalira kumbuyo komwe uko. Tsopano, ine ndikumukonda mkazi wanga. Iye wandibalira ine ana awa kuno.” Ndipo anati, “Ine—ine... Ndipo tsopano—tsopano ine ndikubwera kudzakutangani inu nonse. Tsopano inu nonse mukhala nazo izo mwabwino, nanunso. Ine ndikubweretsani inu kuno. Ife tonse tizidzakhalala limodzi, monga banja limodzi lalikulu.” Mukuona? Mukuona? Mukuona? Anati, “Chinthu chimodzi chimene ine ndikufuna kukufunsani inu. Kodi bambo anga okalamba akadali moyo?” Oh!

²⁶⁸ Ndipo mpenyeni iye, chimene iye anachita kwa Benjamini wamng’ono, amene ali choyimira cha handiredi ndi forte-foro

sauzande, monga ife titi tidzazipeze izo mtsogolomu. Mukuona chimene iye anachita? Iye anangothamangira mofulumira kumene kwa Benjamini, anakagwera pa khosi pake ndi kuyamba kumukumbatira iye. Mchimwene wake wamng'ono amene anali atabadwira mu banjalo iye atapita, mwaona; mwa amayi ake, mpingo woyamba, mpingo wa Orthodox. Handiredi ndi forte-foro sauzande anabadwa Iye atachokako, pamene Iye anali kutali kukatenga Mkwatibwi Wake Wamitundu. Oh, mai! Kodi izo sizikuchita basi chinachake kwa inu? Ndi zimenezo apo. Kotero inu mukuona amene iwo ali? Ndi awo pamenepo.

269 Zindikirani tsopano, ngakhale iwo anayesetsa kumuchotsa Yosefe, chisomo chake chinafikira kwa iwo.

270 Ngakhale iwo anayesetsa kuti amuchotse Yesu, Iye akubwererabe kumeneko, chifukwa iwo anali akhungu, ndipo akuwapatsa iwo, mmodzi aliyense, mkanjo woyera. Iye adzawatengera kumene iwo mkati, kwawo, mulimonse. Sizikupanga kusiyana kulikonse, chifukwa Iye ananena kale, "Ine ndidzawapulumsa iwo onse, mulimonse." Mukuona?

Tsopano ndime ya 10. Zindikirani, iwo anapempha "kubwezera." Mukuona?

271 Tsopano, ngati uyo akanakhala Mkwatibwi, zikanakhala monga Sitefano: "Atate, akhululukireni iwo," inu mukudziwa. Mukuona?

272 Koma awa ndi Ayuda amene angobweramo kumene, mwaona. Iwo anapempha kubwezera. Zindikirani kachiwiri, mwaona, kachiwiri Iye anati... Zindikirani, sikuti... Iye anati, "Ndi abale anu," Ayuda. Handiredi... Tsopano iwo ankafuna kubwezera. Iwo anati, "Oh, ife tikupita kuti... Ife, ife tikufuna kuti Inu mukabwezere mmalo mwathu kumusi uko."

273 Iye anati, "Kanthawi pang'ono chabe, tsopano, kanthawi pang'ono chabe." Pakuti, zindikirani, ndiroleni ine ndiwerenge izo apa. Ziri mu—ndime ya 10. Chabwino.

Ndipo iwo anafuula ndi liwu lokweza, kumati, Mpakana liti, O Ambuye, woyera ndi woona, muleka inu kukaweruzi ndi kukabwezera magari athu pa iwo amene akukhala pa dziko lapansi?

Ndipo mikanjo yoyera inapatsidwa kwa mmodzi aliyense wa iwo; ndipo kunanenedwa kwa iwo, kuti iwo ayenera kupumulabe... kanthawi pang'ono, mwaona, (chiyani?) kanthawi pang'ono, kufikira antchito amzawo...

274 Mukuona? Tsopano ndi chiyani chimenecho? Aneneri tsopano akulalikira kwa Israeli. Mukuona?

...kufikira antchito amzanu nawonso... antchito amzanu ndiponso abale anu, amene ayenera kuphedwa...

275 Mwaona, iwo amene anakonzedweratu kuti adzachitidwe chomwecho. Mukuona?

*...ayenera kuphedwa monga iwo zinawachitikira,
ziyenera kukwaniritsidwa.*

276 Mwaona, mwa kuyankhula kwina, izo zinakonzedweratu kwa iwo. Ndi Malemba, kuti iwo ayenera kuchita zimenezo. “Ndipo ingopumulani kwa kanthawi pang’ono. Tsopano inu muli nayo mikanjo yanu; inu mukupita kwanu; ndipo ingokhalani pamenepo kwa kanthawi pang’ono, mwaona, yembekezani kanthawi pang’ono chabe.”

277 Tsopano zindikirani. Tsopano zindikirani, “Abale anu.” “Abale anu akuyenerabe kuti aphedwe,” chimene chikutanthauza kuti handiredi ndi forte-foro sauzande amene ati adzayitanidwebe mu Chisautso. Ndipo handiredi ndi forte-foro sauzande amene ayitanidwa.

278 Ndikukhumba ife tikanakhala nayo nthawi. Ife mwina tikhoza kudzazitenga izo mawa usiku, ngati Ambuye alola, ife...basi ife tisanalowe kumene mu Chisindikizo china. Mukuona?

279 Komanso, tsopano penyani, iwo ayenera kudzaphedwa ndi wotsutsakhristu. Ife tangodutsamo kumene mmenemo; ndipo zindikirani, mu kukwera kwake kotsiriza, pamene iye akuswa—akuswa pangano limenelo ndi Ayuda awo kumusi uko. Ndipo apo iye akupita. Mukuona?

280 Ayuda awa, handiredi ndi forte-foro sauzande, ndi oti adzayitanidwe ndi mboni ziwiri za Chivumbulutso 11. Tsopano, inu mukukumbukira, iwo anali oti adzanenere.

281 Inu mwawerengapo zimenezo. Ndi angati awerengapo zimenezo? [Osonkhana akuti, “Ameni.”—Mkonzi]. Ndithudi, ife tonse tikulidziwa, powerenga Lembalo.

282 Ndipo iwo adzanenera, mboni ziwiri izi zidzanenera, mu nthawi ya theka lachiwiri la sabata ya sevente la Daniele. Zimenezo ndi zaka zitatu ndi theka zotsirizazo.

283 Mukukumbukira momwe ife tinaitengera sabata ya sevente ya Daniele? Ine ndinati ife tidzaifuna iyo pamene tidzafika mkati umu. Ine sindinkadziwa chifukwa chake, koma ine basi... Chinachake chinandiuza ine kuti ife tikanadzaifuna iyo, ndipo apa ife tiri. Eya. Mukuona?

284 Zindikirani, mu nthawi ya Daniele. Tsopano kumbukirani, Daniele anauzidwa kuti, “Mesiya akanadzabwera,” kalongayo, “Mesiya,” kani, “ndipo Iye akanadzanenera. Israeli anali adakali nawobe masabata sevente otsalira. Ndipo mkati mwa masabata sevente, Mesiya akanadzadulidwa, ndipo nsembe za tsiku ndi tsiku zikanadzachotsedwapo.” Nkulondola uko? “Koma zinalipobe zaka zitatu ndi theka, zoyikidwiratu.”

285 Mu kampata aka, Iye akutenga Mkwatibwi Wamitundu, tsopano, Mkwatibwi akupita mmwamba, ndipo pamene Iye akupita mmwamba, aneneri awiri akuwuka kwa Israeli. Mukuona?

286 Ndipo miyoyo iyo yomwe yakhala itaphedwa, tsopano, kutsika kudutsa apa, enieni, Ayuda owona kudutsa pamenepo, amene anali nalo dzina lawo pa Bukhu, amene ankakhala moyo wolondola ndi kumachita chinthu cholondola, ankakhala moyo wa Chiyuda mpaka pa dontho. Iwo, iwo anaphedwa ndi Eichmann ndi ena ambiri. Anthu owona mtima, mamillioni a iwo kumusi uko! Ndi Achijeremani aja anawawombera iwo mpaka kufa, ndi kuwazinga iwo, ndi kuwapha iwo, ndi kuwapachika iwo pa mipanda, ndi kuwatentha iwo, ndi kuwawotcha iwo, ndi china chirichonse. Hitler wopandamagazi, kapena wa mtima-wamagazi, wanjala uja, ndi Stalin, ndi Mussolini, ndi anthu onse amenewo amene ankawada Ayuda awo!

287 Ine ndikuganiza kuti ndicho chimodzi cha—chimodzi cha zinthu zomwe zikuligwira fuko lino pamodzi, chifukwa iwo nthawizonse akhala akumulemekeza Myuda, uko nkulondola, anamupatsa iye malo. Iwe ukamulemekeza Myuda, ndipo Mulungu adzakulemekeza iwe.

288 Tsopano, pali gulu la Ayuda amene ali zigawenga, chimodzimodzi basi monga pali Amitundu omwe ali mwanjira yomweyo.

289 Koma Myuda weniweni, Mulungu anayika dzina lake pa Bukhu maziko a dziko lapansi asanakhazikitsidwe. Ndipo apa iye anali, ataphedwa mu nthawi iyi. Ndipo kumbukirani, taganizani za zimenezo tsopano, momwe ziliri zangwirowo. Atangotha kuphedwa kumene mamillioni amenewo a Ayuda, anthu osalakwa, ndi mafuko a mdziko; apa Lemba likuti, mu nthawi iyi kumene, imene mmodzi aliyense ali pansi pa guwa, akuzindikira chimene chinachitika, ndipo iwo akupatsidwa mikanjo yoyera.

290 Ndipo iwo anati, “Chabwino, bwanji? Kodi ife tingabwerere ku ufumu pakali pano?” Ufumu wa Chiyuda uli woti udzakhazikitsidwe pa dziko lapansi, inu mukudziwa. Yohane anati ufumuwo unali pamenepo, mwaona, kuti udzakhazikitsidwe.

Tsopano, uwu ndi Ufumu wa Uthenga, mukuona.

291 Koma ufumu wa Ayuda udzalalikidwa ndi awa—aneneri awiri awa, kotero zindikirani u—u—ufumu wa dziko lapansi apa.

292 “Ufumu wa Kumwamba ukulalikidwa,”...ndi Ayuda, kapena kwa...ine ndikutanthauza, “kwa Amitundu.”

293 Ufumu wa pano pa dziko lapansi, uli woti udzakhazikitsidwe mu Zakachikwi, pambuyo pa, Zakachikwi kwa Ayuda.

294 Tsopano zindikirani. Zindikirani ichi tsopano, apa, pamene iwo—pamene iwo akulalikira, mwaona.

295 Asanati awa—aneneri awa asanatulukire powonekera; Ayuda awa amene anafa pansi pa Eichmann ndi iwo ali, mmodzi aliyense wa iwo amene anakonzedweratu, akupatsidwa (mwa chisomo) mkanjo woyera. Mmodzi aliyense wa iwo akupatsidwa mkanjo woyera. Mukuona.

Tsopano chikuchitika ndi chiyani? Mwamsanga pamene icho chikuchitika . . .

296 Ine ndikuyang’ana koloko imeneyo kumbuyo uko, ndipo ine ndikudziwa kuti tiri—tikuchedwa. Koma ine sindikufuna kuti . . . Mwaona, ine—ine . . . Iwo . . . ndikuwazindikira anthu osawuka awo ayima apowo. Mulungu akuthandizeni inu, abale. Ine ndikuyembekeza kuti aliyense wa inu adzapatsidwa mkanjo woyera pa tsiku limenelo, mwaona. Mwaimirira, mukusinthana mmbuyo ndi mtsogolo, ndipo miyendo ikupweteka. Ndipo ena a inu mwagwira ntchito tsiku lonse. Ine ndikudziwa chimene icho chiri. Ndipo taonani apa . . . Ndipo ena a akazi aang’ono osawuka achikulire ayimirira. Ine ndinazindikira ena a amuna awa akuwapatsa akaziwo mipando yawo; ndipo winawakenso wamupatsa, mayi wina wamng’ono wosauka ali ndi mwana. Ndipo ine—ine—ine—ine ndikuziwona izo zonse, mwaona, ndipo ine ndiri wotsimikiza kuti Iye akutero. Zindikirani. Koma ine sindikufuna kukusungani inu motalika kwambiri. Ngati ine ndingakhoze kungokufikitsani inu poti muwone Uthengawu, ndizo zonse zomwe ine ndikufuna kuti inu muchite, mwaona.

297 Tsopano zindikirani Ayuda awa. Ine ndiyenera kuchita ichi, polinga kuti inu muwone vumbulutso la Chisindikizo ichi; muwone chimene izo ziri, miyoyo iyi ya pansi pa guwa, ndi omwe iwo ali. Tsopano zindikirani.

298 Mu nthawi ya Daniele, tsopano, theka lachiwiri la sabata ya sevente. Tsopano kumbukirani, “Mesiya anali woti adzadulidwe pakati.” Ndipo pakati. Chabwino, theka la seveni ndi chiyani? [Osonkhana akuti, “Zitatu ndi theka.”—Mkonzi]. Zitatu ndi theka. Kodi Khristu analalikira motalika bwanji? [“Zaka zitatu ndi theka.”] Uko nkulondola. Tsopano, “Koma zidakalipobe zoikidwiratu, kwa anthu,” (chiyani?) “zaka zina zitatu ndi theka.”

299 Chabwino, mu nthawi iyi, bwanji, mwaona, chimene chikuchitika, ndi, Mkwatibwi Wamitundu akusankhidwa mmibadwo seveni ya mpingo, ndipo akupita mmwamba.

300 Ndipo pamene zikuchitika mwanjira imeneyo, Ayuda onse awa amene anaphedwa kumeneko chifukwa cha khungu, akugona pansi pa guwa, Mulungu akubwerapo ndipo akuti, “Inu mwaona chimene icho chinali? Tsopano ine ndikukupatsani mmodzi aliyense wa inu mkanjo.”

Iwo anati, “Mpakana liti, Ambuye? Pamene ife tidzalowe tsopano?”

³⁰¹ Anati, “Ayi, ayi, ayi, ayi. Anthu amzanu, Ayuda, ayenera kuvutika pang’ono pokha, panobe. Iwo ayenera kuphedwa monga inu munaphedwera. Chirombocho chiyenera kudzawapeza iwo pamene icho chidzaswa pangano lake.”

³⁰² Tsopano zindikirani. Ndipo tsopano zindikirani, kamodzi... Tsopano ingokumbukirani, aneneri awa ali oti adzanenera molingana ndi Chivumbulutso 11. Inu, inu munakweza manja anu, inu munawerengapo izo. Mukuona? Ndipo iwo adzapatsidwa mphamvu.

³⁰³ Ndipo ife tipeza amene iwo ali, mu miniti yokha, Ambuye akalola. Tsopano zindikirani amene aneneri awa ali. Ndipo tsopano Baibulo likutiwuza zimenezo apa. Ndithudi, Iye akutero. Ndithudi! Mukuona?

³⁰⁴ Tsopano, zindikirani, pakati pa izi, zaka zitatu ndi theka tsopano, kuti iwo akunenera pansi apa ndipo a—Chivumbulutso apa chinati... Ndipo iwo—iwo ananenera kwa masiku sauzande firii handiredi ndi forte. Ngati...

³⁰⁵ Tsopano, kalendala yachizolowezi ya Chiyuda, nthawi yachizolowezi ya kalendala ya Mulungu, imakhala ndendende masiku sarte pa mwezi. Kalendala ya Chiroma, ndi yomwe inasokoneza izo. Kalendala yachizolowezi imakhala ndi masiku sarte pa mwezi.

³⁰⁶ Tsopano, ngati mukufuna kutenga masiku sarte, ndi kuwonjezera zaka zitatu ndi theka kwa iwo, ndi kuwona masiku sarte, ndipo, chabwino, muli ndi chiyani? wani sauzande firii handiredi ndi... kapena masiku thuu handiredi ndi sikisite. “Masiku wani sauzande thuu handiredi ndi sikisite (masiku sikisite),” ndendende zaka zitatu ndi theka.

³⁰⁷ Tsopano, inu mukuona, palibe kulakwitsa kwa izo. Ndi zimenezo pamenepo, kungogwirizana pamodzi monga—chipsyepsye cha nkunda kubwera pamodzi. Zindikirani, aneneri awiri amenewo analalikira kwa zaka zitatu ndi theka, kwa Ayuda. Mmenemo, mukuitanidwa, handiredi ndi forte-foro sauzande.

³⁰⁸ Ndiyeno, zindikirani, aneneri awiri awa ndiwo ndendende Mose ndi Eliya. Mukuona? Mukuona? Tsopano taonani, taonani, wawo... Taonani utumiki wawo. Tsopano tayang’anani zomwe aneneri awa akuchita. “Iwo ali nayo mphamvu yokantha dziko lapansi ndi mliri, mowirikiza monga iwo angafunire.” Ndani anachita zimenezo? Mose. “Iwo ali nayo mphamvu yotseka miyamba, ndipo iyo siyinavumbe mu tsiku la utumiki wawo.” Ndani anatseka miyamba kwa zaka zitatu ndi theka? [Osonkhana akuti, “Eliya.”—Mkonzi]. Ndi awo kumeneko. Ndi amenewo. Mwaona, ndicho...

309 Mwaona, munthu, pamene iye amwalira, iye samasintha khalidwe lake. Iye samasintha mapangidwe ake, mwaona. Taonani, pamene—pamene, asanati. . .

310 Pamene Sauli anabwerera mmbuyo, ndipo kunalibe aneneri ku dzikolo, iye sankakhoza kumvetsa choti nkuchita—choti achite. Iye anayima motsutsa izo. Iye anali akupita ku nkondo. Iye anapita kwa mfiti ya ku Endori.

311 Tsopano, anali magazi a ng'ombe ndi mbuzi okha, iye amakhoza kuchita izi. Ndipo iye anawuyitana mzimu wa Samueli.

312 Ndipo pamene Samueli anabwera, pamenepo iye anayima, mu mkanjo wake wa uneneri. Osati chokhacho, koma iye anali akadali mneneri. Anati, “Bwanji iwe wandiyitana ine kuchokera ku mpumulo wanga,” mwaona, iye anati, “powona kuti iwe wasanduka mdani kwa Mulungu?” Iye anati, “Panthawi iyi, mawa usiku, iwe ukagwa ku nkondo. Ndipo pa nthawi iyi, mawa usiku, iwe udzakhala ndi ine.” Ndipo ndizo ndendende zomwe zinachitika. Mukuona? Osati zokhazo. . . Iye anali akadali mneneri. Mukuona?

313 Ndipo anthu awa akadali aneneri. Tsopano ife tizama pang'ono mu zimenezo, mu maminiti pang'ono chabe, Ambuye akalola. Mukuona?

314 Oh, mai, momwe ine ndimawakondera Mawu amenewo! Nzosadabwitsa, “Munthu sadzakhala moyo ndi mkate wokha. Koma ndi Mawu onse amene atuluka kuchokera mkamwa ya Mulungu!”

315 Aneneri awiri awa ndi Mose ndi Eliya, molingana ndi ntchito zawo zomwe zikufaniziridwanso kachiwiri. Kuti, umenewo wakhala nthawizonse uli utumiki wawo. Tsopano zindikirani, basi monga momwe iwo ankachitira. Izo sizinawasinthe iwo. Kumbukirani, amuna awa sanafe konse. Muzingopenya basi. . .

316 Tsopano, musasokoneze, ife tisanachoke kwa izi. Musati musokoneze utumiki wa Eliya wa nthawi yachisanu ndi utumiki wake wa nthawi yachinayi. Ine ndakhala ndikukuuzani inu, kuti Mpingo wa Amitundu ukuyembekezera Eliya. Kulondola.

317 Ndipo apa iye ali cha kuno ndi Myuda. Kumbukirani, iye sangakhoze kubwera kanayi; iyo—iyo ndi nambala ya mdani. Iye ayenera kukhala faivi.

318 Nthawi yoyamba imene iye anabwera, iye anali Eliya, mwiniwake. Nthawi yotsatira yomwe iye anabwera, iye anali Elisha. Nthawi yotsatira yomwe iye anabwera, iye anali (chiyani?) Yohane M'batizi. Nthawi yotsatira yomwe iye akubwera, ndi ya mngelo wachisanu ndi chiwiri. Ndipo nthawi yachisanu yomwe iye akubwera, iye ali ndi Mose kutsidya uko, akulalikira kwa iwo. Ndithudi. Inde, bwana. Musati mumusokoneze iye. Uh-huh.

319 Faivi, ngati inu mukudziwa anu—mawerengero anu a Baibulo, faivi ndi nambala ya chisomo chovutikira. Ndipo ndicho chomwe Iye wachita. Tsopano yang'anani, inu mukufuna kudziwa pamene izo ziri. Kodi Yesu anali kuvutikira kwa chisomo? J-e-s-u-s, Faivi, l-a-b-o-r. Nkulondola uko? Kuvutikira, kwa—kwa chikondi kwa inu. Ndipo ngati inu mufika kwa Iye, inu mumabwera chotani, mwa chiyani? F-a-i-t-h mu l-a-b-o-r. Nkulondola uko? Kuvutikira ndi chiwerengero cha chisomo, chabwino, kwa okhulupirira.

320 Zindikirani, Eliya woyamba, ameneyo anali iyeyo. Wachiwiri anali Elisha. Wachitatu anali Yohane. Wachinayi anali mngelo wachisanu ndi chiwiri, kapena mtumiki wotsiriza kwa Mpingo, molingana ndi Malaki 4 ndi Chivumbulutsa 10:7. Tsopano, nthawi yachisanu, iye ndi mtumiki kwa Ayuda, kwa handiredi ndi forte-foro sauzande, kwa Ayuda, Mpingo utatha kupita.

321 Ine—ine—ine ndikungomverera mwachirendo pang'ono, mwaona. Mukuona? Penyani, ngati ena akuganiza kuti... Ine ndikufuna kuti inu mumvetse izi tsopano, mwaona. Ngati ena akuganizabe kuti Malaki 4, “kudzabwezeretsa” anthu, ndi chinthu chomwecho chimene iye akukachita kumusi uko kwa Ayuda, ndi kumaganiza kuti zonsezo ndi zofanana, ndiroleni ine ndiwongole izo kwa inu, kwa miniti yokha. Mwaona, izo zingakhale zosokoneza pang'ono. Chifukwa, inu mukukumbukira, mu Malaki 4, amati, “Kubwezeretsa Chikhulupiro cha makolo... kapena cha ana kubwerera kwa makolo.” Mwaona, kubwerera kwa makolo!

322 Tsopano ndiroleni ine ndikuwonetseni inu kusiyanika kwa utumikiwo. Ngati iye atabwera kudzakwaniritsa Chikhulupiro cha ana kubwerera kwa makolo, iye angadzamukane Khristu. Iye angadzabwerere ku lamulo. Nkulondola uko? Makolowo ankasunga chilamulo. Mukumvetsa zimenezo?

323 Zindikirani, pamene Elisha, pamene iye anabwera kudzakwaniritsa utumiki wake mu Malaki 4, mwaona, monga Malaki 4, Eliya anali yekhayekha.

324 Koma pamene iye akubwera kudzatumikira kwa Ayuda, pa Chivumbulutsa 11, iye ali limodzi ndi Mose. Kotero, apo palibe kusokonezeka, ayi nkomwe. Mukuona? Mukumvetsa zimenezo?

325 Pamene Elisha akubwera, wa Malaki 4, iye ali yekhayekha. Eliya adzakhala; osati Eliya ndi Mose. “Eliya” adzawuka. Koma kudzoza komweko, kumene, anati Eliya adzabwera kwa gawo lotsiriza la m'badwo wa mpingo, “kudzabwezeretsa Chikhulupiro cha ana kubwerera ku Chikhulupiro chapachiyambi cha makolo,” Chikhulupiro cha atumwi, chimene inu mukuyenera kubwererako. Ndipo wotsutsakhristu wawatulutsamo iwo onse. “Kuti adzabwezeretsenso,” monga

Malemba ena onsewo agwirizana pamodzi. Mwaona, iye akubwera yekhayekha. Mukuona?

³²⁶ Koma pamene iye akubwera kwa Mpingo, Baibulo... kapena akubwera kwa handiredi ndi forte-foro sauzande, Baibulo momveka bwino likunena kuti awiri onse iye... Pali awiri a iwo, osati mmodzi wa iwo. Awiri a iwo! Ndipo utumiki wake woyamba sukanawatenga Ayuda ndi kuwayika iwo kubwerera ku chilamulo, iye akudzakhala... chifukwa iye akubwera, kudzalalikira Khristu kwa handiredi ndi forte-foro sauzande, ameni, "Ndi Uyo pamenepo, Mesiya uja amene anadulidwa." Amen! Ndi zimenezotu, koteru musazisokoneze zimenezo. Izo si chisokonezo. Lemba silimanama, ayi nkomwe.

³²⁷ Ulemelero! Oh, pamene ine ndinachiwona icho, ine ndinali kulumpha mmwamba! Ine ndinati, "Zikomo Inu, Ambuye," pamene ine ndinali kuchiyang'ana icho chikuchitika kunja uko. Ndinamuwona Eliya uyo akupita kumeneko kwa m'badwo woyamba uja, ali yekhayekha, ndipo iye anali yekhayekha. Kenako pamene ine ndinadzamuwona iye akubwera kachiwiri, kutali cha kwinakwakenso, apo panali awiri a iwo kumeneko pamene izo zimachitika. Ndinati, "Ndi zimenezotu. Izo, izo zikuchita izo, Ambuye. Amen! Ine ndaziwona izo tsopano! Aleluya!" Ndizo ndendende.

³²⁸ Ngati ine ndikanapanda kuzitchula izo, izo zikanakhala zosokoneza pang'ono kwa winawake. Koma Iye—Iye anandiiza ine kuti ndizinene zimenezo, koteru ndatero.

³²⁹ Zindikirani, amuna awa akusungidwa amoyo ndi Mulungu, kuchokera ku utumiki wawo wapachiyambi, kwa ntchito ya mtsogolo; iwo anawutumikira iwo mwabwino kwambiri. Mukuona? Tangoganizani, mzimu umenewo wa Eliya ukutumikira kasanu; Mose, kawiri. Chiyani? Akusungidwa amoyo kwa kupitiriza, kwa ntchito ya mtsogolo.

³³⁰ Panalibe mmodzi wa iwo amene anafa tsopano; musamazikhulupirire zimenezo. Iwo onse anawonedwa, amoyo, akuyankhula kwa Yesu pa Phiri la Chiwalitsiro. Koma, kumbukirani, iwo ayenera kufa.

³³¹ Tsopano, tsopano, Mose anafa kwenikweni. Koma iye anawuka, chifukwa iye anali choyimira changwiro cha Khristu. Mukuona? Palibe amene anadziwa konse kumene iye anayikidwa. Angelo anabwera kudzamutenga iye. Mukuona? Iye anali ndi Angelo onyamula maliro. Uh-huh. Chifukwa chiyani? Palibe munthu wachivundi akanakhoza kumunyamulira iye kumene iye anali kupita. Iye anangopita kudutsa mu mchitidwewo, ndizo zonse. Iye anali ndi Angelo, onyamula maliro, mwaona, chifukwa iwo anamutengera iye kumene iye ankayenera kuti akakhale. Palibe aliyense akudziwa.

³³² Ngakhale kwa Satana, sanadziwe nkomwe. Iye anakangana naye Mngelowamkulu. Uko nkulondola. Iye sanakhoze kumvetsa

chimene chinachitika kwa Mose. “Ine ndinamuwona iye akunjenjemera cha pamenepo. Ndipo akuyang’ana kunja cha ku dzikolo, ndi kumayang’ana mmbuyo kwa anawo, ndi zina zotero, ine ndinamuwona iye akunjenjemera. Koma anaponda pamwamba pa Thanthwelo, ndipo iyo inali nthawi yotsiriza yomwe ine ndinamuwona iye.”

³³³ Ndiro Thanthwelo! Ndiro Thanthwelo! Ndiroleni ine ndidzayime pa Thanthwe limenelo, pa mapeto a ulendo wanga! Inde, bwana! Tsopano, a... Abale anga achikuda ankakonda kubwera pano ndi kudzayimba nyimbo yaing’ono, “Ngati ine ndikanakhoza, ine ndithudi ndikanayima pa Thanthwe limenelo pamene Mose anayima.” Inde, bwana! Oh, ndiro Thanthwe lomwe ine ndikufuna kuyimapo, nanenso. Mwa chikhulupiriro ine ndikuyima pamenepo.

³³⁴ Koma kumbukirani, Eliya, iye anangofika potopa, chifukwa iye anali nayo ntchito yambiri patsogolo pake. [M’bale Branham wayimikira. Osonkhana akuseka—Mkonzi]. Koteri iye anatheratu mwabwino ndithu, ndipo Mulungu anangomutumizira iye mayendedwe opitira Kwawo, uko nkulondola, anatumiza gareta. Nkulondola uko? Anamutengera iye m mwamba. Iye sanafe konse, chifukwa Iye anamusunga iye wamoyo. Iye anamusungira iye ntchito yoti adzachite mtsogolo. Anamudzoza munthu, aponso, mwaona, adzatulukire mu Mzimu wake.

³³⁵ Koma iwo ayenera adzalawe imfa. Tsopano Chivumbulutso, mutu wa 11. Tsopano, tiyeni tipite, ine ndiri pomwepa mulimonse. Tiyeni tingogunda izo, Chivumbulutso 11. Penyani ndipo muwone ngati awiri onsewo sakuphedwa. Inde, bwana. Iwo awiri onse ayenera adzalawe imfa. Inde, bwana. Utumiki wawo ukadzatsirizika, iwo adzalawa imfa. Chivumbulutso 11, ndipo tiyeni tiyambire pa 7.

*Ndipo pamene iwo...adzatsiriza umboni wawo,
chirombo chimene chinatuluka kuchokera ku
maphompho opandamalire...chidzachita nkondo
mowatsutsa iwo,...*

³³⁶ Oh, mai, iye sangakhoze kupirira nazo zimenezo; ojera odzigudubuza aja abwereranso kachiwiri, mwaona. Chabwino. Chabwino.

*...kuchokera kudzenje lopanda malire...
chidzachita nkondo mowatsutsa iwo, ndipo
chidzawagonjetsa iwo, ndi kuwapha iwo.*

³³⁷ Koma penyani chimene chikuchitika. Iwo akufaniziridwa mwangwirowo tsopano.

*Ndipo mitembo yawo idzagona mu msewu—mu
msewu wa mzinda waukulu uwo,...mwauzimu...
wotchedwa Sodomu ndi Igupto, kumene Ambuye wathu
nawonso anapachikidwa, (Yerusalemu, mwaona).*

338 Tsopano iwo ayenera adzalawe imfa, (sichoncho iwo?) uko nkulondola, utumiki wawo ukadzatha.

339 Chifukwa chiyani? Utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri, utumiki wa Eliya kwa mngelo wachisanu ndi chiwiri, osati. . . Bwanji osati, ndi chifukwa chiyani sunati, kani, ine ndikuyesetsa kunena kuti, utumiki wa mngelo wachisanu ndi chiwiri sunabwere ndi Mose, ngati iye ali wachisavundi, chimodzimidzi momwe zikanakhalira ndi Eliya? Ndi chifukwa chiyani osati iwo. . . Ndi chifukwa chiyani Mulungu sanangotumiza, kuti, “Eliya, iwe—iwe wagwira ntchito molimbikira kwambiri, Ine. . . ndi chirichonse, malo osiyanasiyana onse awa. Ine—ine ndikukhulupirira ine ndingotumiza Mose kumusiko”? Chifukwa chiyani?

340 Tayang’anani pa utumiki wa Mose. Eliya anali mneneri kwa mafuko onse; koma Mose anali wopereka lamulo kwa Ayuda okha. Amen. Mose ali kumeneko kuti akati. . . Chifukwa chimene iye akubwerera ndi Eliya. . . Ayuda amenewo akuti, “Dikirani, ife tikanasangabe lamulo kuno.” Koma apa pakuyima Mose mwiniwake; ndipo apa pali Eliya akuyima naye iye. Oh! Mukuona? Iye akubwera kwa Ayuda okha. Mukuona? Mose anangopita kwa Myuda basi; mneneri Eliya anali wa kwa mafuko onse. Koma Mose anadzakhala mneneri kwa Ayuda, ndi wopereka lamulo. Mukuona? Umenewo unali uthenga wake, lamulo.

341 Koma kodi uthenga wa Eliya unali wotani? Kwa akazi odula-tsitsi; zipembedzo. Inde, bwana. Ndipo iye anawang’amba iwo kwenikweni mzidutswa. Nkhope zopentedwa; anawauza iwo, “Inu mudzadyetsedwa kwa agalu.” Iye anangowang’amba kwenikweni iwo.

342 Ndiyeno pamene Mzimu wake unabwera pa Yohane, iye anatulukira kuchokera ku chipululu ndipo anachita chinthu chomwecho. Kulondola. Anati, “Inu musati muziganiza kuti ndife a *ichi* kapena *icho*. Mulungu ali wokhoza mwa miyala iyi kudzutsa ana kwa Abrahamu.”

343 Anayenda kupita kwa Herodiya, anati, “Ndipo iwe ukutanthauza kundiuzwa ine kuti wakwatira mlamu wako yemwe. . . ?” Anati, “Sikololedwa kwa iwe kuti uchite zimenezo!” Oh, m’bale! Psyii! Hum! Iye anamuwuzwa iye. Ndithudi.

344 Zindikirani, miyoyo iyi ili yoti iyembekezere kwa kanthawi pang’ono, kuti handiredi ndi forte-foro. . . kuti aphedwe. Oh, si choncho zimenezo, siziri. . . ? Izo zikungoyika Baibulo pamodzi.

345 Tsopano nthawi yanga yatha ndendende, ngati ine nditi ndikutulutseni mofulumira. Koma ine ndiri nazo zinthu pang’ono chabe zochulukirapo zoti ndinene, ngati inu

mungapirire nazo. [Osonkhana akuti, “Pitirizani!”—Mkonzi]. Ine ndikudziwa kuti kwatentha. Ndipo ine ndikutuluka thukuta.

³⁴⁶ Koma, mvetserani, ine ndiri nacho chabe chinachake choti ndikuuzeni inu. Icho ndi chabwino kwambiri basi, icho chikungotentha mu mtima mwanga. Ine ndikuyembekeza kuti inu simunaiwale izo, mwaona. Ndiroleni ine ndinene izi, mu kukhalapo kwa Iye. Mwa chisomo Chake, Iye anandirolanso ine kuti ndiwawone anthu anga, osati kale kwambiri, ali mmikanjo yoyera. Inu mukukumbukira zimenezo? Mukukumbukira? Inu mukuikumbukira nkhaniyo, osati kale kwambiri? Mkwatibwi wa Amitundu, iwo ali kumeneko tsopano. Iwo onse anali mmikanjo yoyera.

³⁴⁷ Ine ndinali nditadzuka. Ine ndinali ndiri pa msonkhano. Chakhala chiri pafupifupi chaka chapitacho, kupitirira pang’ono. Ine ndinadzuka mmawa wina, ndipo ine ndinawuka. Ndipo ine ndinati, “Wokondedwa?” kwa mkazi wanga. Iye sanasunthe. Ana pafupifupi... Ndimayenera kuti ndidzuke ndi kuwatengera iwo ku sukulu, cha kuno kumene ku malo akale. Chabwino, ine—ine ndinadzuka pa bedi, inu mukudziwa, ndipo ndinatsamira. Inu mukudziwa momwe; kudzuka ndi kungotsamira mutu wako kumbuyo kutsamira thabwa la kumutu. Ife tiri nalo limodzi la mabedi achikale. Ndipo kotero ine ndinangotsamira kumbuyo monga *choncho*.

³⁴⁸ Ndipo ine ndinaganiza, “Mnyamata, iwe uli kale fifitefirii. Ngati iwe uti umuchitire chirichonse Mulungu, kulibwino iwe uchitiretu icho, chifukwa iwe ufika pokhala kwambiri—pokalamba kwambiri, pakapita kanthawi.” Mwaona.

³⁴⁹ Ndipo ine ndinaganiza, “Inu mukudziwa, uko nkulondola, tsopano.” Ine ndinaganiza, “Mnyamata, iwe ukudziwa, ine sindiri kutali kwambiri. Ine ndiyenera kupita posachedwapa.” Ine ndinati, “Ndizo—ndizo wamkulu ndi chaka kuposa momwe abambo anga anakhalira moyo.” Mukuona? Ine ndinaganiza, “Ine ndiyenera kuchokapo posachedwapa. Ine ndinachiwona icho. Ndipo, apa, ine sindinamuchitire Mulungu kalikonse, panobe.” Ine ndinaganiza, “Ine nthawizonse ndakhala ndikufuna nditamuchitira Iye chinachake.” Ine ndinaganiza, “Ine ndiyenera kufulumira ndi kukachita icho, ngati ine nditi ndichite icho. Ndipo ine sindikudziwa momwe nditi ndichitire icho, ndizo zonse.”

³⁵⁰ Ine ndinaganiza, “Mwamuna, ine ndikuyembekeza kuti ndikhala moyo kuti ndidzamuwone Iye akubwera. Ine sindikufuna kuti ndidzakhale chipukupuku, kapena mzimu.”

³⁵¹ Mwaona, ine nthawizonse ndimakhala ndikuwopa mzimu. Ndipo tsopano, inu mukudziwa, izo zimakhala ngati wa a... Ine nthawizonse ndimaganiza, kuti ngati ine nditadzakumana ndi M'bale Neville ndipo iye nkukhala kamtambo kakang’ono koyera kakuyendayenda, inu mukudziwa. Ndipo ine

ndingadzati, “Moni, M’bale Neville.” Ndipo iye angati, “Moni, M’bale Branham,” mwa chokhudzira chinachake; iye sakutha kuyankhula. Koma ine ndikanamangodziwa kuti uyo ndi M’bale Neville. Eya. Ine ndingafune kumugwira dzanja lake monga momwe ine nthawizonse ndimachitira. Chifukwa, ndizo zonse zomwe ine ndimazidziwa, zokhudza anthu. Mwaona, ine ndikanafuna kumugwira dzanja lake, koma iye alibe dzanja. Ilo liri pansi uko mmanda, litavunda. Mukuona?

³⁵² Ine ndinaganiza, “Mai, ine ndikuyembekeza ine sindikuyenera kud zadutsa mu zimenezo.” Tsopano, ine ndinali... Tsopano ine ndikuwuzani inu choonadi. Ine—ine ndinkawopa kufa; osati kuwopa kuti ndingatayike, koma ine sindinkafuna kuti ndidzakhale mzimu. Ine ndimafuna kuti ndidzangokhalabe munthu. Ine ndinkafuna kudzayembekezera Mk watulo, mwaona. Ine ndinkangofuna kukhala monga choncho. Ine sindinkafuna kuti ndizikhala mzimu ayi, kumapita uku ndi uku. Ine ndinali nditagona pamenepo, ndikuganiza zimenezo.

³⁵³ Ndipo, zonse mwakamodzi, panali chinachake chinachitika. [M’bale Branham anakhwatsitsa zala zake—Mkonzi].

³⁵⁴ Tsopano, inu mukudziwa, ndipo nonse inu mukuzidziwa, za masomphenya. Ndipo ngati awa anali masomphenya, ine sindinakhalepo nawo onga amenewo, mwaona. Ndipo ine ndakhala ndiri nawo kuyambira ndiri mnyamata wamng’ono.

³⁵⁵ Ndipo, zonse mwakamodzi, chinachake chinachitika. Ndipo ine ndinadzimverera ndekha ndikuchokapo. Ine ndinaganiza, “Uh-oh.” Ndipo ine—ine ndinaganiza, “Ine—ine ndamwalira kale, mwaona, ndipo ndiri—ine ndapitiratu.” Mukuona?

³⁵⁶ Ndipo ine ndinafika ku malo, ndipo ine ndinaganiza, “Ine ndikukhulupirira ine ndiyang’ana mmbuyo.” Izo zinali zenizeni basi, amzanga, monga ine ndikuyimira pomwe pano. Mukuona? Ndipo ndinacheuka pozungulira, kuti ndiyang’ane mmbuyo. Ndipo apo ine ndinali, nditagona pa bedi. Ndipo ndinali nditaziwongola, nditagona pambali pa mkazi wanga.

³⁵⁷ Ine ndinaganiza, “Chabwino, awo mwinamwake anali matenda a mtima.” Mukuona? Ine ndinaganiza, “Chabwino, mwaona, ine ndangomwalira mwadzidzidzi,” imene ingakhale njira yabwino yopitira. Kotero, ine ndinaganiza, “Awo ndi matenda a mtima. Ine sindinasowe kuti ndivutike.” Ine ndinayang’ana, ndipo ndinaganiza, “Chabwino, tsopano, izo ndi zachirendo. Apo ine ndagona, apo pomwe; ndipo apa ine ndayima, pano.”

³⁵⁸ Kotero, ine ndinachewuka. Iwo unkawoneka ngati wawukulu kwambiri—ngati munda wawukulu kwambiri, choncho, kapena chinachake, munda wawukulu basi wotambalala wa udzu wabuluu. Ndipo—ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine ndikudabwa chomwe ichi chiri?”

359 Ndipo, zonse mwadzidzidzi, pamene ndinayang'ana, apa panabwera masauzande kuchulukitsa ndi masauzande a akazi achichepere, onse ali mmikanjo yoyera, tsitsi likulendewera pansi mpaka mchiuno mwawo, opanda nsapato, ndipo iwo anali kuthamanga molunjika kwa ine. Ine ndinaganiza, "Tsopano ichi ndi chiyani?"

360 Ine ndinachewuka pozungulira, ndinayang'ana mmbuyo *kumeneko*, ndipo apo ine ndinali; ndipo ine ndinadzayang'ana mmwamba mbali *iyi*, uko iwo amabwera. Ine ndinadzaluma chala changa. "Ine—ine—ine—ine sindikugona, ndendende." Koma, ine ndimakhoza kumverera. Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ndiye, chinachake apa, chachirendo."

361 Ndipo akazi awa onse amabwera, akuthamanga. Ndipo ine sindinawawonepo akazi okongola chomwecho! Ndipo iwo onse amabwera, akuthamangira kwa ine. Ndipo pamene amathamangira kwa ine. . .

362 Inu mukudziwa momwe ine ndakhala ndikuchitira, kukhala ngati. . . Iwo amanditcha ine wodana ndi akazi, koma ine sindiri, mwaona. Koma, ine—ine ndikungoganiza, kuti mkazi wabwino ndi mmodzi mwa. . . ndi ngale. Koma, ine ndikuganiza kuti, amene siali wabwino, ali, monga Solomononi amanenera, "madzi mmagazi ako." Koteri ine ndithudi ndiribe nawo ntchito—akazi a mbiri yoyipa kapena odzimva.

363 Ndipo koteri akazi onse awa amabwera. Iwo amayamba kuponyera mikono yawo mondikumbatira ine. Tsopano, icho ndi chachilendo. Inu mukudziwa ine sindikanalolera zimenezo. Choteri, ndipo iwo anali. . . Tsopano, ine ndinena ichi mwanjira, yakuti, ine ndiri—ine ndiri mu gulu losakanikirana. Koma, iwo anali, iwo anali akazi. Iwo anali akazi. Ndipo iwo—iwo anali kundikumbatira ine, aliyense, ndipo akuti, "Wathu—m'bale wathu wofunikira!" Ndipo mmodzi amakhoza kundikumbatira ine, ndipo kenako wina nkudzandikumbatiranso ine.

364 Ine ndinali nditayima pamenepo, ndikuyang'ana. Ine ndinaganiza, "Chabwino, tsopano, ichi ndi chiyani?" Mukuona? Ndipo iwo anali atayima pamenepo. Ine ndinaganiza, "Chachitika ndi chiyani?" Ine ndinayang'ana mmbuyo pansi. Apo ine ndinali, nditagana pansi kumene *pamenepo*; ndipo apa ine ndinali, nditayima *apa*. Ine ndinaganiza, "Tsopano, icho ndi chosamvetsetseka. Ine—ine sindikuzimvetsa izi."

365 Ndipo akazi amenewo akufuula, "Oh, m'bale wathu wofunikira," ndi kumandikumbatira ine. Tsopano, iwo anali chidutswa chirichonse, mwa kumverera, akazi.

366 Tsopano mundikhululukire ine, alongo, pamene ndikunena izi, chifukwa. . . Koma inu mumamvetsera kwa adokotala anu; ndipo ngati ife tiribe malingaliro oyera, ndiye sindife Akhristu. Ine sindikusamala. . .

³⁶⁷ Ine nthawizonse ndakhala ndikukhala moyo woyera. Mulungu akudziwa zimenezo. Pamene ndinali mnyamata wamng'ono, Mngelo wa Ambuye anandiuza ine kuti ndisadzayipitse thupi langa, kusuta, kapena kumwa. Ndipo icho chakhala chiri choona. Mwa chisomo cha Mulungu, ine ndakhala ndikuzisunga zimenezo. Pamene ine ndinali wochimwa, ine sindinali kuthamangathamanga ndi akazi. Ndipo chotero. . .

³⁶⁸ Koma mwamuna aliyense yemwe angalole mkazi kumukumbatira mmikono mwake, iyeyo pokhala wopangidwa ndi minofu ya chimuna, ndipo mkaziyo, ali ndi yachikazi, apo pamakhala zogirigisha. Ine sindikusamala kaya ndiwe ndani, tsopano, musandiuze ine kuti inu simuli, ngati inu muli munthu wathanzi.

³⁶⁹ Koma, osati Kumeneko; chifukwa iwe sumakhala nawo, konse, makhungu osiyana. Iwe sungachimwe konse Kumeneko. Uko kunali kusinthika. Kumeneko kunalibenso china choposa chikondi cha pa abale basi kwa akazi amenewo.

³⁷⁰ Ngakhale, mu chisomo chimene iwo amayang'anapo, ine ndikuganiza, a—mkazi, mkazi wabwino amene amadzisunga yekha mwabwino, ndi kumayenda monga dona, iye amakhala—amakhala chitsanzo cha ngale padziko lapansi. Ine—ine ndimakonda chirichonse chimene chiri chachisomo. Ine ndikuganiza kuti, a—a mkazi amene amasunga malo ake, ndi kumayesetsa kukhala dona, amakhala—amakhala thunthu la ulemu. Ine ndimakhulupirira zimenezo. Ndipo ine ndikuganiza kuti, iye amene siali, basi zimakhala ngati a—Khristu ndi wotsutsakhristu, chinthu chomwe chomwecho.

³⁷¹ Ine—ine ndimakonda chirichonse chomwe chiri mwachirengedwe. Monga kavalo wokongola, kapena chirichonse, iye amangoyima mu thunthu la kavalo wokongola weniweni. Kapena, chirichonse chonga icho, phiri lokongola, akazi okongola, amuna okongola, chirichonse chimene chimayima mmapangidwe a Mulungu, ine nthawizonse ndimachiyamikira icho.

³⁷² Ndipo awa anali angwiro. Koma zinalibe kanthu kuti iwo anandikumbatira ine mochuluka bwanji mmikono mwawo, ndipo iwo anali akazi, inu mukumvetsa, koma apo sipakanakhala tchimo konse. Zokhudzira zachimuna ndi zokhudzira zachikazi, zonse, zinali zitachokapo. Ndikuthokoza Mulungu! Iwo anali alongo anga, kwathunthu.

³⁷³ Ine ndinayang'ana. Ndipo ine ndinayamba ku. . . Ine—ine ndinayang'ana mmanja anga; ine ndinawona kuti nawonso anali achichepere kwambiri. Ndipo ndinayang'ana; ine ndinali wamng'ono, nanenso. Ndipo ine. . .

³⁷⁴ Ndipo kutaya tsitsi kwanga, monga wachinyamata; atayika carbohic acid pa ilo, wometa anatero, ndipo analichotsapo ilo

lonse pamene ine ndinali mnyamata chabe. Ndipo icho chakhala nthawizonse chonga ngati—chinthu kwa ine, mwakuti ine—ine—ine ndimazizidwa mwamsanga, chifukwa chakuti liwombo langa likadali lofewa, inu mukudziwa. Ndipo mizu ya tsitsi ikadalipo pamenepo, koma iyo inawotchedwa ndi carbolic acid, ndipo tsitsi silingakhoze kumera konse, mwaona.

³⁷⁵ Ndipo ine ndinapita, mkazi wanga, pamene ine...zaka zambiri zapitazo, ndipo anakandipezera ine kachidutswa ka tsitsi kuti ndizivala, kachidutswa kakang'ono ka tsitsi, kuti ndizivala, kuti ndiziphimba mutu wanga. Koma nthawizonse ndimachita wamanyazi kulivala ilo, chifukwa limawoneka ngati ndi chinachake chonyengezera. Ndipo ine sindimafuna kanthu konyengezera.

³⁷⁶ Ndipo kotero ine ndinaganiza, “Ine ndizingovala kachisoti.” Ndiye, ine ndinatero, kwa kanthawi. Inu mukudziwa chimene iwo anachita? Iwo ankafuna kumanditcha ine “bishopu” ndiye, anati ine ndinkafuna kukhala...Mukuona? Ine ndinangoti, “Chisiyeni icho chizipita.”

³⁷⁷ Kotero ine ndimangovutika nako kuzizira koyipa, ndi kumalola izo...Koma, ine...inu...kungotsegula mazenera amenewo, kapena chirichonse, kungolola mpweya pang'ono kuti ulowe modutsa monga choncho, mnyamata, ine ndimawumva iwo.

³⁷⁸ Tsopano ine ndinapita kwa dokotala ndi kukamufunsa iye, chimene anali kuganiza. Iye anati, “Chabwino, taonani, anu—mabowo anu ndi otseguka, inu mukumatuluka thukuta chifukwa cholalikira, mpweya umenewo umabwera, iwo—iwo umayika nyongolosi yachifuwa apa mmamina, ndipo iyo imayendera chotsika mpaka kummero kwanu, mmawa wotsatira inu mumasasa mawu, ndi zimenezotu.”

³⁷⁹ Ndipo—ndipo chotero, oh, mai, anyamata inu amene muli nalo tsitsi, inu simukudziwa momwe inu muyenera kukhalira wothokoza, ndi chifukwa chokhala nalo ilo. Uko nkulondola. Mukuona?

³⁸⁰ Chabwino, tsopano, ine ndinadzapeza, ndiye, kuti ine—ine ndidza...Limodzi la masiku awa, ngati ine sindidzakhala nawo mano anga, ine ndidzayenera kukhala nawo ena a iwo, ndipo, kotero, kapena mwina kuchita popanda iwo.

³⁸¹ Chotero ngati munthu—ngati munthu...Chabwino, sindikanaganiza kuti zingakhalenso zochuluka kwa mwamuna, ngati iye akanafuna kutero, kumavala kachidutswa katsitsi, kuposa momwe zingakhalire kwa mkazi kuvala chimodzi cha mbewa izi kapena makoswe awa, chirichonsecho chimene iwo amachiyika mu tsitsi mwawo monga choncho, kuti alikongoletse ilo. Mukuona? Koma—koma, ndithudi, ngati iwe utachita zimenezo, zimatengera cholinga chomwe ukuchitira zimenezo.

Mwaona? Zimatengera cholinga chomwe iwe ukuchitira zimenezo. Ndipo koteru . . .

³⁸² Koma, komabe, nditayima pamenepo, ine ndinamverera mmwambamu, ndipo ndinali nalo tsitsi langa kachiwiri. Mai! Ine ndinali mnyamata. Ndipo awa, onse awa, achinyamata! Ndipo ndinaganiza, “Chabwino, kodi izi si zachirendo! Ndi awa apa.” Ndipo iwo onse anali akuthamanga . . .

³⁸³ Ndipo ndinayang’ana, akubwera, ndipo—ine ndinamuwona Hope akubwera. Iye anadzayang’ana . . . Inu mukudziwa, iye anamwalira ali ndi zaka twente-thuu. Iye anali akadali wokongola basi monga anali nthawizonse. Ambiri a inu mukumukumbukira iye; maso aakulu akuda amenewo. Iye anali Wachijeremani. Tsitsi lake lakuda likugwera kumbuyo kwake. Ine ndinaganiza, “Tsopano, iye akati wafika pano, iye adzati—adzanena kuti, ‘Bill.’ Ine ndikudziwa iye adzatero. Ine ndikudziwa kuti adzati, ‘Bill,’ pamene adzafika pano.”

³⁸⁴ Ine ndinali ndikuyang’ana. Ndipo aliyense wa akazi awa akubwera ndi kumandikumbatira ine, akuti, “Oh, m’bale wofunika, ndife okondwa kukuonani inu!” Ndipo ine ndinaganiza . . . Aliyense atavala mofanana basi, koma iwo anali nalo tsitsi lawo mosiyanasiyana, inu mukudziwa, tsitsi lofiira, ndi tsitsi lakuda, ndi tsitsi la bulondi. Ndipo—ndipo iwo anali akubwera, koma iwo onse anali achichepere.

³⁸⁵ Ndipo pamene iye anadzafika kwa ine, ine ndinaganiza, “Ine ndingowona chimene iye ati anene.”

³⁸⁶ Ndipo iye anadzayang’ana mmwamba pa ine, ndipo anati, “Oh, m’bale wathu wofunika!” Iye anadzandikumbatira ine, ndipo anangopitirira. Mkazi wina anabwera, anadzandikumbatira ine, motsatira.

³⁸⁷ Ndipo ndinamva phokoso. Ndipo ndinayang’ana cha mbali *iyi*, ndipo apa panabwera gulu la amuna, achinyamata, onse ali mu usinkhu wa pafupifupi twente. Iwo anali ndi tsitsi lakuda, ndi tsitsi la bulondi. Ndipo iwo onse anali atavala mikanjo yoyera, ndipo osavala nsapato. Ndipo iwo anadzathamangira kwa ine ndikuyamba kumandikumbatira ine, akufuula, “M’bale wofunika!”

³⁸⁸ Ine ndinaganiza. Ndipo ndinacheuka mmbuyo, ndipo apo ine ndinali, nditagonabe pamenepo. Ndipo ndinaganiza, “Chabwino, tsopano, ichi ndi chachirendo.”

³⁸⁹ Ndipo pomwepo Liwu linayamba kuyankhula kwa ine. Ine sindinaliwone konse Liwulo. Ilo linati, “Iwe wasonkhanitsidwa, iwe—iwe wasonkhanitsidwira kwa anthu ako.” Ndipo kenako amuna ena anandinyamulira ine pamwamba, anadzandikhazika ine pamwambapo, pa chinthu chachitali chachikulu monga *chonchi*.

Ine ndinati, “Ndi chifukwa chiyani mwachita zimenezo?”

Anati, “Pa dziko lapansi iwe unali mtsogoleri.”

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, ine—ine sindikumvetsa zimenezi.”

³⁹⁰ Ndipo Liwu limenelo likuyankhula kwa ine. Ine sindimakhoza konse kuliwona Liwulo. Tsopano, Ilo linali chabe pamwamba panga, likuyankhula kwa ine.

³⁹¹ Ine ndinati, “Chabwino, ngati ine—ngati ndapambana, ine ndikufuna ndimuwone Yesu.” Ine ndinati, “Ine...Iye anali chomwecho...Iye anali moyo wanga wonse. Ine ndikufuna ndimuwone Iye.”

Ndipo kotero Iye anati, “Iwe sungakhoze kumuwona Iye tsopano. Iye akadali pamwamba kwambiri.”

³⁹² Mukuona, apo panali pansi pa guwa, apobe, mwaona, malo achisikisi, kumene anthu amapitako, mwaona; osati achiseveni, kumene kumakhala Mulungu, malo achiseveni. Achisikisi!

³⁹³ Ndipo iwo anali—ndipo iwo onse anali kumeneko, ndipo iwo anali akudutsapo. Ndipo ine ndinati...Zinkawoneka ngati kunali makamaka mamillioni a iwo. Ine sindinawawonepo iwo...Ndipo, pamene ine ndinakhala pamenepo, akazi awa ndi amuna akuthamangabe ndi kumandikumbatira ine, kumanditcha ine “m’bale.” Ndipo ine ndinakhala pamenepo.

³⁹⁴ Ndiyeno Liwu lija linati, “Iwe wasonkhanitsidwira kwa anthu ako, monga Yakobo anasonkhanitsidwira kwa anthu ake.”

Ine ndinati, “Onse awa, anthu anga? Kodi onse awa ndi a Branham?”

Iye anati, “Ayi. Iwo ndi omwe unawatembenezira kwa Khristu.”

³⁹⁵ Ine ndinayang’ana pozungulira. Ndipo apo panali mkazi wokongola kwenikweni akubwera. Iye ankawoneka chimodzimodzi basi. Iye anadzatambasulira nkono wake mondikumbatira ine, ndipo iye anati, “Oh, m’bale wanga wofunika!” Iye anayang’ana pa ine.

³⁹⁶ Ine ndinaganiza, “Mai! Iye amawoneka ngati Mngelo.” Ndipo iye anadzadutsa.

Ndipo Liwu lija linati, “Kodi iwe sunamuzindikire iye?”

Ine ndinati, “Ayi, ine sindinamuzindikire.”

³⁹⁷ Anati, “Iwe unamulondolera iye kwa Khristu pamene iye anali atadutsa zaka nainte.” Anati, “Iwe ukudziwa chifukwa chimene iye akuganizira mochuluka za iwe?”

Ine ndinati, “Mtsikana wokongola ameneyo anali atadutsa zaka nainte?”

³⁹⁸ “Eya.” Anati, “Iye sangakhoze kusinthanso tsopano.” Anati, “Ndi chifukwa chake iye akuti, ‘M’bale wofunika.’”

399 Ine ndinaganiza, “Oh, mai! Ndipo ndimachita mantha ndi izi? Bwanji, anthu awa ndi enieni.” Iwo, iwo sanali kupita kulikonse. Iwo samatopa, kukhala Kumeneko.

Ndipo ine ndinati, “Chabwino, chifukwa chiyani ine sindingathe kumuwona Yesu?”

400 Anati, “Chabwino, tsopano, Iye adza—Iye adzabwera tsiku lina. Ndipo Iye adzabwera kwa iwe, poyamba, ndipo akadzatero iwe udzaweruzidwa.” Anati, “Anthu awa ndi owatembenuza ako amene iwe wawatsogolera.”

401 Ndipo ine ndinati, “Inu mukutanthauza kuti, pokhala mtsogoleri, kuti ine. . .kuti Iye adzandiweruza ine?”

Anati, “Inde.”

402 Ndipo ine ndinati, “Kodi mtsogoleri aliyense adzasowa kuweruzidwa monga chomwecho?”

Anati, “Inde.”

Ine ndinati, “Nanga bwanji Paulo?”

Iye anati, “Iye adzaweruzidwa ndi ake.”

403 “Chabwino,” Ine ndinati, “ngati gulu lake liti likalowwe, chimodzimodzinsola langa, chifukwa ine ndalalikira ndendende Mawu omwewo.” Ndi zimenezotu. Ine ndinati, “Pamene iye anabatiza mu Dzina la Yesu, ine ndinatero, nanenso. Ine ndinalalikira. . .”

404 Ndipo mamillioni anafuula, onse pamodzi, anati, “Ife tikupumula pa Chimenecho!”

405 Ndipo ine ndinaganiza, “Mai! Ngati ine ndikanadziwa kokha izi ndisanabwere kuno, ine ndikanawapangitsa anthu kuti adzabwere kuno. Iwo sangakhoze kukwanitsa kuchiphonya ichi. Bwanji, tayang’anani apa!” Ndipo kenako. . .

406 Ndipo Iye anati, “Tsopano, tsiku lina Iye adzabwera, ndipo zikadzatero. . .Tsopano, kumeneko, ife sitimadya, kumwa, kapena kugona. Ife tonse timakhala mmodzi.”

407 Chabwino, si ungwirowo; ndi choposa ungwirowo. Si chapamwamba; ndi choposa upamwamba. Palibe dzina lingakhoze. . .Inu simungathe kuganizira. . .Mulibe mawu mu chinenero amene angafotokoze izo. Inu mwafika basi, ndizo zonse.

408 Ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ichi, ichi chingakhale changwirowo. Ndiyeno ife tidzachita chiyani potsatira?”

409 Anati, “Ndiye, pamene Yesu adzabwera, ndipo ife tiri. . . ndipo Iye adzakuweruza iwe, kapena chifukwa cha utumiki wako, ndiye ife tidzabwerera ku dziko lapansi ndi kukatenga matupi.” Chabwino, ine—ine ndinali ndisanaganizapo nkomwe za zimenezo mmbuyomo. Zimenezo ndi ndendende Lemba. Anati, “Kenako ife tidzabwerera ku dziko lapansi ndi kukatenga matupi, zikadzatero ife tidzadya. Ife sitimadya kuno, komanso

ife sitimagona.” Anati, “Ife timadya kumusi uko, koma ife tidzabwereranso ku dziko lapansi.”

410 Ine ndinaganiza, “Mai, kodi izi si zodabwitsa! Oh, mai! Ndipo ine ndinkachita mantha ndi chimenecho. Nchifukwa chiyani ine ndinkachita mantha ndi kumwalira, kuti ndidzabwere ku ichi? Chabwino, ichi ndi ungwiwo, kuwonjezera ungwiwo, kuwonjezera ungwiwo. Oh, ichi ndi chodabwitsa!”

411 Mwaona, ife tinali pansi kumene pa guwa. Mukuona? Izo zinali zimenezo, mwaona, pansi kumene pa guwa, kuyembekezera Kudza, mwaona, kuti Iye apite kukawatenga iwo amene anali kugona mu...a—matupi omwe akugona mu fumbi, kuti adzatiwukitse ife kachiwiri; kudzabwera, kudzatidzutsa ife.

412 Monga Yesu anabwera kudzera mu paradiso, ndipo anamudzutsa Abrahamu, Isaki, ndi onse amenewo, inu mukudziwa, amene anali kuyembekezera chiwukitsiro choyamba. Iwo analowa mu mzindawo ndipo anawonekera kwa ambiri.

413 Izo ndi zangwiwo Mwamalemba. Masomphenyawo anali chimenecho, kapena chirichonse chimene icho chinali, iwo anali mwangwiwo Mwamalemba.

414 Ndipo ine ndinati, “Chabwino, kodi izi si zodabwitsa!” Ndipo kenako ine ndinaganiza, “Kodi izo si zodabwi-...?”

415 Ine ndinamva chinachake chikulira, monga kavalo. Ndipo ndinayang’ana. Ndipo kavalo wanga wokwerapo wamng’ono amene ine ndinkakonda kumukwera, Prince wamng’ono, ine ndinkaganiza zochuluka kwambiri za iye. Apa iye anali, atayima pamenepo pambali panga, ndipo anadzayika mutu wake cha pa phewa langa, kuti andikumbatire ine. Monga ine ndinkakondera kumupatsa iye shuga, inu mukudziwa, ndipo iye anadyzaika lake. . . Ine ndinayika nkono wanga pa iye. Ine ndinati, “Prince, ine ndimadziwa kuti iwe udzakhala kuno.”

Ine ndinamverera chinachake chikunyambita dzanja langa. Apo panali galu wanga wakale wosaka mbira.

416 Pamene—pamene Bambo Short, kumusi kuno, anamupatsa iye chiphe, ndinalumbirira kuti ndimupha Bambo Short chifukwa cha chimenecho. Ine ndinali pafupifupi zaka sikisitini zakubadwa. Iwo anamuthirira iye chiphe, anamupatsa iye batani la galu. Ndipo bambo anga anandipezerera ine ndiri ndi mfuti, ndikupita kumusi uko kukamuwombera iye, komweko ku sitieshoni ya polisi. Ndipo ine ndinati, “Ine ndimupha iye.” Ine ndinati, “Chabwino. . .” Ine ndinapita kumanda a galuyo. Ine—ine ndinakamukwirira iye. Ine ndinati, “Fritz, iwe wakhala uli monga bwanawe kwa ine. Iwe wakhala ukundiveka ine ndi kunditumiza ine ku sukulu. Pamene iwe unakalamba, ine ndinali woti ndizikusamalira iwe. Tsopano iwo akupha iwe.” Ine ndinati, “Ine ndikukulonjeza iwe, Fritz, kuti iye sakhala moyo.” Ine

ndinati, “Ine ndikukulonjeza iwe, kuti iye sakhala moyo. Ine ndidzamupeza iye pa msewu nthawiyina, akuyenda, ndiye ine ndidzathamangira pa iye, mwaona.” Ndipo ine ndinati, “Ine ndidzamupha iye chifukwa cha iwe.”

417 Koma inu mukudziwa chiyani? Ine ndinamulondolera bamboyo kwa Khristu, ndinamubatiza iye mu Dzina la Yesu, ndipo ndinadzamuyika iye pa imfa yake. Inde, bwana. Ine ndinatembenuka mtima pafupifupi zaka ziwiri zitachitika zimenezo. Ine ndinawona zinthu mosiyana pamenepo, mwaona. Ine ndinamukonda iye m'malo momuda iye.

418 Komano, koma, komabe, apo panali Fritz atayima pamenepo, akundinyambita ine pa dzanja. Ndipo ine ndinali . . . Ine ndinayang'ana.

419 Ine sindimakhoza kulira. Palibe amene akanakhoza kulira. Chonse chinali chisangalalo. Iwe sukanakhoza kukhala wachisoni, chifukwa kunali konse chisangalalo. Iwe sukanakhoza kufa, chifukwa kunali konse Moyo. Mukuona? Mukuona? Sukanakhoza kukalamba, chifukwa kunali konse unyamata. Ndipo ndicho chimene . . . Ndi zangwiro basi. Ine ndinaganiza, “Oh, kodi izi si zodabwitsa!” Ndipo mamillioni . . . Oh, mai! Ine ndinali kwathu komwe, mwaona.

420 Ndipo—ndipo pomwepo ine ndinamva Liwu. Ndipo Ilo linafuula, linati, “Zonse zimene iwe unazikonda . . .” mphotho ya utumiki wanga. Ine sindikusowa mphotho. Iye anati, “Zonse zimene iwe unazikonda, ndi zonse zimene zinakukonda iwe, Mulungu wazipereka kwa iwe.”

Ine ndinati, “Ambuye alemekezeke!”

421 Ine ndinamverera mwachirendo. Ine ndinaganiza, “Vuto ndi chiyani? Ndikumverera mwachirendo.” Ine ndinatembenuka ndipo ndinayang'ana. Ndipo pa bedi paja, thupi langa linali likusuntha. Ine ndinati, “Oh, ine sindikuyenera kubwerera, ndithudi. Musati, musandilole ine kuti ndizipita.”

422 Koma Uthenga unkayenera kuti udzalalikidwe. Mu mphindi chabe, ine ndinali pa bedi kachiwiri, mwaona, monga choncho.

423 Osapitirira pafupifupi miyezi iwiri yapitayo, izo . . . Inu munazimva izo zikuwerengedwa mu—mu *Voice* ya Amuna Amalonda. Izo zapita mdziko lonse, mwaona. Ndipo M'bale Norman, muno, ine ndikuganiza iye ali muno penapake usikuuno. Iye anamasulira kuchokera pamenepo, ndipo anazitumiza izo mu timabukhu. Izo zapita konsekonse. Ndipo atumiki analemba, ambiri a iwo, ndipo anati . . .

424 Mmodzi apa, ine ndingonena za yemweyu. Pakhala pali mahandireda a iwo, ndithudi. Mmodzi uyu anathamanga, anati, “M'bale Branham, masomphenya anu a mu *Voice* ya Amuna Amalonda . . .”

425 Ndipo ine ndikumuyamikira Tommy Nickels, ngakhale iye siali ndi Amuna Amalonda, panonso. Ine sindikudziwa chifukwa chake, koma iye siali. Koma iye anayika izo mmenemo molondola basi, pamene ine ndinanena. Momwemo mu magazini yautatu ija, iye anati, “Pamene ine . . . Pamene Paulo anabatiza mu Dzina la Yesu, ndipo anawalamulira anthu kuti achite zomwezo, inenso ndachita zomwezo.” Mwaona, iye anaziya izo momwe izo zinaliri. Mukuona? Ndipo kotero ndiye ine—ine—ine ndinaganiza, “Mai!”

426 Mtumiki uyu analemba, anati, “M’bale Branham, masomphenya anu . . .”

427 Chimene, iwo akanakhoza kukhala masomphenya. Anati . . . Tsopano, ine sindikufuna kunena kuti, “kusinthidwa.” Ngati Paulo . . . Ngati ine ndinatengedwera mmwamba moyambirira umu ndi kukawona zimenezo, nanga bwanji Paulo amene anatengedwera mmiyamba yachitatu? Chimenecho chinali chiyani? Iye anati iye sakanakhoza nkomwe kuyankhula za izo, mwaona, ngati iye anatengedwera mmwamba. Ngati uko kunali kutengedwera mmwamba, ine sindikudziwa. Ine sindingathe kunena. Ine sindingathe kukuuzani inu.

428 Koma mtumiki uyu anati, “M’bale Branham, masomphenya anu amamveka Mwamalemba kwambiri ndipo onse abwino kufikira inu mutayankhula za kavalo kukhala ali kumeneko.” Anati, “Kavalo kupezeka Kumwamba?” Anati . . . Tsopano mukumuona mwamuna wachipembedzo uyo, nzeru, malingaliro? Mukuona? Iye anati, “Kumwamba kunapangidwira anthu, osati akavalo.”

429 Chabwino, ine ndinakhala pansi. Billy, mwana wanga pano, anayika kalatayo pomwe pano mu ofesi ya tchalitchi chakale, pafupifupi miyezi itatu kapena inayi yapitayo.

430 Ine ndinati, “M’bale wanga wofunika, ine ndikudabwa ndi nzeru zako, koma, ndi kudziwa kwako kwa Lemba. Ine sindinanene kuti ndinali Kumwamba. Ine ndinati izo zinali mmalo okhala ngati paradizo, chifukwa Khristu anali akadali pamwamba, mwaona. Koma,” ine ndinati, “ngati izo zingakukhutitse iwe, utsegule ku Chivumbulutso 19. Ndipo pamene Yesu akubwera kuchokera mmiyamba ya Kumwamba, Iye akukwera pa kavalo woyera, ndipo oyera mtima onse pamodzi ndi Iye akukwera akavalo.” Kulondola. Mwamtheradi. Inde, ndithudi.

431 Ndipo mmwamba Mmalo omwewo, munali chimodzi chowoneka ngati mphungu, ndipo china chowoneka ngati ng’ombe, ndipo china . . . Chabwino, mai, ali kuti akavalo aja amene anabwera kudzamutenga Eliya? Zikungowonetsera, mwaona, malingaliro a munthu amangofuna chinachake choti atsutsepo. Uko nkulondola.

432 Tsopano zindikirani. Koma ine ndimangoganiza, monga wofunika uyu, m'bale waumulungu, Yohane... Ine ndinangoganiza kuti iwo akanakhala malo abwino oti ndibayirepo izo, basi ndisanatseke, mwaona. Ngati Yohane anayang'ana Kumeneko, ndipo awo anali abale ake, mwaona, abale ake amene ankayenera kuvutika pang'ono; ndiye, mukuona, Ambuye Mulungu anandilora ine kuti ndiwawone abale anga ndi oyera mtima amene amayembekezera Kudza kwa Ambuye. Zindikirani, iwo sanali pansi pa guwa la nsembe; angawo sanali. Koma, awa anali, iwo anali ofera. Mukuona? Angawo sanali pansi pa guwa la ofera.

433 Tsopano ine ndikufuna kuti inu mumvetsere mwacheru kwenikweni. Ndipo ine nditseka, moona mtima, basi pafupifupi mu maminiti teni, pa teni koloko, ngati ine nditi ndingodula zimenezo ndi kudzamalizitsa izo mawa.

434 Penyani. Iwo, iwo sanali anga...iwo amene Ambuye anandiwonetsa ine, Mkwatibwi, Iye sanali pansi pa gawo la ofera, ayi, guwa la nsembe la ofera; koma anali atalandira mikanjo yoyera, povomereza chisomo chokhululukira cha Mawu amoyo. Khristu anali atawapatsa iwo mikanjo yoyera. Ine sindikuganiza, pakutsegula...

435 Kapena, ine ndikuganiza, kani, pakutsegula kwa Chisindikizo Chachisanu ichi, monga ine ndikukhulupirira, kuti Icho chatseguka kwa ife. Ine ndinazichita izo ndi chikumbumtima chabwino, ndi vumbulutso loyera pamaso pa Mulungu. Osati kuyesera kungochipanga icho, kuganiza, chifukwa ine nthawizonse ndinkatsutsa bungwe, sindikanakhala wa iwo nkomwe. Koma Icho chatseguka kwa ine tsopano.

436 Ndipo ine ndikuganiza chinthu china. Pa kutseguka kwa Chisindikizo Chachisanu ichi, mu tsiku lino, chikuwongola chiphunzitso pomwe pano, chimene ine ndikhoza kuchikamba, cha kugona kwa moyo. Tsopano, ine ndikuzindikira kuti muli anthu muno amene amakhulupirira zimenezo, mwaona, mu kugona kwa moyo. Ine ndikuganiza kuti Ichi chikutsutsa zimenezo. Iwo sakugona. Iwo ali moyo. Matupi awo, akugona. Koma, moyo, siuli mmanda, iwo ali mu Kukhalapo kwa Mulungu, mwaona, pansi pa guwa.

437 Apa ndi pamene ine ndimatsutsana ndi m'bale wofunika, mphunzitsi. Ndipo, ine ndikuzindikira, ine ndikudziwa ine ndikuwawona ena a anthu ake akhala pano. Amene, ine ndikuzindikira kuti uyu ndi mphunzitsi wamkulu. Iye ndi dokotala, ndipo a—Dokotala wa Zauzimu, ndi Ph., LL.D. Ndipo iye ndi—iye ndi munthu wabwino kwenikweni, nayenso. Ine ndikuganiza kuti iye anatsogola, pa nthawi ino. Koma iye anali munthu wabwino, ndi wolembe wabwino. Ndipo ndi M'bale Uriah Smith, mlembi wa *Daniele ndi Chivumbulutso*. Tsopano,

kwa anthu inu amene muli otsatira ziphunzitso zake, mwaona, tsopano ine sinditero . . . Ine sindiri basi . . . sindikufuna kunena izi mwamwano, koma ine basi . . . Mukuona?

438 Koma, M'bale Smith, ndipo akuyesetsa kuthandizira, mwaona, ndipo akuyesetsa kuthandizira kugona kwa moyo, mmenemo iye akunena kuti, "Moyo umagona. Ndipo kulibe guwa la nsembe Kumwamba. Kutu, guwa lokhalo limene linakambidwa ndiro," kuti iye—amakhulupirira kuti ndi Kumwamba, "ndiro guwa la nsembe zofukiza." Koma kwa inu anthu okondedwa . . . Ndipo osati kutsutsana ndi m'bale wanga. Ine mwina- . . . ndikuyembekeza kudzakomana naye iye kumbali inayo, mukuona. Osati kutsutsana naye mphunzitsi wamkuluyo.

439 Koma kungokuwonetsani inu momwe Ichi chikutsutsira zimenezo, mwaona. Icho chikutsutsa zimenezo. Kutsegulidwa kwa Chisindikizo ichi, mu tsiku lotsiriza lino, chikungochotsa kugona kwa moyo pa njirayo. Mukuona? Iwo ali moyo. Iwo siali akufa. Mukuona? Zindikirani.

440 Zindikirani ichi tsopano. Tsopano, ngati kulibe guwa la nsembe Kumwamba, ndiye Nsembe ya tchimo ili kuti ndiye, Mwanawankhosa? Pakuyenera kukhala malo amene Mwanawankhosa wophedwayo, wamagazi, akukhala kumeneko, pamene Magazi . . . izo.

441 Tsopano, zofukiza zinali zonunkhira, zinthu zonunkhira zimene iwo ankaziwotcha, zimene Baibulo linati anali "mapemphero a oyera mtima." Ngati kulibeko nsembe paguwa, ndiye mapemphero sangalandiridwe. Ndi mwa Magazi okha, a pa guwa la nsembe, amene amalola mapemphero kupita kwa Mulungu.

442 M'bale Smith amalakwitsa, mwaona. Osati kutsutsana naye iye; ine ndikuganiza ndazipanga ndekha kumveka bwino, ndi chikondi chapaubale ndi maulemu chifukwa cha ntchito yake yayikulu, mwaona. Koma iye amalakwitsa.

443 Chisindikizo Chachisanu chatsegula zimenezo, mwaona, mwaona; zinthu zina zambiri, ngati mwazigwira izo. Mukuona? Ine ndikuyembekezera mafunso anga, mwaona, ngati ine . . . Chabwino.

444 Tsopano, likasa linali kuti; Mwanawankhosa wophedwa, wovulazidwa, wokhetsa magazi, wamagazi kwa chitetezero, kwa mapemphero onunkhira awa?

445 Zindikirani, Baibulo limati, "Ngati kachisi wathu wokhalamo uyu wapadziko lapansi adzapasuka, ife tiri naye wina amene akuyembekezera kale." Ndi kumene ine ndinawawona oyera amenewo. Mukuona?

446 Penyani pamene mwana . . . Mundikhululukire ine kachiwiri, alongo, chifukwa cha zoyankhula zosapsyatira izi pamaso pa akazi achichepere. Koma, penyani. Pamene mayi ali ndi

pakati, ndipo mulu waung'ono uwo wa minyewa ikugwedezeke ndi kumalumphwa, inu mukumvetsa, ilo ndi thupi lachibadwa. Ndipo basi monga momwe chirengedwe chikuchitira ndi thupi lachibadwa...

⁴⁴⁷ Kodi inu munayamba mwamuzindikirapo mkazi wanu ana asanabadwe? Iye nthawizonse, njira yonse, kotsiriza, amakhala wachifundo kwenikweni, wokoma. Ngati iye sanakhalepo, moyo wake wonse, iye adzakhala nthawi imeneyo. Kodi inu munayamba mwazindikirapo chiyero chake, kapena kumverera kwake, inu munawazindikirapo amayi?

⁴⁴⁸ Ndipo inu mumamuwona wochimwa wina kunja uko, akumamuseka mayi amene ali—mkazi wa pakati. Ine ndikuganiza kuti izo ndizopusa. Umenewo ndi moyo ukubwera ku dziko lapansi.

⁴⁴⁹ Koma kodi inu munazindikira, pozungulira mayi ameneyo pamawoneka kuti pamakhala kumverera kokoma? Icho ndi chiyani? Ndi thupi laling'ono lauzimu, moyo wauzimu, ukuyembekezera kuti ubwere mu thupi laling'ono ilo mwamsanga ilo likangobadwa. Tsopano ilo limangobadwa; koma, pamene ilo libadwa, ilo limabadwa. Thupi lauzimu limalumikizana ndi thupi lachibadwa.

⁴⁵⁰ Ndipo, kenako, Baibulo limaphunzitsa kuti ife tsopano ndi obadwa mwa Mulungu. Ndife obadwa mwa Mzimu Woyera kuti mwa ife muli Khristu, mwana wa Mulungu akuwumbidwa mwa ife. Ndipo pamene thupi lapadziko ili lipasuka, thupi lauzimu ili limabwera kuchokera mmimba mwa dziko lapansi, pamakhala thupi lina likuyembekezera kuti likalandire limenelo. “Ngati kachisi wapadziko uyu agwetsedwa, pali thupi lina loti limulandire iye.” Thupi lachivundi ili limavala chisavundi. Lapadziko ili limavala lakumwamba. Izi, mukuona chimene ine ndikutanthauza? Pali thupi lachibadwa limene liri lochimwa; koma, mu kapangidwe kake, chimodzimodzi monga ilo, pali thupi lina limene ife timapitako.

⁴⁵¹ Ndipo ndine woyamikira kwambiri kwa Mulungu kuti ine ndikhoza kunena, monga m'busa wanu ndi m'bale, Ine ndinakawawona anthu amenewo, kotero ndithandizeni ine, mu thupi limenelo, ndipo ndinakawagwira iwo ndi manja anga. Uko nkulondola. Zindikirani.

⁴⁵² Penyani. Tayang'anani pa Mose, Eliya. Mose atamwalira, ndipo Eliya atatengedwa kupita Kumwamba, iye anayima apa pa Phiri la Chiwalitsiro ali ndi zokhudzira zake za kuyankhula, kumva, kumvetsa, ndipo anayankhula ndi Yesu asanapachikidwe. Tsopano, kodi iye anali ndi thupi la mtundu wanj?

⁴⁵³ Tayang'anani pa Samueli, pambuyo pa kumwalira kwa pafupifupi zaka ziwiri. Anayitanidwanso mu—phanga usiku umenewo, ndi mfiti ya ku Endori, ndipo anayankhula ndi

Sauli ndi chinenero; anamumva Sauli, anamuyankhanso, ndipo anadziwiratu zinthu zimene zikanati zidzachitike. Komabe, mzimu wake unali usanasinthe. Iye anali mneneri.

⁴⁵⁴ Pamene mzimu wa Eliya ubwera pa munthu, iwo udzamuyendetsa iye basi monga Eliya. Iye adzapita ku chipululu. Iye adzakonda chipululu. Iye adzakhala wodana ndi akazi amakhalidwe oyipa. Iye adzakhala wotsutsa bungwe. Iye sadzanyengerera aliyense. Ndipo ndizo basi... Ndiwo, umenewo udzakhala mzimu wake. Iwo unali, nthawi iliyonse imene iwo unabwera, mwaona.

Mose adzakhala munthu yemweyo.

Tsopano, ndipo ife tikupeza, mu Chivumbulutso 22:8, chinthu chomwecho.

⁴⁵⁵ Tsopano, kapena kukhazikitsa izo, kwa iwo amene... Miyoyo imeneyo (tsopano penyani izi) pansi pa guwa, za kutsegula kwa Chisindikizo ichi, imene inali itaphedwa mu nthawi ya pakati pa imfa ya Khristu ndi kukwera mmwamba kwa Mpingo; gulu la Eichmann, ndi onsewo, Ayuda owona amenewo ali ndi maina awo pa Bukhu. Ngati inu mungayang'ane, m'bale wanga, molingana ndi Lemba, iwo ankatha kuyankhula, kufuula, kuyankhula, kumva, ndipo anali ndi zokhudzira zonse faivi. Osati amagona m'manda, atakomoka. Iwo anali mmaso kwenikweni, ndipo amatha kuyankhula, kuyankhula, kumva, china chirichonse. Nkulondola uko? Oh, tithandizeni ife!

⁴⁵⁶ Maminiti awiri. Amen. Ine... pepani ndakusungani inu kwa theka la ora. Ayi, ine sindingathe, ine sindimayenera kunena zimenezo, mwaona. Mukuona? Uko nkulondola, mwaona.

⁴⁵⁷ Koma, penyani, apa pali kupambana kwa kumvetsa kwanga, kopambana. Ndipo molingana ndi vumbulutso limene linaperekedwa kwa ine mmawa uno kutangotsala pang'ono kucha, ndi Ambuye Yesu Khristu, ndi chimenecho Chisindikizo Chachisanu chotsegulidwa, choti chipite ndi zinayi zinazo. Mwa chisomo Chake, Iye anapereka icho kwa ine, chisomo Chake kwa inu ndi ine. Ife tikumuthokoza Iye chifukwa cha Icho. Ndipo, ndi thandizo Lake, ine ndikufuna kukhala pafupi kwambiri... monga ine ndingakhalire moyo, kuwaphunzitsa ena kuti azichita chinthu chomwecho, kufikira ine ndidzakomane ndi Iye, limodzi ndi inu, mu Ulemelero, pamene zinthu zonse zidzatha. Ine ndikumukonda Iye chifukwa cha ichi, ndipo ndiko kupambana kwa kudziwa kwanga kwa Icho.

⁴⁵⁸ Ndipo ine ndikukhulupirira moona, ndi mtima wanga wonse, kuti mavumbulutso owona a kuwululidwa kwa Chisindikizo Choyamba, Chachiwiri, Chachitatu, Chachinayi, ndi Chachisanu, ndi otsegulidwa tsopano kwa ife.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine

...?...

Pa mtengo wa Kalvare.

[M'bale Branham akung'ung'uza *Ndinkonda Iye*—Mkonzi].

⁴⁵⁹ Tsopano, mwakachetechete, molemekeza, pamaso pa Mulungu! Momwe ife tawonera Chisindikizo ichi chikutsegulidwa kwa ife, Mulungu kuchita kuwatenga ana Ake Omwe okondedwa ndi kuchititsa khungu maso awo, ndi kuwatumiza iwo, chifukwa chirungamo Chake Chomwe—chirungamo chimafula chiweruzo cha tchimo. Taganizani za zimenezo. Chirungamo Chake, ndi chiyero Chake zimafula chirungamo. Lamulo lopanda chilango si lamulo. Ndipo malamulo Ake Omwe, Iyemwini, Iye sangawanyoze ndi kukhalabe Mulungu.

⁴⁶⁰ Ndi chifukwa chake Mulungu ankayenera kukhala munthu. Iye sakanatenga cholowa mmalo, mwana amene sanali... mwana wamba chabe kwa Iye, kapena chinachake. Mulungu anadzakhala ziwiri zonse, Yesu anadzakhala ziwiri zonse Mwana ndi Mulungu, njira yokhayo imene Iye akanachitira izo molungama. Mulungu ankayenera kuchitenga chilangocho, Iyemwini. Izo sizikanakhala zolungama, kuti achiyike icho pa winawake, munthu wina. Chotero, Umunthu wa Yesu anali Mulungu, wowonetseredwa mu thupi, wotchedwa Emmanuele.

⁴⁶¹ Ndipo kuti achite zimenezo, ndi kuti atenge Mkwatibwi, ndi kupulumutsa gulu lotayika la Amitundu, Iye ankayenera kuwachititsa khungu ana Ake Omwe. Ndipo kenako nkuwalanga iwo chifukwa cha icho, mu thupi, chifukwa chomukana. Koma chisomo Chake chinapereka mikanjo. Koma, Moyowo, mukuona chimene chinachitika.

⁴⁶² Ndipo ngati Iye ankayenera kuchita zimenezo, ndi cholinga choti ife tidzakhale ndi mwayi, ife tingawukane bwanji mwayi umenewo mu chikondi? Ngati alipo mchipinda chino, usikuuno, munthu ameneyo, wamng'ono kapena wamkulu, amene kufikira nthawi ino wakana mwayi umenewo umene unamutengera Mulungu mtengo woterowo, ndipo inu mukufuna kuti mulandire mwayi umenewo woperekedwa ndi Mulungu, usikuuno; kuti inu simukusowa kukhala, monga momwe ife tikudziwira konse, kukhala wofera, ngakhale inu mungakhale. Koma mkanjo woyera waperekedwa kwa inu. Ndipo ngati Mulungu akugogoda pa mtima wanu tsopano, bwanji osavomereza izo! [M'bale Branham anagogoda pa guwa—Mkonzi].

Tsopano tiyen tiweramitse mitu yathu kachiwiri.

⁴⁶³ Ngati munthu ameneyo, kapena anthu, ali muno, amene akukhumba zimenezo, kapena akufuna kulandira izo pa maziko a chikhulupiro chanu mwa Magazi okhetsedwa amene Mulungu anakukhetserani inu, anavutika kuposa chirichonse chimene wachivundi aliyense. Sipakanakhala munthu wachivundi amene akanavutika monga chomwecho.

Mpaka, nkhwawa Yake Yomwe inalekanitsa madzi Ake ndi Magazi Ake, mmitsempha Mwake. Iye asanapite ku Kalvare, madontho a Magazi ankatuluka mthupi Lake, ndi nkhwawa yotero ndi mtima wosweka chifukwa cha chimene Iye ankayenera kuchita. Koma, akanakhoza kuchikana icho, nayenso. Koma, mololera anachita icho kwa inu ndi ine. Kodi inu mungakane chikondi chosafanizirika choterocho?

⁴⁶⁴ Ndipo inu mukuona izo tsopano, mwa kutsegula kwa Zisindikizo izi; icho chimene inu mwachita, ndi chimene Mulungu wakuchitirani inu. Ndipo inu mwakonzeka kupereka moyo wanu kwa Mulungu, ndipo ngati Iye angakukhwathuleni inu kuchokera mmanja mwa wotsutsakhristu mwa amene inu mulimo tsopano, kodi mungavomereze mwayi Wake, pa kungokweza dzanja lanu kwa Iye, kunena kuti, “Mulungu, mwa ichi, ine ndikuwonetsera, ine ndikuvomereza mwayi umenewo wa chisomo?”

⁴⁶⁵ “Ndipo, M’bale Branham, ine ndikusowa mapemphero anu, kuti ine ndizikhalabe wokhulupirika nthawizonse.”

⁴⁶⁶ Kwezani dzanja lanu, ndipo ine ndipemphera. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mutanthauze izo tsopano. Musati—musachite zimenezo pokhapokha mukutanthauza izo. Ndipo pomwepo pamene inu mwakhalapo, muvomereze izo pomwepo. Chifukwa, kumbukirani, inu simukanakweza dzanja lanu pokhapokha Chinachake chitakuuzani inu kuti muchite zimenezo. Ndipo palibe china chirichonse chimene chikanakhoza kuchita icho koma Mulungu.

⁴⁶⁷ Kotero, tsopano, pamene inu mwaona Malemba akufutukulidwa mwangwiro! Inu mwaona chimene chakhala chikuchitika, kudutsa mmusi mmibadwo, zaka zingapo zapitazi, zaka twente kapena sarte. Inu mwaziwona izo zikutsimikiziridwa mwangwiro. Inu mwaona Lemba likunena ndendende chimene chachitika, ndi chimene chikukonzekera kuti chichitike. Ndiye, pa maziko a chikhulupiriro mu ntchito ya Khristu, pamene inu mwakhala pakali pano, ndipo mwakweza manja anu, itini, “Kuyambira miniti ino mpaka mtsogolo, icho chakhazikika. Ine ndikumutenga Khristu tsopano kukhala Mpulumutsi wanga. Ndipo ine ndizimukhalira moyo Iye, moyo wanga wonse. Ndipo ine ndikukhumba kuti Mulungu andidzaze ine ndi Mzimu Woyera.” Ndipo ngati inu simunabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, dziwe likhala likukuyembekezerani inu.

Tiyeni ife tipemphere.

⁴⁶⁸ Ambuye Mulungu, panali chiwerengero chachikulu cha manja pakati pa anthu, amene anakwera mmwamba. Ine ndikutsimikiza kuti Inu ndi Ambuye Yesu yemweyo amene munapanga chitetezero kwa ife, zaka zambiri zapitazo. Ndipo powona Zisindikizo izo zikuwululidwa, ndi zinthu zazikulu zimene zachitika pomwe pano mu zaka zingapo

zapitazi, ine ndikukhulupirira ndi mtima wanga wonse kuti khomo la chifundo likuyamba kutsekeka, ndipo Inu mwakonzekera kuti muwuyambe ulendo Wanu tsopano kuti mudzawombole anthu Anu. Pamene pakadali malo, ndi khomo lotseguka, monga izo zinakhalira mmasiku a Nowa, mulole kuti miyoyo yofunika iyi imene ikukhala mu thupi la kachisi uyu amene ati adzapasulidwe tsiku lina, amene anakweza mmwamba dzanja lachivundi lija, mkati mwa iwo; chifukwa cha kwawo—kukhudzidwa kwawo ndi kuvomereza kwawo, kuti iwo akukhulupirira ndipo akufuna kuvomereza malingaliro Anu kwa iwo, kwa chipulumutso, pa Bukhu losindikizidwa—lotseguka ili limene latsegulidwa kwa ife. Perekani kwa iwo, usikuuno, Ambuye, mkanjo wa chirungamo cha Yesu Khristu, ndipo muveke moyo wawo mmenemo, kuti iwo akakhoze kuyima pamaso Panu mu Tsiku limenelo limene layandikira, angwiwo, mwa Magazi a Khristu.

⁴⁶⁹ Ambuye Mulungu, ngati iwo sanabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu! Ndipo pa vumbulutso limene Inu mwandipatsa ine lokhudza izo; ndi powona kuti Paulo anawalamulira anthu amene anali ngakhale atabatizidwa ndi Yohane M'batizi, kuti akabatizidwenso kachiwiri mu Dzina la Yesu Khristu, kuti alandire Mzimu Woyera, mu Machitidwe 19. Ine ndikupempha kuti Inu muwatsimikizire iwo, Ambuye, za Choonadi, ndipo mulole kuti iwo akumvereni Inu.

⁴⁷⁰ Ndipo kenako mu kumvera kwa kuvomereza kwawo, ndi kumvera ku kuvomereza kwawo, ndipo mpaka kupita ku madzi; mulole Inu kuti, pobwezera, muwadzaze iwo ndi Mzimu Woyera, kwa mphamvu ya utumiki, moyo wawo wonse. Ine ndikuwapereka iwo tsopano kwa Inu, mu Dzina la Mwanawankhosa woperekedwa nsembe wa Mulungu, Yesu Khristu. Amen. Amen.

Ndinkonda Iye, ndinkonda Iye
Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine
Nandigulira chipulumutso changa
Pa mtengo wa Kalvare.

⁴⁷¹ Tsopano kwa inu amene munakweza manja anu mmwamba: Mverani kulamulira kwa Mzimu, kumene kungatsatire—kukhazikitsidwa kwa Mawu, kwa wochimwa wolapa. Mutsatire izo, mu kachitidwe kalikonse. Ndipo Mulungu wa Kumwamba akupatseni inu mphotho chifukwa cha kuyima kwanu kwa Iye. Ambuye akudalitseni inu.

⁴⁷² Mawa usiku, mudzabweretse mapensulo anu ndi mapepala, tsopano, monga inu mwakhala mukuchitira. Ife tikuyembekeza kudzakhala pano nthawi yomweyo, pa hafu pasiti-seveni, ndendende, Ambuye akalola. Ndipo pa...mundipempherere ine, kuti Mulungu adzatsegule Chisindikizo Chachisanu Ndi Chiwiri kwa ine, mawa, kuti ine ndidzathe kuchibweretsa Ichu

kwa inu pamene Iye akupereka Icho kwa ine. Kufikira nthawi imeneyo, ife tiyimbenso. Osati kupyolera mu nyimbo kokha, koma kupyolera mu matamando kwa Iye amene anafa mmalo mwathu ndi kudzatiwombola ife. *Ine ndinkonda Iye.*

Ine . . .

Ndi abusa anu tsopano.

. . . ndinkonda Iye, ndinkonda Iye

Chifukwa Iye anayamba kundikonda ine. 

63-0322 Chisindikizo Chachisanu
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org

CHIVUMBULUTSO CHA ZISINDIKIZO ZISANU NDI ZIWIRI
(The Revelation Of The Seven Seals)

Mauthenga khumi awa analalikidwa ndi M'bale William Marrion Branham pa Marichi 17 mpaka pa Marichi 24, 1963, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., ndipo *Chisindikizo Chachisanu ndi chiwiri* chinapitirira pa Marichi 25 ku Sherwood Motelo. Titapeza matepi apachiyambi omveka ndi otsirizika kwathunthu, Mauthenga awa abwerezedwanso molingana ndi dongosolo latsopano. Kuyesesa konse kwapangidwa pochotsa molondola Uthenga wolankhulidwa pa matepi a maginito kupita ku tsamba losindikizidwa, ndipo atsindikizidwa mkatimu mosachotsera mawu ena.

Maufulu onse mu bukhu ili ndi osungidwa. Bukhu ili silingagulitsidwe, kapena kusindikizidwanso, kumasuliridwa mu zilankhulo zina, kapena kugwiritsidwa ntchito popezera ndalama wopanda kufotokoza kwa chilolezo cholembedwa cha William Branham Evangelistic Association. Kunasindikizidwa kachiwiri mu 2005.

CHICHEWA

©2026 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org